

***NDONDOMEKO ZA NJIRA***

***ZA***

***KUCHULUKITSA***

**HARVESTIME INTERNATIONAL INSTITUTE**

Phunziro limeneri ndi gawo limodzi la maphunziro a **Harvest International Institute** ndipo cholinga chake ndi kukonzekeretsa okhulupilira kuti akatute zokolora zambiri zauzimu.

Mutu waukulu mumaphunzirowa ndikuphunzitsa zimene Yesu anaphunzitsa, zimene zinasandulitsa anthu wamba monga asodzi, otolera misonkho ndi ena kulalikira Uthenga Wabwino ndi kuwonetsera mphamvu ya uthengawo mu nthawi yawo.

Bukuli ndi phunziro limodzi mwa maphunziro ambiri amene cholinga chake ndikuwakopa okhulupilira kuti akakonze dongosolo, kuyendetsa, ndi kubweretsa pamodzi anthu kuti Uthenga Wabwino ukalalikidwe.

@Harvestime International Institute

## ZAMKATI MWA BUKULI

Kagwiritsidwe Ntchito Ka Bukuli.....	3
Ndondomeko Zothandizira Kuphunzira Limodzi Pagulu.....	4
Mau Oyamba.....	5
Zolinga za Maphunzirowa.....	7

## NDONDOMEKO ZA NJIRA ZA KUCHULUKITSA

1. Asodzi a Anthu.....	8
2. Tsiku la Zinthu Zochepa.....	16
3. Mafanizo a Kuchulikitsa.....	40
4. Chimodzi Kuphatikiza Chimodzi Zimakhala Zopitilira Ziwiri.....	50
5. Mawu Oyamba a Kukula kwa Mpingo.....	58
6. Kukula kwa Mkati.....	70
7. Kukula mu Chiwerengero.....	90
8. Kukula Mmadera.....	104
9. Kukula Polumikiza.....	112
10. Zisankho Kapena Ophunzira.....	127
11. Kukula Mopinimbira.....	143
12. Malo Ochitirapo Maphunziro.....	154
13. Mayankho a Mafunso Odziyetsa Nokha.....	163

## ***KAGWIRITSIDWE NTCHITO KA BUKULI***

### **KAKONZEDWE KA BUKULI**

Phunziro liri lonse limakhala ndi zinthu izi:

**Zolinga:** Izi ndi zimene mukuyenera kukwaniritsa kapena kudziwa pa mapeto pa phunziro. Welangani zimenezi musanayambe phunziro lanu.

**Vesi Yotsogololera:** Ndimeyi imatsindika mfundo yayikulu mu phunziro lathu.

**Zopezeka mu Magawo:** Gwiritsani ntchito Baibulo lanu kuti mufufuze mavesi amene sanalembedwe mu bukuli koma angotchulidwa.

**Mayeso Odziyesa Nokha:** Osathamangira kulemamba mayeso musanamalize kuwerenga chaputala, komanso polemba musagwiritse ntchito Baibulo kapena bukuli polemba mayesowa. Mayankho amayesowa muwapeza kumapeto a bukuli.

**Zophunzira Zowonjezera:** Ndime imeneyi ikuthandizani kuti muwerenge mau Mulungu ndi kuzamitsa ukadaulo wanu pophunziro komanso kugwiritsa ntchito mu utumiki zimene mwa.

**Mayeso Omaliza:** ngati mwayamba kuphunzira phunziroli mukuyenera kulemba mayeso pamapeto a phunziroli ndipo mayesowo aperekedwa kwa aphunzitsi anu kuti mupatsidwe malikisi.

### **ZOWELENGA ZINA ZOFUNIKA POPHUNZIRA PHUNZIROLI**

Mudzafunikira Buku Lopatulika

## NDONDOMEKO ZOTHANDIZIRA KUPHUNZIRA LIMODZI PAGULU

### MKUMANO WOYAMBA

**Kutsekulira:** Yamabani ndi pemphero ndi kudziwana wina ndi mnzake ndipo ophunzira alembetse mayina.

**Khazikitsani Ndongomeko Zapagulu:** Musankhe amene atsogolere mkumano wanu, sankhaninso malo ndi masiku amene mudzikumana.

**Mayamiko ndi Matamando:** Yitanirani kupezeka kwa Mzimu Woyera pamene muchita mkumano wanu.

**Gawani Mabuku Kwa Ophunzira:** Awuzeni ophunzira dzina laphunziro, zolinga zake ndi dongosolo.

**Perekani Nchito Yoyamba.** Ophunzira ayenera kuwerenga ma chaputala amene apatsidwa ndikulemba mayeso odziyesa okha isanafike nthawi ya mkumano wina. Ndipo kuchuluka kwa machaputala amene adziphunzitsidwa pa mkumano uli onse kuzitengera kutalika kwa chaputala komanso kumvetsetsa kwa ophunzira.

### MKUMANO WACHIWIRI NDI KUKUMANA KWINA PATSOGOLO

**Kutsekulira:** Tsekulirani ndi pemphero kenako lembani mayina awophunzira atsopano ndikuwapatsa buku lawo. Muyitane mayina a wophunzira amene abwera. Komanso osayiwala mayamiko ndi matamando kwa Mulungu.

**Kukumbutsira:** Yambani ndi kubwereza mwachidule zimene munaphunzitsa mu mkumano wanu womaliza.

**Phunziro:** Afunseni ophunzira ndemanga zawo kapena mafunso okhudza phunziro limene aphunzira komanso mmene angagwiritsire ntchito zimene aphunzira pamoyo wawo ndi utumiki.

**Mayeso Odziyesa Nokha:** Konzetsani mayeso amene ophunzira amaliza ndipo mukhonza kusankha kupereka mayankha kapena kuwachotsa mubukuli kuti ophunzira adziperezere okha mayankho.

**Mayeso omaliza:** Pamapeto pa maphunziro amenewa, gulu la ophunzira onse lidzapemphedwa kulemba mayeso omaliza ndipo aphunzitsi awonetsetse kuti ophunzira wina ali yense ali ndi buku laphunziroli.

## MAWU OYAMBA

Baibulo limakamba za kulengedwa kwa dziko lapansi komanso Adamu ndi Hava (Genesis 1). Lamulo loyamba limene Mulungu anawapatsa ndi loti achulukane:

**Mulungu ndipo adalenga munthu m'cifanizo cace, m'cifanizo ca Mulungu adamlenga iye; adalenga iwo mwamuna ndi mkazi.**

**Mulungu ndipo anadalitsa iwo, ndipo adati kwa iwo, Mubalane, mucuruke, mudzaze dziko lapansi, muligonjetse: mulamulire pa nsomba za m'nyanja, ndi pa mbalame za m'mlengalenga, ndi pa zamoyo zonse zakukwawa pa dziko lapansi. (Genesis 1:27-28).**

Kuchulukakanaku sikunali kwa kuthupi kokha ayi, komanso kunali kwa ku uzimu. Monga mmene Adamu ndi Hava amachulukana ku thupindiye kuti akanalidzadza dzikoli ndi enanso ngati iwowo; amene anamdziwa Mulungu ndi kuyenda mu chiyanjano ndi Iye. Akanakhala akuchulukana mu uzimu monganso kuthupi.

Kugwa kwa munthu ku uchimo kunaika dongosolo lochulukakanali pa chiposezo (Genesis 3). Tchimo linabweretsa imfa ya kuthupi imene inatchinga kuchulukana kwa kuthupi (Genesis 2:17). Tchimo linabweretsanso imfa ya uzimu imene ndi kulekana kwa uzimu kwa munthu wochimwa ndi Mulungu wolungama. Ukunso kunatchinga kuchulukana kwa uzimu.

Pakuti Mulungu anamkonda munthu kwambiri, choncho adapanga dongosolo lopulumutsa anthu ku imfa ya uzimu yowawayi. Mulungu anatumiza Yesu Khristu kufera zolakwa za anthu onse. Yesu analipira chilango cha imfa mmalo mwathu, keneko anagonjetsa imfa pa kuukanso ku imfa (Yohane 20).

Munthu aliyense ayenera kusankha kulandira dongosolo la Mulungu la chipulumutso pa kupempha chikhulukiro cha machimo ndi kulandira Yesu ngati Mpulumutsi. Monga wokhulupirira mwa Yesu amene machimo ake akhulukidwa, ndiye kuti mwapulumutsidwa ku imfa ya uzimu.

Ngakhale kuti thupi loonekali lidzafa tsiku lina, mudzakhale ndi moyo ku uzimu ndipo mudalandira matupi atsopano amene adzakhala ndi moyo nthawi zonse.

**...Koma tonse tidzasandulika, m'kamphindi, m'kutwanima kwa diso, pa lipenga lotsiriza; pakuti lipenga lidzalira, ndipo akufa adzaukitsidwa osabvunda, ndipoife tidzasandulika...Ndipo pamene cobvunda ici cikadzabvala cisabvundi ndi caimfa ici cikadzabvala cosafa, pamenepo padzicitika mau olembedwa, 20 Imfayo yamezedwa m'cigonjetso (1 Akorinto 15:51,52,54).**

Pamene mwalandira Yesu ngati mpulumutsi wanu, zili ngati kulengedwanso ndi Mulungu kachiwiri. Baibulo limati “kubadwanso mwatsopano”:

**Yesu anayankha nati kwa iye, Indetu, indetu, ndinena ndi iwe, Ngati munthu sabadwa mwatsopano, sakhoza kuona Ufumu wa Mulungu (Yohane 3:3).**

Moti “Kubadwa mwatsopano” sikutanthauza kubadwa kuthupi. Kumatanthauza kubadwa ku uzimu. Mumalengedwanso ku uzimu monga olengedwa atsopano mwa Khristu. Ndinu “atsopano” chifukwa simukhalanso mu uchimo ndi kuchita makhalaidwe akale a uchimo:

**Cifukwa cace ngati munthu ali yense ali mwa Kristu ali wolengedwa watsopano; zinthu zakale zapita, taonani, zakhala zatsopano (2 Akorinto 5:17).**

Pa chiyambi cha dziko lapansi, Mulungu koyambirira analamulira anthu ake olengedwe mwatsopano kuti achulukane. Lamulo lake loyamba lolenganso, okhulupirira “obadwa mwatsopano” ndi chimodzimodzi. Tikuyenera kuchulukana mu uzimu ndi kulidzadza dziko lapansi ndi ena ngati mmene ifeyo tilili; anthu amene ndi okonda Mulungu ndi kuyenda muchiyanjano ndi Iye.

Pamene Yesu anayitana anthu kuti amutsatire, uku kunali kuitanira anthu ku chichulukitso cha uzimu (Luka 5:10). Lamulo lake lomaliza kwa okhulupirira linali loti achulukane ku uzimu (Machitidwe 1:8). Kuti tikwanitse kufikira anthu zikwi amene akufa ku uchimo asanamve uthenga, okhulupirira aliyense akuyenera kukhala ochitachita ndi kuphunzira mfundo za kuchukana ku uzimu.

Phunziroli limagawanso ndi njira za Mbaibulo za kukhala ochitachita mu uzimu zimene zikupangitsani inu kuchuluka mwa kumvera lamulo la Mulungu. Muphunzira za mmene mungachulukani ku uzimu monga munthu komanso ngati gulu pa tchalitchi. Ngati mugwiritse ntchito mfundo za Mbaibulo zimene zikuphunzitsidwa mu phunziro, muzakhala ndi udindo wa kuchulukana zikwi kwa okhulupirira ophunzitsidwa ndi olimbikira.

Ngati mukuphunzira maphunziro a Havestime International Institute mwandondomeko, phunziro ili ndi lachitatu mu mabuku atatu, amene amakamba za kuchulukitsa antchito ophunzitsika a ku uzimu kupyolera kumapeto kwa buku lachiwiri.

Maphunziro amene akupezeka mu buku la chitatu ndi awa “*Kuumba Maonedwe a Dziko a Mbaibulo,*” “*Njira Zophunzitsira,*” *Njira Zochukitsa,*” ndi “*Mfundo za Mphamvu.*” Maphunziro amenewa amabweretsa chidziwitso cha chosowa cha ku uzimu cha dziko lapansi ndi kulongosolo za mmene mungafikirire chosowacho kudzera mu ziphunzitso ndi maulaliki a Mbaibulo, kuchulukana ndi machitachita a mphamvu za uzimu.

## ZOLINGA ZA MAPHUNZIROWA

Pakutha pa phunziroli muyenera:

- Kubalana ku uzimu kudzera mu kugwiritsa ntchito njira zochulukana za Mbaibulo.
- Kuomba mkota pa mfundo za kuchulukana zimene zinaphunzitsidwa mu mafanizo a Mchipanagano Chatsopano.
- Kulongosola mmene okhulupirira angachulukanire ku uzimu pa kubadwisa mazana a okhulupirira atsopano.
- Kupanga kunyumba kwanu ngati malo ochulukaniranapo ku uzimu.
- Kuomba mkota pa mfundo za kuchulukana mkati mwa mpingo.
- Kuomba mkota pa mfundo za kukulitsa kuchulukana kwa mpingo.
- Kuomba mkota pa mfundo za kutalikitsa kuchulukana kwa mpingo.
- Kuomba mkota pa mfundo za kulumikiza kuchulukana kwa mpingo.
- Kulimbikitsa otembenuka mtima kumene kuti asangokhala ophunzira kokha ayi.
- Kudziwa zinthu zimene zimatchinga kuchulukana ku uzimu.
- Kukhazikitsa Havestime International Institute ngati malo ochulukana ku uzimu.

## CHAPUTALA CHA 1

### ASODZI A ANTHU

#### ZOLINGA:

Pakutha pa chaputalachi muyenera:

- Kulemba Vesi Lotsogolera kuchokera pantima.
- Kudziwa lamulo loyamba ndi lotsiriza la Yesu kwa ophunzira ake.
- Kupereka tanthauzo la “kuchukitsa.”
- Kulongosola za kuchulukana kwa ku uzimu.
- Kupereka tanthauzo la “njira.”
- Kupereka tanthauzo la “ndondomeko za njira”
- Kulongosola “njira zosiyanasiyana za kuchulukitsa ku uzimu”
- Kuomba mkota pa mfundo za usodzi wodziwika umene tingautanthauzire ku usodzi wa uzimu.

#### VESI LOTSOGOLERA:

**Ndipo Yesu ananena nao, Idzani pambuyo panga, ndipo ndidzakusandutsani inu asodzi a anthu (Marko 1:17).**

#### MAWU OYAMBA

Pamene Yesu anayamba utumiki wake pa dziko lapansi, anayitana anthu ambiri kuti akhala ophunzira ake oyamba:

**Ndipo Yesu ananena nao, Idzani pambuyo panga, ndipo ndidzakusandutsani inu asodzi a anthu (Marko 1:17).**

Lamulo loyamba kwa akuphunzira amenewa linali likuti achulukane ku uzimu. Ngati amamutsatira, Iye anawapanga “asodzi a anthu.” Akanachulukana pamene “amasodza” amuna ndi akazi ku uzimu.

Uthenga wotsiriza wa Yesu kwa akuphunzira ake unali owaytanira ku kuchulukana ku uzimu:

**Komatu mudzalandira mphamvu, Mzimu Woyera atadza pa inu: ndipo mudzakhala mboni zanga m'Yerusalemu, ndi m'Yudeya lonse, ndi m'Samariya, ndi kufikira malekezere ace a dziko.**



**Ndipo m'mene adanena izi, ali cipenyere iwo, ananyamulidwa; ndipo mtambo unamlandira iye kumcotsa kumaso kwao (Machitidwe 1:8-9).**

Kodi ophunzira akanakwaniritsa bwanji ntchito yotumidwa ndi Yesu? Kodi zikanatheka bwanji gulu la anthu ochepawa kuchulukana mkufikira dziko lonse?

### **NJIRA ZOCHULUKITSA**

Yesu anaulula njira zenizeni zimene zikanapangisa ophunzira ake kukwaniritsa lamulo lochulukana ku uzimu. Lamulo loyamba limenenso ndi lofunika linaperekedwa ngati gawo la kutumidwa ku Machitidwe 1:8. Ophunzira akanachulukana kudzera mu kulandira mphamvu ya Mzimu Woyera. Njira zina zinaululidwa pamene ophunzira a Yesu anayamba kuchuluka ndi kufikira dziko lapansi ndi uthenga wabwino. Njira zimenezi zikupezeka mmabuku a Machitidwe ndi Makalata mu Chipangano Chatsopano.

Phunziroli limalongosola njira za kuchulukana ku uzimu. Limaphunzitsa za mmene mungagwiritsire ntchito kuti kuchulukane ku uzimu ndi kukwaniritsa lamulo la Mulungu. Koma koyamba, muyenera kumvetsetsa pamene tikuti “kuchulukana.” Mawu oti “kuchulukana” akutanthauza kuti kukhala ambiri mu chiwerengero pa kuberekana. Kuchulukana ndi njira yochulukitsa. Pamene chinthu chachulukitsidwa, ndiye kuti chikuonjezeraka mobwereza mu mchitidwe ofanana.

Mu dziko limene timakhalali, amuna ndi akazi amachulukana pokhala ndi ana. Amachulukana kuthupi. Kuchulukana ku uzimu kumachitika pochulukana ku uzimu. Okhulupirira amachulukana pogawana uthenga wabwino ndi anthu ena, ndi kuwatsogolera kukhala okhulupirira, ndi kuwakhazikitsa kukhala ophunzira a Ambuye Yesu Khristu.

Baibulo limaulula za njira za Mulungu za kuchulukana ku uzimu. Choncho “njira” ndi dongosolo lofuna kukwaniritsa cholinga chapaderadera. Tsono “ndondomeko za njira” ndi dongosolo la njira zimene zimaikidwa pamodzi kuti mukathe kufikira cholinga chanu.

Motero “Ndondomeko za njira zochulukitsa” ndi njira zimene zimapangitsa okhulupirira kufikira cholinga chawo cha kuchulukana ku uzimu. Cholinga sichisintha. Tikuyenera kuchulukana ku uzimu pa kufikira dziko lonse lapansi ndi uthenga wabwino. Pali njira zambiri zimene tingathe kugwiritsa ntchito kuti tithe kufikira cholingachi. Njirazi ndi “ndondomeko” kapena madongosolo osiyanasiyana amene tingathe kuchuluka.

Pamene munthu agwira ntchito limodzi ndi njira za Mulungu zochulukitsa, zotsatira zake ndi kuchulukana ku uzimu. Moti okhulupirira amachulukana mkati mwa mmimba umene ndi mpingo.

## **KUITANIDWA KU NTCHITO**

Anthu amene Yesu anawaitana koyamba ngati akuphunzira ake anali asodzi. Anali anthu a ntchito zawo. Samasodza nsomba zawo pakamodzi. Amagwiritsa ntchito maukonde a akulu ndipo amapha nsomba zochuluka zosiyanasiyana.

Pamene Yesu anawaitana kuti akhale “asodzi a anthu,” amawaululira dongosolo la kuchulukana ku uzimu. Ophunzira ake amayenera “kusodza” amuna ndi akazi kuchokera ku maiko onse, zikhalidwe, ziyankhulo ndi mbali zonse za anthu. Maukonde awo a uzimu amayenera adzadze.

Yesu anaitanira anthu ku ntchito. Iye ananena kuti adzawapanga kukhala asodzi a wanthu. Sadzakhala ozangoyang’anira ntchito dongosolo la Mulungu. Koma adzakhala otenga nawo mbali pamene adzakhala akusodzera miyoyo ya muyaya ya amuna ndi akazi.

Kuitana kwa Yesu kukadali chimodzimodzi lero lino. Tikuyenera kukhala asodzi a anthu. Ngati sitikusodza, ndiye kuti sitikutsatira.

## **ASODZI A ANTHU**

Kodi ndi chifukwa chiyani Yesu adagwiritsa chitsanzo cha usodzi poitana ophunzira ake?

Koyamba, chifukwa choti chanali chitsanzo choti akanatha kuchimvetsa mwachangu. Anthu amenenewa moyo wawo unali usodza. Moti kusodzaku chinali chinthu chimene amachipatsa nthawi ndi mphamvu yawo. Pamene Yesu anawaitana kuti akhale asodzi a anthu, iwowo anamvetsa kuti ayamba “kusodza” anthu ku uzimu, monganso mmene amasodzera nsomba kudziko lapansi. Amatha kumvetsanso zimene zimafunika pa kuitanaku. Kusodza ku uzimu kumafuna kupereka nthawi komanso mphamvu zawo.

Chachiwiri, Yesu anagwiritsa ntchito chitsanzo cha usodzi poitana ophunzira chifukwa pali mfundo za kusodza kwa kuthupi kumene kutha kugwiritsidwa ntchito ku uzimu. Mfundozi ndi izi:

### **MUKUYENERA KUPITA KUMENE KUMAPEZEKA NSOMBA:**

Ngati mukufuna kusodza nsomba, mukuyenera kupezeka kumene nsomba zimapezeka. Nsomba zimapezeka mmadzi. Simuzasodza nsomba pamene mukuzidikira pamwamba pa phiri kapena mkatimkati mwa chipululu.

Monga wokhulupirira, mukuyenera kumene kupita kumene nsomba zili ku uzimu. Amuna ndi akazi amakhala mdziko. Simungamadikirire mu mpingo kuti osakhulupirira akupezeni

momwemo. Mukuyenera kupita kaya ndi pamsika, kusukulu, mmalo ogwiramo ntchito ndi “kusodza” paliponse pamene pali anthu osapulumsidwa.

### **MUKUYENERA KUZINDIKIRA MALO:**

Pamene mukusodza ku dziko lapansi, ndi zofunikira kuganizirapo za malo. Mukuyenera kuonetsetsa kuya kwa madzi pa nthawi imeneyo. Mukuyenera kudziwa kuti madziwo ndi amchere kapene ayi. Mukuyenera kuonetsetsa mmene mphepo ikuombera. Zinthu zonsezi za kudziwo zimatha kukudziwitsani za mtundu wa ngalawa imene komanso njira zimene mugwiritse ntchito pofuna kusodza.

Momwemomse kudziwo lapansi. Mukuyenera kuzindikira malo anu amene mukapezeka amuna ndi akazi. Kodi zosowa zawo ndi chani? Nanga zimene zikuchitika mmoyo wawo ndi chani? Izi zidzakuthandizani kudziwo njira zimene mugwiritse ntchito posodza miyoyo yawo.

Pamene Yesu anakumana ndi mkazi pa chitsime ku Yohane 4, Anazindikira malo amene anampeza iye. Mkaziyo amafuna madzi. Yesu anagwiritsa ntchito madziwo kuti adziwe chosowa chake cha ku uzimu. Njira imene anagwiritsa ntchito “inamuululira” mu Ufumu wa Mulungu.

Mudzikoli ngati mukugwiritsa ntchito njira zosodzera mtundu wa nsomba umene umakhala mmadzi amchere, simungasodze nsomba za mtundu umenewo chifukwa sizikhala mmadzi amchere. Koma zimapezeka mmadzi a bwinobwino.

Ngati simuzindikira malo a mudziko la uzimu, muzapezeka kuti mukusodza mtundu wa nsomba mmadzi amchere amene nsombazo sizikhalamo. Izi zili chonchi chifukwa simutha kumvetsa kumene anthu amapezeka ndi mmene mungawafikirire.

### **MUKUYENERA KUGWIRITSA NTCHITO NJIRA ZOSIYANASIYANA:**

Msodzi wabwino amagwiritsa ntchito njira zosiyanasiyana zosodzera nsomba. Amagwiritsa ntchito zakudya zosiyanasiya kuti athe kukopa nsomba. Amagwiritsanso zipangizo zosiyanasiyana zophera nsomba monga zitsulo, maukonde, mikondo kapena madengu. Motero nsomba zosiyana zimakopekansa ndi njira zosiyana zophera. Ichi ndi chifukwa chake nsodzi ayenera kugwiritsa ntchito njira zosiyanasiyana zophera nsomba.

Choncho nsodzi atha kuphunzira zina mwa njirazi mmabuku omwe amakamba za usodzi. Atha kuphunzira njirz zina ndi zimene zimachitika komanso kuoneka zokhudza usodzi. Motero njira zimene amagwiritsa ntchito zimasintha, koma cholinga sichimasintha ndiko kusodza nsomba.

Choncho ngati muli nsodzi wa uzimu wochitachita, mukuyenera kugwiritsa ntchito njira zosiyanasiyana. Chomwechonso anthu osiyanasiyana amakopeka ndi uthenga wabwino wolalikiidwa mu njira zosiyana. Ena amatha kuvulazidwa ndi uthenga wabwino pomwe ena amatha kutonthozedwa ndi uthenga wabwino omwewo mu nthawi yosowa. Ena “amakhuzidwa” ndi njoranzo zosiyanasiyana.

Njira za kusodza mu uzimu ndi zosiyanso, koma cholinga nthawi zonse chimakhala chomwecho...ndiko kusodza miyoyo ya anthu.

### **MUKUYENERA KOPONYA NDI KUKOKA:**

Kaya mukugwiritsa ntchito chitsulo chosodzera, ukonde, mkondo kumene mumasodza, mukuyenera kuponya mmadzi ndi kukokanso kawiri.

Mu dziko lathuli, mmene mumaponyera ukonde mmadzi ndizofunuka ndithu. Kuponya kwanu kukuyenera kukhala kwa chindunji. Mukuyeneranso kugwiritsa ntchito chotengera kuti musungiremo nsomba zanu mukasodza.

Mu dziko la uzimu, talonjezedwa kuti “ngati tiponya mawu a Mulungu” sadzabwerera chabe. Adzakwaniritsa cholinga chimene chake mmitima ndi mmiyoyo ya anthu (Yesaya 55:11). Pamene mugwiritsa ntchito mawu a Mulungu, mudzakhala chindunji nthawi zonse. Zotsatira zake “azasodza” amuna ndi akazi.

### **MUKUYENERA KUDZIWA NTHAWI:**

Nthawi ya tsiku ndi nyengo za pachaka zimakhudza usodzi mdziko lathu. Nsomba zina zimathawa ndipo simungazisodze mmadera komanso mnyengo zina. Nsomba zambiri zimasodzedwa kumayambiriro a tsiku pamene zikuyandikira pamwamba pa madzi kuti zidye. Ngati mukusodza mu nyengo yolakwika kapene mu nthawi yosayenera, simungasodze nsomba zambiri.

Nthawi ndi yofunikira ngakhale ku usodzi wa ku uzimu. Muphunzira kutsogolo kwa phunziroli za kufunika kwa “kusodza” malo olandirika a mdziko pamene nsomba “zimaluma” ku uzimu.

### **MUKUYENERA KUKHALA ODEKHA:**

Munthu amene ndi nsodzi wa kudera lathu amayenera kukhala odekha. Amayenera kudikira nsomba kuti zilowe mu ukonde. Momwemonse usodzi wa ku uzimu wa kudziko:

**Potero, lezani mtima, abale, kufikira kudza kwace kwa Ambuye. Taonani, wolima munda alindira cipatso cofunikatu ca dziko, ndi kuleza mtima naco kufikira cikalandira mvula ya myundo ndi masika (Yakobo 5:7).**

### **KUCHULUKANA KU UZIMU**

Kusodza kwa dziko lapansi kumachulukitsa nsomba. Kusodza kwa dziko la uzimu kumachulukitsa anthu mu Ufumu wa Mulungu. Kuberekana kwa anthu kumachulukitsa chiwerengero cha anthu. Kubalananso mu uzimu kumachulukitsa anthu ku uzimu.

Kuchulukana kwa umunthu ndi zotsatira za moyo. Kuberekana kwa ku uzimu ndi zotsatiranso za moyo. Sizimabwera kudzera mu dongosolo la munthu ayi. Kuchulukana ku uzimu kumabwera kudzera mmoyo wa uzimu ochokera kwa Mulungu.

Mu thupi la munthu, kubalana kumayamba mmimba mwa mkazi ndi dzila limodzi la moyo. Dzilalo limachulukana ku “mimba” ya uzimu ya mpingo. Muphunzira za mmene kuchulukana kwa ku uzimu kumayambira pamene mukuphunzira za “Tsiku la Zinthu Zochepa” mu chaputala chikudzachi.

## MAYESO ODZIYETSA NOKHA

1. Lembani Vesi Lotsogolera kuchokera pantima.

---

---

2. Kodi malamulo oyamba ndi otsiriza amene Yesu anapereka kwa ophunzira ake ndi ati?

---

3. Kodi kuchulukana ndi chani?

---

4. Kodi wokhulupirira amachulukana bwanji ku uzimu?

---

5. Perekani tanthauzo la mawu oti “njira.”

---

6. Perekani tanthauzo la mawu oti “ndondomeko za njira.”

---

7. Longosolani kutanthauza kwa mawu awa “ndondomeko za njira zochulukana ku uzimu.”

---

8. Ombani mkota pa za mfundo usodzi wa kudziko umene umapereka tanthauzo la usodzi wa ku uzimu.

---

(Mayankho a mafunsowa akupezeka kumapeto kwenkweni kwa bukuli).

## KUPITILIZA KUPHUNZIRA

Maitanidwe a Yesu ochulukana ku uzimu si oti munthu atha kusankha kapena kuganizira. Ndi lamulo ndithu. Werengani tchatili limaene likufananitsa kutuma kwakukulu kumene Baibulo limakamba. Onani mavesi onse mu Baibulo lanu. Onaninso ulamuliro umene mulinawo kuti mukwaniritse lamulolo. Onetsetsani kukula kwake kwa utumiki wanu, uthenga wake, ndi ntchito zimene mukuyenera kuchita mkatikati mochulukana.

<b>Mabuku</b>	<b>Ulamuliro</b>	<b>Kukula kwake</b>	<b>Uthenga</b>	<b>Ntchito</b>
Mateyu 28:1-20	Ulamuliro onse	Mitundu yonse	Zinthu zonse zimene Yesu Analamulira	Kupanga ophonzira pa kupita, Kubatiza kuphunzitsa
Marko 16:15	Dzina la Yesu	Dziko lonse kwa zolengedwa Zonse	Uthenga wabwino	Mukani mukalalikire, kuchiritsa odwala
Luka 24:46-49	Dzina la Yesu	Mitundu yonse kuyambira Yerusalemu	Kulapa Kukhululukidwa machimo	kulalikira kulengeza kuchita umboni
Yohane 20:21	otumidwa ndi Yesu monga Otumidwa ndi Atate	(Kukula kwa utumiki, uthenga, ndi ntchito ndi zofanana monga ngati Yesu).		
Machitidwe 1:8	Mphamvu ya Mzimu Woyera	Yerusalemu Yudeya, Samaria Ndi malekezere a Dziko lapansi	Mkhristu	Mboni

## CHAPUTALA CHA 2

### TSIKU LA ZINTHU ZOCHIPA

#### ZOLINGA:

Pakutha pa chaputalachi muyenera:

- Kulemba Vesi Lotsogolera kuchokera pamtima.
- Kuomba mkota pa za mfundo za kuchukukitsa.
- Kudziwa mitundu ya kukula mu uzimu.
- Kulemba mndandanda wa mavesi amene amasonyeza kuti kuchukana ndi za Malemba.
- Kudziwa zinthu zimene zimaoulula zolakwika zokhuza kukula mu chiwerengero.

#### VESI LOTSOGOLERA:

**Pakuti wapeputsa tsiku la tinthu tating'ono ndani? (Zakariya 4:10).**

#### MAWU OYAMBA

Kukula mu thupi la munthu kumayamba ndi dzira limodzi la moyo zimene ndi zotsatira za ubale waukulu pakati pa mkazi ndi mamuna. Dziralo limachulukana mkati mwa mmimba ya mkazi kufikira munthu wina amalengedwa. Pamene chakhwima, munthu watsopanoyi amakhalanso ndi kuthekera kochulukana.

Kukula ku uzimu kumayamba ndi ubale wa pakati pa munthu ndi Ambuye Yesu Khristu. Moyo wa uzimu umalowa mkati mwa moyo ndi mzimu wa munthu amene walandira Yesu ngati mpulumutsi. Malawi a moyo, utetezedwa mkati mwa mimba ya uzimu ya mpingo, umakula kufikira wophunzira watsopano amalengedwa. Wophunzira ameneyi amakhalanso ndi kuthekera kubadwisa ku uzimu potsogolera enanso kwa Ambuye Yesu Khristu.

Palibe kanthu ndi kudziko la kuthupi kaya la ku uzimu, kuchulukana kumayamba ndi chithu chimodzi chamoyo ngati dzira. Izi ndi zimene Mulungu ananena:

**Pakuti wapeputsa tsiku la tinthu tating'ono ndani? (Zakariya 4:10).**

Muchaputala ichi muyamba ndi zinthu zazing'ono. Muphunzira mfundo zenizeni za kuchulukana ndi mitundu ya kukula mu uzimu. Muphunziranso chidwi cha Mulungu pa kuchulukana kwa ku uzimu ndi zinthu zina zimene zimaonetsa maganizo olakwika pa kukula mu chiwerengero. Muyamba ndi mfundo zenizeni, zinthu zochepa zimene zazikulu zimachokerapo.



## **MFUNDO ZENIZENI ZA KUCHULUKANA**

Mukuyenera kumvetsa mfundo zenizeni za kuchulukana ku uzimu kuti muthe kuphunzira ndi kugwiritsa ntchito ndondomeko za njira zake. Mfundo za kuchulukana sizimasintha, komano njira zimene mumagwiritsa ntchito ndi zimene zimasintha. Njira zimasintha, koma cholinga chimakhala chomwecho chomwecho sichimasintha.

Cholinga komanso mfundo za Mulungu nthawi zonse zimakhala zomwezo, koma njira zofikira zolingazi zimasintha. Cholinga cha Mulungu kuchokera pachiyambi chakhala....

**...Kuti pa tinakonzedwe a makwaniridwe a nyengozo, akasonkhanitse pamodzi zonse mwa Kristu, za kumwamba, ndi za padziko (Aefeso 1:10).**

Monga moyo wawo wa uzimu wa anthu ake ndi masinthidwe a mbiri ya nyengo za amitundu, Mulungu amasintha njira zake monga zifunikira kuti akwaniritse cholinga chake. Mwachitsanzo, pamene atate mbanja la Israyeli analephera ntchito yawo ku uzimu, Mulungu anadzutsa ansemba. Pamene ansembe anayamba za chinyengo, anaitana aneneri kukhala ngati atsogoleri a kuuzimu.

Yesu anagwiritsa ntchito njira zosiyana za utumiki. Sanathandize anthu onse mofanana. Njira zake zinali zosiyana, koma cholinga chake chinali sichinasinthe ndiko ...Kukhudza ndi kusintha miyoyo ya anthu.

Izi ndi zina mwa mfundo zenizeni zimene mukuyenera kudzimvetsa mu “tsiku la zinthu zochepa” musanayambe kuchulukana:

### **MULUNGU AMAKHALA NDI CHIDWI NDI GULU LA ANTHU:**

Chidwi cha Mulungu nthawi zonse chakhala pa dziko lonse:

**Pakuti Mulungu anakonda dziko lapansi kotero, kuti anapatsa Mwana wace wobadwa yekha, kuti yense wakukhulupirira iye asatayike, koma akhale nao moyo wosatha (Yohane 3:16).**

Mulungu....

**...wosafuna kuti ena aonongeke, koma kuti onse afike kukulapa (II Petro 3:9).**

Yesu anaonetsa chidwi chomwecho pamene anati:

**Pakuti Mwana wa munthu anadza kufunafuna ndi kupulumutsa, cotayikaco (Luka 19:10).**

**...pakuti sindinadza kudzaitana olungama, koma ocimwa (Mateyu 9:13).**

Mulungu amakhuzidwa ndi gulu la anthu. Amakhuzidwanso ndi chiwerengero. Komanso amkhuzidwa ndi kuchulukana kwa okhulupirira amene amachulukana pa kulalikira uthenga wabwino. Pamene mukuyamba phunziro la njira zochulukitsa, muyamba ndi chidwi chomwecho ngati Mulungu—amene akufikira dziko lonse ndi uthenga wabwino.

#### **NDI MULUNGU AMENE AMABWERETSA KUKULA:**

Kuchulukana mu uzimu sikungakwaniritsidwe popandapo Mulungu. Mulungu ndiye amene amabweretsa kukula:

**...kama Mulungu anakulitsa (I Akorinto 3:6).**

#### **MUNTHU AYENERA KUGWIRIZANA NDI MFUNDO ZA MULUMGU:**

Mmawu mulu mfundo za Mulungu zimene zimagwiritsidwa ntchito mmagawo onse a moyo ndi utumiki wathu. Mulungu amagwira ntchito kudzera mwa anthu amene amadziwa kugwiriza ndi mfundozi. Kuchokera pa chiyambi cha dziko lapansi, Mulungu wakhala akugwira ntchito padzikoli kudzera mwa anthu. Adampatsa Adamu ndi Hava ntchito yosamalira munda. Anagwiritsa ntchito munthu wotchedwa Nowa kuti ateteze moyo pa dziko munthawi ya chigumula cha madzi.

Mulungu anadzutsa Abrahamu kukhala woyamba wa mtundu wa Israyeli umene kudzera mwa iye anadziululu yekha kwa mitundu ina ya dziko lapansi. Mulungu anagwiritsanso ntchito aneneri, mafumu ndi oweruza kuti akwaniritse cholinga chake mu nthawi ya Chipangano Chakale.

Muchipangano Chatsopano, munthu wotchedwa Yohane Mbatizi, “anakonzekeretsa njira ya Ambuye.” Yesu anayamba utumiki wake ndi anthu wamba ndipo pamene anabwerera kumwamba adasiya tsogolo lake la Uthenga wabwino mmanja mwa akuphunzira ake. Nkhani yonse ya Mbaibulo ndi imodzi ya kwa munthu amene akugwirizana ndi mfundo za Mulungu ndi cholinga chofuna kufikira cholinga chake.

Izi ndi zoona mu kuchulukana kwa ku uzimu. Mulungu samusiya munthu kumbali kuti afalitse mau ake. Amagwiritsa ntchito anthu amene amavetsa ndi kugwirizana ndi mfundo zake za kuchulukana. Paulo anaomba mkota za mgwirizano wa ubalewu:

**Ndinanka ine, anathirira Apolo; kama Mulungu anakulitsa (I Akorinto 3:6).**

Paulo anatsindika za change cha okhulupirira kukwaniritsa udindo wawo mu dongosolo la Mulungu.

**Pakuti, amene ali yense adzaitana pa dzina la Ambuye adzapulumuka. 14Ndipo iwo adzaitana bwanji pa iye amene sanamkhulupirira? ndipo adzakhulupirira bwanji iye amene sanamva za iye? ndipo adzamva bwanji wopanda wolalikira? Aroma (10:13-14).**

**YESU NDIYE MASO ATHU A KUCHULUKITSA:**

Yesu anati:

**Ndipo Ine, m'mene ndikakwezedwa kudziko, ndidzakoka anthu onse kwa Ine ndekha (Yohane 12:32).**

Yesu apapa amalankhula za “kukweza pamwamba” pa mtanda pamene anafera zochimwa za anthu onse. Kupyolera mu imfa yake, adzakoka anthu onse mwa mphamvu ya uthenga wake. Pamene mugawira anthu uthenga wabwino, Yesu amakwezedwa pamwamba. Pamene wakwezedwa mmoyo wanu ndi mumpingo wanu, anthu amaitanidwa ndi mphamvu ya uthenga wabwino. Kuchulukanatu ndi kotheka ngati Yesu wakwezedwa pamwamba.

**MAWU A MULUNGU AMAYAMBITSA KUKULA:**

Yesu anafotokozapo za fanizo la kukula mu Mateyu 13:1-9. Analongosola fanizolo kuyambira Mateyu 13:18-23. Werengani ndimeyi mu Baibulo lanu. Mu fanizoli, mbewu zimaimira Mau a Mulungu. Mulungu analonjeza kuti pamene tabzala Mau ake, sadzapita pachabe.

**Momwemo adzakhala mau anga amene aturuka m'kamwa mwanga, sadzabwerera kwa Ine cabe, koma adzacita cimene ndifuna, ndipo adzakula m'mene ndinawatumizira (Yesaya 55:11).**

**...Waona bwino pakuti Ine ndidzadikira mau anga kuwacita (Yeremiya 1:12).**

Mawu a Mulungu ndiwo amene amabweretsa kusintha mmiyoyo ya anthu. Kusinthako kumabweretsa kukula komanso kuchukukana molingana ndi Mau a Mulungu.

**MZIMU WOYERA AMABWERETSA KUCHULUKANA:**

Mu unthenga wake otsiriza wa Yesu kwa ophunzira ake anati:

**Komatu mudzalandira mphamvu Mzimu Woyera atadza pa inu: ndipo mudzakhala mboni zanga m'Yerusalemu, ndi m'Yudeya lonse, ndi m'Samariya, ndi kufikira malekezero ace a dziko (Machitidwe 1:8).**

Mphamvu ya Mzimu Woyera ndi imene imapangitsa kuchulukana. Mphatso za Mzimu Woyera zimakonzekeretsa kuchulukana. Chipatso cha Mzimu Woyera chimapangitsa kuberekana. Tisanthula nchito ya Mzimu Woyera mu kuchulukana kwa ku uzimu kumapeto kwa phunziroli.

### **KUCHULUKANA NDI UDINDO WOTHANDIZANA:**

Mu nthawi ya mpingo woyamba, kufalikira kwa uthenga wabwino sikunali kwa azibusa, aneneri, alaliki, ndi aphunzitsi amene anali ndi mipingo yawo ayi. Okhulupirira wina aliyense wa Chipangano Chatsopano amachulukana ku uzimu. Ngati tikufuna tifikire dziko ndi uthenga wabwino tikuyenera kuchita ngati mpingo woyamba. Kuyambira atsogoleri ndi anthu wamba akuyenera kugawana udindo wa kuchulukana ku uzimu. Kukula kwa dziko mu chiwerengero kukufunika membala wina aliyense amene ali mu thupi la Khristu kubwerera ku dongosolo la utumiki wa mu Chipangano Chatsopano. Sitingafikira dziko lapansi ndi kumangodzionetsera kapena kudzipereka mosakwanira.

Pali ndithu akhristu okwanira mu dziko lapansi amene angathe kufikira dziko lonse lapansi ndi uthenga wabwino. Koma amene akusowa ndi chiwerengero chokwanira cha akhoza kukhudzika ndi kuvomera mwayi wa kuchulukana.

Lamulo limene linaperekedwa ndi Yesu kwa okhulupirira loti “mukani” kudziko lonse ndi uthenga wabwino. Simukuyenera kudikira lamulo loti “mukani” chifukwa linaperekedwa kale. Mogwirizana ndi uthenga wabwino, lamulo ndi lakuti “mukani” ndipo penyetsetsani zoletsa, osati kusiya ndi kudikira “kumuka.”

### **MITUNDU YA KUKULA**

Baibulo limatiuza za mitundu inayi ya kukula kapena kuchulukana:

#### **KUKULA MU MADERA:**

Kukula kumeneku kunalosedwa kale ndi Ambuye Yesu:

**Komatu mudzalandira mphamvu Mzimu Woyera atadza pa inu: ndipo mudzakhala mboni zanga m'Yerusalemu, ndi m'Yudeya lonse, ndi m'Samariya, ndi kufikira malekezero ace a dziko (Machitidwe 1:8).**

Kukula kukuyenera kufikira ngakhale madera a mitundu yonse ya dziko lapansi.

### **KUKULA MU CHIWERENGERO:**

Mpingo ukuyenera kukula mu chiwerengero pamene ukukula mmadera. Kukula mu chiwerengero kwa mpingo kumapezeka mu buku la Machitidwe. Mwachitsanzo, mpingo unakula kuchokera 12 kufika 120 Machitidwe 1:15, mkuzafika 3,000 Mchitidwe 2:41 ndi kuzafika 5,000 Machitidwe 4:4.

### **KUKULA KU MITUNDU:**

Mpingo woyamba unakulanso ku mitundu. Uthenga wabwino unafalikira kupitilira Ayuda mpaka amitundu (anthu a mitundu yonse).

### **KUKULA KU UZIMU:**

Kukula mu chiwerengero si ndiye kuti ndi kukuchukana ku uzimu. Pamene mukuphunzira phunziroli, kukula ku uzimu kwa mkati ndikofunikiranso. Otsatira a Yesu akuyenera kukula mu makhalidwe a uzimu momwemonso mu chiwerengero.

**Koma kulani n'cisomo ndi cizindikiritso ca Ambure wathu ndi Mpulumutsi Yesu Khristu (II Petro 3:18).**

Khumbo la Mulungu ndi loti...

**Koma ndi kucita zooni mwa cikondi tikakule m'zinthu zonse, kufikira iye amene ali mutu ndiye Kristu (Aefeso 4:15).**

### **KUSINDIKA ZA CHIWERENGERO**

Anthu ambiri amakana nkhani ya kuchulukana ku uzimu ndi kukula kwa mpingo chifukwa amakhulupirira kuti kumakamba za chiwerengero ndi zolakwika. Komatu Mbaibulo muli mawu ambiri amene amakamba za chiwerengero. Mwachtsanzo onani Numeri 1:1-3; 2:23-24; 26:1-4; Chibvumbulutso 7:9; 20:8; Genesis 22:17; ndi Ahebri 6:14.

Yesu analankhulapo za mafanizo ambiri okhuza kukula mu chiwerengero. Muziphunzira zimenezi mu phunziro lina. Anaonetseranso kuti kukula kwenikweni kwa chiwerengero kunalembedwa Kumwamba:

**Ndinena kwa inu, koterokudzakhala cimwemwe Kumwamba cifukwa ca wocimwa mmodzi wotembenuka mtima, koposa anthu olungama makumi asanu ndi anai mphambu asanu ndi anai, amene alibe kusowa kutembenuka mtima (Luka 15:7).**

Kuchulukakanaku kumapezekanso mu mbiri ya mpingo mu buku la Machitidwe. Chidule cha kukula kwa mpingo kumapezeka mu buku la Machitidwe monga 1:15; 2:41; 4:4; 6:7; 9:31; 12:24; 16:5; 19:20; ndi 28:30-31.

Simukuyanera kukana nkhani ya kuchulukana chifukwa cha mavuto ochepa amene apezeka chifukwa cha maganizo olakwika a zakuchulukana. Komano, mukuyenera kudziwa ndi kuthana ndi mavutowo. Pali kuganiza kolakwika pa nkhani ya kuchulukana pamene zinthu izi zikupezeka:

#### **KUKULA MU CHIWERENGERO NKOFUNIKA KUPOSA KUKULA MU UZIMU:**

Pamene kukula mu uzimu kwaleka kukopa gulu la anthu, pamakhala kulakwa kolankhulano za chiwerengero. Atumiki ambiri amalankhula zimene anthu amazikonda kuzimva ndi cholinga chofuna kukopa khamu lambiri. Koma Baibulo limachenjeza kuti...

**Pakuti idzafika nthawi imene sadzalola ciphunzitso colamitsa; komatu poyabwa m'khutu adzadziuniikitsa aphunzitsi monga mwa zilakolako za iwo okha: ndipo adzalubza dala pacoonadi, nadzapatukira kutsata nthanu zacabe (II Timoteo 4:3-4).**

#### **KUDZIKWEZA KUMATSOGOLA:**

Werengani I Mbiri 21:18. Chidwi cha Davide pa chiwerengero chimogozana ndi Satana ndipo unali mchitidwe wa kudzikudza. Pamene muyamba kusangalala ndi khamu lalikulu la anthu, ndiye kuti chidwi chanu ndi cholakwika.

#### **KUDZIYENEREZA KUMAKHALAPO:**

Pali tchimo la kuthupi limeme pa Agalatiya 5:20 amalitcha kuti “kudzidierekeza” kumene ndi mchitidwe wa ngati nsanje, umene zotsatira zake ndi kuzifanizira ndi anthu ena pa nkhani ya chipambano. Pamene muli a nsanje chifukwa cha mautumiki a pamwamba ndi kuyamba kumazifanizira ndi ena ndi cholinga choti mukule, ndiye kuti muli ndi maganizo pa nkhani ya chiwerengero.

## **CHIDWI CHIMAKHALA PA KUKULA KWA MPINGO MMALO MWA UFUMU WA MULUNGU**

Cholinga cha kuchulukana mu uzimu ndiko kutembenuza anthu anthu kupita kwa Yesu Khristu ndi kuyamba kuwaphunzitsa kufikira akhala anthu odalilika, ndi wochitachita mu ufumu wa Mulungu. Pali kusiyana pakati pa kukula kwa mpingo ndi kukula kwa ufumu. Ngati mpingo woyamba ugawanika ndipo 100 mwa mamembala awo akupita ku mpingo wachiwiri, ndiye kuti kukula kwa mpingo kwachitika mu mpingo wachiwiri, koma palibe kukula kwa Ufumu. Kuchulukana sikunachitike. Kwangokhala kusinthana kwa mamembala omwe analipo kale.

Cholinga cha kuchulukana si kukopa mamembala atsopano kuchoka mu mpingo wina, koma kufikira iwo amene sanamve uthenga wabwino. Kuika chidwi pa chiwerengero ndi zolakwika pamene cholinga cha kukula kwa mpingo chikusinthana ndi kukula kwa Ufumu.

### **MUNTHU MMODZI AMAKANIDWA:**

Yesu anatumikira kwa anthu ambiri panthawi ya utumiki wake (Luka 6:17; 7:11; 8:37; 9:14-16; 14:26; 23:27; Yohane 6:2). Koma Yesu sanakane munthu ngakhale mmodzi chifukwa cha khamu la anthu. Amaitana anthu ngakhale pakati pa khamu la anthu ndi kuwatumikira (Yohane 5:3-13; Marko 5:24-34). Mu Yohane 4, anatumikira kwa mkazi mmodzi amene pamapeto pake anabweretsa khamu la mudzi wonse kwa Yesu.

Ku machitidwe 8 pali nkhani ya chitsitsimutso chachikulu chimene analalikira Filipino mu mzinda wa Samariya. Mkatikati mwa mikumano yawo Mulungu analankhula kwa Filipino kuti achoke ku Samariya ndi kupita ku chipululu pakati pa Yerusalemu ndi Gaza.

Filipo mwachangu anachoka mkusiya chitsitsimutso chachikulu chimene anatumikira. Anachoka kudziko kumene kunali anthu ambiri pamodzi mkupita kumalo ayekha. Annsiya khamu ndi cholinga chofuna kutumikira munthu mmodzi, mdindo wa ku Itopiya amane amachokera ku Yerusalemu. Munthuyi mkutheka anali ndi kuthekera kofalisa uthenga wabwino mu mbali yonse ya Afilika.

Zaka zambiri zapitazo ku Mangalande pa ntchito ya umishoni anthu awiri okha ndi amene amapezeka chifukwa cha nyengo yoipa. Mtumiki woyitanidwayo amayesera kupempha Achimwenye amane amkagwira ntchito kummawa kwa Amerika, koma anaganiza kuti amaononga nthawi chifukwa cha kuchepa kwa anthu. Koma mmodzi wa anthu awiriwa anamva kuitana kwa Mulungu ndipo anapereka moyo wake kwa Mulungu. Mwezi usanathe anagulitsa malonda ake ndipo amakonzeka kukagwira ntchito kwa Amwenye kummawa kwa Amerika. Anakhalako zaka 35 akuchita utumiki pakati pa athuwa. Dzina lake linali David Brainard.

Musanyoze zinthu zochepa. Kumbukirani, kuwala kochepe kungawale kuposa mmene dzuwa limawalira...kukhoza kuwala usiku.

### **CHIDWI CHIMACHOKA PA ANTHU MKUKHALA PA ZINTHU:**

Pamene kuchulukana kwabweretsa kukula kwa mpingo, chidwi chathu nthawi zambiri chimachoka pa anthu mkupita pa zinthu. Chifukwa cha kukula, mamangidwe a mpingo waukulu amafunika ndipo zochita zimachoka pa kuchulukitsa ophunzira mkupita pa mamangidwe a mpingo. Pamene chidwi chanu chachikulu chili pa mamangidwe ndi cholinga chofuna kukhala ndi anthu ambiri, chiwerengero chimapangitsa inu kuiwala cholinga chanu chenicheni.

Mulungu amakhuzidwa kwambiri ndi anthu kuposa mamangidwe. Mbiri ya Baibulo ya ntchito ya Mulungu mdziko imakhala pa anthu. Pamene kuchuluka kwapangitsa kuchotsa chidwi pa anthu mkuika pa zinthu monga mamangidwe, ndiye kuti zimenezi ndi zolakwika.

### **ENA AMAWERUZIDWA POYANG'ANA CHIWERENGERO:**

Sibwino kuweruza uzimu wa munthu wina kapena utumiki poyang'ana chiwerengero. Khamu lanthu si chizindikiro cha uzimu. Chipambano mu chiwerengero nthawi zina si umboni oti mpingo walephera kukhala mpingo. Nthawi zina, kukhulupirika ku Mau a Mulungu ndipo Yesu Khristu amabweza osati kukopa. Mwachitsanzo, pamene Yesu anayamba kuphunzitsa uthenga wosatchuka wa imfa yake, ambir amene amamutsata Iye amasiya kumutsata (Yohane 6:52-64).

Pali zifukwa zina zimene zimapangitsa kuti kukula kusaoneke. Baibulo limaphunzitsa kuti pali nyengo zina za kukula mu zimu monganso pali kukula kwa zinthu ku dziko. Mu dziko lathuli, nyengo zina za chaka zomera sizimaberekana. Zimakhala opanda masamba kapena zipatso mkumaoneka ngati nthambi zokufa pa nthaka. Koma mu nyengo yoyenera, zomerazi zimaberekana moti masamba komanso zipatso zimaonekera.

Momwemonso kudziko la uzimu. Pali nthawi zina pamene malo ena mdzikomu amalandira uthenga wabwino kuposa malo ena. Pa kudziwa ndandandawu wa kakulidwewu mukhoza kuika chidwi pa zochita zanu za moyo wa uzimu mmunda “kupsa mkukolora.”

Ndondomeko za chiwerengero cha Mulungu sizifanana ndi za munthu. Tipaphatikiza kuti tichukulukane. Koma nthawi zina Mulungu amachotsera ndi cholinga chofuna kuchulukana. Pamene Hananiya ndi Safira anachotsedwa mu mpingo chifukwa cha uchimo (Machitidwe 5), okhulupirira anaonjezedwa (Machitidwe 5:14). Nthawi zina Mulungu amagwiritsa ntchito mgawano pofuna kuchulukitsa. Pamene Paulo ndi Banaba anagawana, Mulungu anachulukitsa mphamvu ya umishoni (Machitidwe 15:36-41). Nthawi zambiri Mulungu amachepetsa



chiwerengero ndi cholinga chofuna kukwaniritsa cholinga chake chachikulu. Werengani nkhani ya Gideoni mu Oweruza 7.

Musaweruze utumiki kapena munthu poyang'ana chiwerengero. “Osapeputsa zinthu zochepa. Pamene mnyamata anapereka mkatendi nsomba ziwiri kwa Yesu, zinafikira chosowa cha khamu la anthu amene anali ndi njala. Mulungu amagwiritsa ntchito zinthu zonyozeka, mkuzidalitsa, ndi kudzigwiritsa ntchito ku ulemerero wa dzina lake.

### **ZOTSATIRA ZAKE NDI KUBWERETSA KHOLOLA**

Pokana maganizo olakwikwa otsindikiza za chiwerengero zisalepheretse maphunzirowa ndi kugwiritsa ntchito njira za kuchulukutsa. Fanizo la (Mateyu 25:14-30) likuonetseratu kuti Mulungu amayembekezera inu kuti muchulukane ndi zimene mwapatsidwa choncho kukhala ndi madandaulo chifukwa cha mantha sizoloredwa.

**Kodi simunena inu, kuti, Yatsala miyezi inai, ndipo kudza kumweta? Onani ndinena kwa inu, Kwezani maso anu, nimuyang'ane m'minda, kuti mwayera kale kufikira kumweta (Yohane 4:35).**

Pamene Mulungu atumiza okolola mmunda wa uzimu ku dziko, amafuna iwo abwere ndi kholola osati madandaulo:

**Akubzala ndi misozi adzatuta ndi kupfuula mokondwera.**

**Iye amene ayendayenda nalira, ponyamula mbeu yakufesa;  
Adzabweranso ndithu ndi kupfuula mokondwera, alikunyamula mitolo yace  
(Masalmo 126: 5-6).**

## MAYESO ODZIYETSA NOKHA

1. Lembani Vesi Lotsogolera kuchokera pantima.

---

2. Lembani mfundo zenizeni za kuchulukitsa zimene mwaphunzira mu phunziroli.

---

3. Tchulani mitundu inayi ya kukula mu uzimu.

---

---

---

4. Lembani mavesi amene amaonetsa chidwi kuti kuchulukana ndi zochokera Mmalemba.

---

5. Lembani mwachidule zinthu zimene mwaphunzira zosonyeza kuganiza kolakwikwa pa kukula mu chiwerengero.

---

6. Zoonu kapena Zonama: ngati chiganizo chili choona, lembani “zoonu” mumpata koyambirira kwa chiganizo. Ngati chiganizo chili chonama, lembani “zonama mumpata.”

a. \_\_\_\_\_ Amaika chidwi pa chiwerengero si za Mmalemba.

b. \_\_\_\_\_ Ngati mpingo sukukula, ndiye kuti uzimu palibe.

(Mayankho a mafunsowa akupezeka kumapeto kweikweni kwa bukuli).

## KUPITILIZA KUPHUNZIRA

Buku la Machitidwe limatiuza nkhani ya kuchulukana kwa mpingo woyamba. Gwiritsani ntchito magawowa kuti muphunzire bukuli la Chipangano Chatsopano. Magawowa amatsata dongosolo la kuchulukana la Ambuye limene limnaperekedwa pa Machitidwe 1:8 pa za kufalitsa uthenga wabwino kuchokera ku Yerusalemu, kupita ku Yudeya, Samariya, ndi malekedzero a dziko lapansi.

**Wolembe buku:** Luka

**Kumene amalemba:** Bukuli amalemba okhulupirira onse, ngakhale amalemba kwa munthu wotchedwa Tiofelo.

**Cholinga chimene amalemba buku:** Ichi chikupezeka mu Machitidwe 1:1-2. Bukuli limaika chidwi pa zimene Yesu anapitiliza kuchita ndi kuphunzitsa atangokwera kupita kumwamba mu thupi lake la uzimu, ndiye Mpingo.

**Vesi Lotsogolera:** Machitidwe 1:8

### Mawu oyamba

Machitidwe 1:1-11

I. Mawu oyamba: 1:1-2

A. Kwa: Teofelo: 1:1

B. Okhuzana: Zimene Yesu adapitiliza kuchita ndi kuphunzitsa atangopita kumwamba mu thupi lake la ulemerero, Mpingo: 1:1-2

II. Utumiki wa Yesu atatha kuukitsidwa: 1:3

A. Masiku ake: Makumi anayi: 1:3

B. Cholinga chake: Zitsikimizo zosakaikitsa: 1:3

C. Uthenga wake: Ufumu wa Mulungu: 1:3

III. Mkumano wotsiriza wa Yesu ndi akuphunzira ake: 1:4-8

- A. Lamulo la ophunzira: 1:4-5
- B. Funso la ophunzira: 1:6
- C. Chenjezo kwa ophunzira: 1:7
- D. Kutuma ophunzira: 1:8

IV. Kukwera kwa Yesu kupita kumwamba: 1:9-11

- A. Kulongosola za kukwerako: 1:9
- B. Kulengeza za kubwera kwake kwachiwiri: 1:10-11

**Gawo Loyamba:**  
**Kupanga mboni ku Yerusalemu**  
**Machitidwe 1:12-7**

I. Kukonzekeretsa mboni: 1:12-2:4

A. Ophunzira aYesu kudikirira ku Yerusalemu: 1:12-26

1. Kusunkhana kwa ophunzira: 1:12-15

- a. Malo awo okumaniranapo: 1:12-13
- b. Chiwerengero chawo ndi mayina awo: 1:13-15
- c. Cholinga chawo: 1:14

2. Chilimbikitso chopita kwa ophunzira: 1:15-22

- a. Wolankhula: Petulo: 1:15
- b. Uthenga 1:16-22
  - (1) Chiyambi: 1:16-20
  - (2) Malangizo: 1:21-22

3. Yankho la akuphunzira: 1:23-26

- a. Maina oti asankhidwe: 1:23
- b. Pemphero: 1:24-25
- c. Maere: 1:26

B. Ubatizo mwa Mzimu Woyera: 2:1-4

- 1. Mmene zinakhalira: 2:1
- 2. Anthu: 2:1
- 3. Malo ake: 2:1
- 4. Chochitikacho: 2:2-4
  - a. Mphepo: 2:2

- b. Malilime a moto: 2:3
- c. SKulankhula: 2:4

**Gawo Lachiwiri: Ntchito yochitira umbini ku Yerusalemu  
Machitdwe 2:5-7**

I. Mboni zoyamba: 2:4-40

- A. Mmene umboni unaperekedwera: 2:4-6
- B. Zotsatira za umboni: 2:7-13
- C. Ulaliki wa Petulo: 2:14-36
  - 1. Uneneri wokhuzana ndi nthawi: 2:17
  - 2. Uneneri wokhuzana ndi mzimu: 2: 17-18
  - 3. Uneneri wokhuzana ndi chochitikacho: 2:19-20
  - 4. Uneneri wokhuzana ndi chipulumutso: 2:21
  - 5. Ntchito ya Yesu: 2:22-36
    - a. Yesu adatsimikizidwa ndi Mulungu: 2:22
    - b. Yesu adapachikidwa: 2:23
    - c. Yesu adauka kwa akufa: 2:24-32
    - d. Yesu adakwezedwa pa dzanja lamanja la Mulungu: 2:33-35
    - e. Yesu ndi Mbuye ndi Khristu: 2:36
- D. Zotsatira atamva uthenga: 2:37-40
  - 1. Kutsutsika: 2:37
  - 2. Kufunsa: 2:37
  - 3. Langizo: 2:38
  - 4. Malonjezo: 2:38-39
  - 5. Chilimbikitso: 2:40

II. Mpingo woyamba: 2:41-47

- A. Chiwerengero cha anthu mu mpingo woyamba: 2:41
  - 1. Chizindikiro chawo: Iwo amene adalandira Mawu.
  - 2. Chiwerengero chinali: Zikwi zitatu 3,000
- B. Makhaliidwe a Uzimu a mpingo woyamba: 2:42
  - 1. Chiphunzitso cha atumwi.
  - 2. Chiyanjano cha oyera mtima.
  - 3. Mgonero.
  - 4. Pemphero.
- C. Chikhalidwe cha mpingo woyamba: 2:44-46

1. Machitdwe awo a moyo watsiku ndi tsiku: 2:44-45
2. Kulambira ndi kuchitira umboni tsiku ndi tsiku: 2:46
3. Kuchita chiyanjano mmanyumba: 2:46
4. Umodzi: 2:46

D. Umboni wa mpingo watsopano: 2:46-47

1. Chikhalidwe cha umboni: 2:46-47
2. Zotsatira za umboni: 2:47

III. Chozizwa choyamba: 3:1-26

A. Mmene chozizwa chinalili: 3:1-11

1. Malo ake: 3:1
2. Munthu ndi chosowa chake: 3:2-3
3. Uthenga: 3:4-6
4. Chozizwa: 3:7-8
5. Zimene khamu linachita: 3:9-11

B. Kulongosola chozizwa: 3:12-18

1. Munthuyo sanachiritsidwe ndi mphamvu ya atumwi: 3:12
2. Munthuyo anachiritsidwa ndi Mulungu kuti apereke ulemerero kwa Yesu: 3:13-15
3. Munthuyo anachiritsidwa mwa chikhulupiriro mdzina la Yesu: 3:16
4. Munthuyo anachiritsidwa kuti akaonetsere kukwaniritsidwa kwa uneneri: 3:17-18

C. Uthenga wa Petulo: 3:19-26

1. Lonjezo limene Petulo adalinena: 3:19-21
  - a. Chimene Mulungu adatsimikizira Israyeli kuchita: 3:19
  - b. Chimene Mulungu adalonjeza kuchita: 3:19-21
2. Uneneri wa aneneri: 3:22-26
  - a. Uneneri wa Mose ndi aneneri: 3:22-24
  - b. Lonjezo la pangano: 3:25
  - c. Dongosolo la Mesiya: 3:26

IV. Chitsutso choyamba: 4:1-31

A. Kumangidwa: 4:1-4

1. Choyambitsa chitsutso: 4:1
2. Cholinga cha chitsutso: 4:2
3. Mtundu wa chitsutso: 4:3

B. Kuyesedwa: 4:5-14

1. Kubwalo la milandu: 4:5-6
2. Mafunso akubwalo la minlandu: 4:7
3. Mawu a Petulo: 4:8-12
  - a. Maziko a yankho lake: 4:8
  - b. Yankho lake: 4:9-10
  - c. Umboni wake wa Yesu: 4:10-12
  - d. Chilengezo chake cha chipulumutso: 4:12
4. Umboni wa oweruza milandu: 4:13-14
  - a. Chikhalidwe cha umboni: 4:13
  - b. Umboni wa munthu amene anachiritsidwa: 4:14
5. Chisankho: 4:15-22
  - a. Kufuna uphungu: 4:15-17
  - b. Chisankho: 4:17-18
  - c. Yankho la Petulo ndi Yohane: 4:19-20
  - d. Kumasulidwa: 4:21-22
6. Zimene adachita: 4:21-31
  - a. Pemphero la mpingo: 4:23-30
  - b. Ntchito ya mpingo: 4:31

V. Mwambo oyamba wa tchimo: 4:32-5:16

A. Dongosolo la mpingo: 4:32-37

1. Chiyanjano chake: 4:32
2. Umboni wake: 4:33
3. Chuma chake: 4:32-37

B. Tchimo loyamba ndilo loononga chiyanjano: 5:1-10

1. Tchimo: 5:1-2
2. Kuonekera poyera kwa tchimo: 5:3-4
3. Mwambo wake wa tchimo: 5:5-10

C. Zotsatira za mwambo: Umboni wobala chipatso wa chiyanjano: 5:11-16

1. Malingaliro a mantha a mamembala: 5:11
2. Umodzi: 5:12
3. Zozizwa: 5:12, 15-16
4. Zomwe anthu adachita: 5:12-14

VI. Chizunzo choyamba: 5:17-43

- A. Maziko a chitsutso: 5:17
- B. Zotsatira za chitsutso: 5:18
- C. Chiombolo cha Mulungu: 5:19-26
  - 1. Ntchito Zake: 5:19
  - 2. Lamulo Lake: 5:20
  - 3. Zomwe adachita ndi lamulo Lake: 5:21
  - 4. Kuzindikira ntchito zake: 5:21-23
  - 5. Zotsatira za ntchito Zake: 5:24-26
- D. Kuyesedwa: 5:27-40
  - 1. Lamulo la akuluakulu: 5:27-28
  - 2. Chozitchinjiriza cha Petulo: 5:29-32
  - 3. Kusanthula kwa akuluakulu: 5:33-39
  - 4. Chisankho chosalungama cha akuluakulu: 5:40
- E. Zotsatira za chizunzochi: 5:41-42
  - 1. Chikondwerero: 5:41
  - 2. Umodzi: Kukumana tsiku ndi tsiku limodzi: 5:42
  - 3. Kuchitira umboni: Kuphunzitsa ndi Kulalikira: 5:42

VII. Atumiki oyamba: 6:1-7

- A. Kufunikira kwa atumikiwo: 6:1
- B. Atumikiwo anasankhidwa: 6:2-4
  - 1. Maziko a kusankhidwako: 6:2
  - 2. Cholinga cha kus: 6:2 ankhidwako
  - 3. Chisankhocho: 6:3
  - 4. Kufunikira kwa kusankhidwako: 6:4
- C. Atumiki akhazikitsidwa: 6:5-6
  - 1. Njira zomwe zidatsatidwa: 6:5-6
  - 2. Amuna anasankhidwa: 6:5
  - 3. Kuzozedwa kwao: 6:6
- D. Zotsatira za atumikwo: 6:7
  - 1. Mawu anachulukitsidwa: 6:7
  - 2. Ophunzira anachuluka: 6:7
  - 3. Kumvera ku chikhulupiro: 6:7

VIII. Wophedwa woyamba kamba ka chikhulupiro: 6:8-8:1



- A. Mmene analili Stefano: 6:3-15
  - 1. Mmodzi wa asanu ndi awiri: 6:3,5
  - 2. Wozazidwa ndi Mzimu Woyera: 6:5
  - 3. Munthu wa mbiri yabwino: 6:3
  - 4. Munthu wa chikhulupirio: 6:5
  - 5. Munthu wa nzeru: 6:3, 10
  - 6. Munthu wa mphmvu: 6:8
  - 7. Mboni yadalilika: 6:9-10
- B. Chizunzo cha Stefano: 6:11-15
- C. Uthenga wa Stefano: 7:1-53
  - 1. Abrahamu: 7:1-8
  - 2. Makolo a Mchipangano chakale: 7:9-16
  - 3. Mose: 7:17-43
    - a. Ku Aigupto: 7:17-28
    - b. Muchipululu: 7:29-43
  - 4. Chihema: 7:44-50
    - a. Cha Mose: 7:44
    - b. Cha Yoswa: 7:45
    - c. Cha Davide: 7:45-46
    - d. Cha Solomoni: 7:47-50
    - e. Cha Mulungu: 7:48-50
  - 5. Aneneri: 7:51-53
- D. Umboni wa Stefano: 7:54-8:1
  - 1. Malingaliro a akuluakulu: 7:54
  - 2. Chilengezo cha Stefano: 7:55-56
  - 3. Zomwe akuluakulu anachita: 7:57-59
  - 4. Imfa ya Stefano: 7:59-8:1

**Gawo Lachitatu: Umboni wa ku Yudeya ndi ku Samariya  
Machitidwe 8-12**

- I. Kusintha: Zotsatira za imfa ya Stephano: 8:1-4
  - A. Chizunzo: 8:1,3
  - B. Kuikidwa mmanda kwa Stefano: 8:2
  - C. Umboni wopitirira wa mpingo: 8:4
- II. Umboni wa Filipo: 8:5-40
  - A. Utumiki wa ku Samariya: 8:5-25

1. Umboni wa Filipo: 8:5-13
  - a. Ntchito ya Filipo: 8:5-7, 12
  - b. Zimene a Samaliya adachita: 8:6-12
  - c. Simoni wa nyanga: 8:9-13
2. Ntchito ya Petulo ndi Yohane: 8:14-17
  - a. Kubwera kwa Petulo ndi Yohane: 8:14
  - b. Kubwera kea Mzimu Woyera: 8:15-17
  - c. Zimene Simoni adachita: 8:18-19
  - d. Chenjezo la Simoni: 8:20-24
- B. Utumiki wa ku Aitiyopiya: 8:26-40
  1. Kukonzekera: 8:26-28
  2. Umboni: 8:29-35
  3. Zomwe adachita: 8:36-38
- C. Kusintha kupita ku Azotu: 8:39-40

### III. Umboni wa Saulo: 9:1-31

- A. Kusanthulika mtima kwa Saulo: 9:1-9
  1. Cholinga chake: 9:1-2
  2. Masomphenya ake: 9:3-9
  3. Mawu ake: 9:4-7
  4. Kuchita khungu: 9:8-9
- B. Kutumidwa kwa Saulo kudzera kwa Hananiya: 9:10-19
  1. Maitanidwe: 9:10-16
  2. Kutumidwa: 9:17-19
- C. Ntchito ya Saulo: 9:20-31
  1. Saulo ku Damasiko: 9:20-25
    - a. Umboni wake: 9:20-22
    - b. Zimene adachita: 9:21-23
    - c. Kuthawa kwake: 9:23-25
  2. Saulo ku Yerusalemu: 9:26-30
    - a. Kulandiridwa kwake: 9:26-28
    - b. Ntchito yake: 9:28-29
    - c. Kuchoka kwake: 9:29-30
- D. Kusintha: Mpukulo mu mpingo: 9:31

### IV. Umboni wa Petulo: 9:32-12:35

- A. Ku Luda: 9:32-35
  - 1. Okhulupirira: 9:32
  - 2. Munthu wodwala: 9:33
  - 3. Kuchiritsidwa kwa munthu wodwala: 9:34
  - 4. Zomwe adachita: 9:35
- B. Ku Yopa: 9:36-43
  - 1. Imfa ya Dorika: 9:36-37
  - 2. Kuitanidwa kwa Petulo: 9:38-39
  - 3. Utumiki wa Petulo: 9:40-41
  - 4. Zotsatira za utumiki: 9:42-43
- C. Ku Kaisareya: 10:1-48
  - 1. Masomphenya a Koneriyo: 10:1-8
    - a. Koneriyo: 10:1-2
    - b. Masomphenya a Koneriyo: 10:3-6
    - c. Zomwe adachita Koneriyo: 10:7-8
  - 2. Masomphenya a Petulo: 10:9-22
    - a. Msomphenya: 10:9-12
    - b. Kulankhula: 10:13-16
  - 3. Kufika kwa otumidwa: 10:17-22
  - 4. Kufika kunyumba ya Koneriyo: 10:23-48
    - a. Ulendo: 10:23
    - b. Kulandiridwa: 10:24-27
    - c. Chilongosolo: 10:27-28
    - d. Funso: 10:29
    - e. Yankho: 10:30-33
    - f. Ulaliki osamalizitsa: 10:34-43
      - (1) Mulungu opanda tsankhu: 10:34-35
      - (2) Kufalikira kwa Uthenga wabwino: 10:36-37
      - (3) Uthenga wa uthenga wabwino: 10:38-43
    - g. Zimene Koneriyo adachita: 8:44-48
- D. Ku Yerusalemu: 11:1-12:25
  - 1. Vuto lobwera kamba ka kusandulika kwa a mitundu: 11:1-18
    - a. Vuto lake: 11:1-3
    - b. Kulongosola ntchito ya Mulungu pakati a mitundu: 11:4-17
      - (1) Masomphenya: 11:4-10
      - (2) Alendo: 11:11
      - (3) Ulendo: 11:12-16
    - c. Chisankho: 4:18

V. Mpingo wa ku Antiokeya ku Asuri: 11:19-30

- A. Chitsitsimutso cha ku Antiokeya: 11:19-21
- B. Kufika kwa Banaba: 11:22-24
- C. Saulo asankhidwa ngati mbusa wophunzitsa: 11:25-26
- D. Zimene Agabo anaulula: 11:27-30

VI. Chizunzo cha Herode: 12:1-25

- A. Kuphedwa kwa Yakobo: 12:1-2
- B. Kumangidwa kwa Petulo: 12:3-4
- C. Kumasulidwa kwa Petulo 12:5-19
- D. Imfa ya Herode: 12:20-23

VII. Kulalikidwa kwa Mawu: 12:24-25

**Gawo Lachinayi: Umboni ku dziko lonse lapansi  
Machitidwe 13-28**

I. Ulendo woyamba wochita utumiki: 13:1-14:28

- A. Kuitanidwa ku utumiki: 13:1-3
- B. Utumiki ku Pafo wa ku Ku: 13:4-12
- C. Utumiki ku Antiokeya wa Mpisidiya: 13:13-50
  - 1. Kupita ku Pisidiya: 13:13-16
  - 2. Uthenga: 13:17-37
    - a. Chipulumutso cha mu Eksodo: 13:17
    - b. Ulendo wa mu Chipululu: 13:18
    - c. Kugonjetsa Kanani: 13:19
    - d. Ulamuliro wa Saulo ndi Davide: 13:20-23
    - e. Utumiki wa Yohane Mbatizi: 13:24-25
    - f. Kupachikidwa ndi kuuka Kwa Yesu: 13:26-37
    - g. Kuitanidwa: 13:38-41
  - 3. Mmene adayankhira kuitanako: 13:42-50
- D. Utumiki ku Ikoniyo: 13:51-14:5
- E. Utumikiku Lustra: 14:6-25
- F. Utumiki ku Antiokeya: 14:26-28

II. Mkumano wa akuluakulu ku Yerusalemu: 15:1-35

- A. Vuto lake: 15:1-3
- B. Mkumano wa akuluakulu: 15:4-21
  - 1. Mkumano woyamba: 15:4-5
  - 2. Mkumano wa mseli wa atumwi ndi akuluakulu: 15:6
  - 3. Mkumano wachiwiri: 15:7-21
    - a. Uthenga wa Petulo: 15:7-11
    - b. Uthenga wa Paulo ndi Banaba: 15:12
    - c. Uthenga wa Yakobo: 15:13-21
- C. Chisankho: 15:19-21
- D. Makalata: 15:22-35

III. Ulendo wachiwiri wa utumiki: 15:36-18:22

- A. Kutsutsana: 15:36-41
- B. Utumiki wa ku Lustra: 16:1-5
- C. Utukiwa wa ku Trowa: 16:6-10
- D. Utumiki wa ku Filipo: 16:11-40
- E. Utumiki wa ku Tesalonika: 17:1-9
- F. Utumiki wa ku Bereya: 17:10-14
- G. Utumiki wa ku Atene: 17:15-34
- H. Utumiki wa ku Korinto: 18:1-18
- I. Utumiki wa ku Efeso: 18:19-21
- J. Yerusalemu ndi Antioki: 18:22

IV. Ulendo wachitatu wa utumiki: 18:23-21:14

- A. Ku Galatiya: 18:23
- B. Utumiki wa ku Efeso: 18:24-19:41
  - 1. Apolosi: 18:24-28
  - 2. Ophunzira a Yohane: 19:1-7
  - 3. Sukulu ya ku Turano: 19:8-12
  - 4. Ana a Skeva: 19:13-17
  - 5. Kupereke otembenuka: 19:18-20
  - 6. Chisankho: 19:21
  - 7. Otchinjiriza Demetriyo: 19:23-41
- C. Utumiki wa ku Makedoniya ndi ku Helene: 20:1-5

- D. Utumiki wa ku trowa: 20:6-12
- E. Utumiki wa ku Mitilene: 20:13-38
  - 1. Ulendo: 20:13-16
  - 2. Mkumano ndi akuluakulu a ku Efeso: 20:17-35
    - a. Kuunika utumiki wake: 20:17-21
    - b. Kuona za kutsogolo: 20:22-24
    - c. Chikumbumtima cha Paulo: 20:25-27
    - d. Chenjezo 20:28-31
    - e. Kuvomerezeka kwa Mulungu: 20:32
    - f. Chitsanzo cha Paulo mu mtsautso: 20:33-35
  - 3. Kusanzikana: 20:36-38
- F. Utumiki wa ku Turo: 21:1-6
- G. Utumiki wa ku Ptolemai: 21:7
- H. Utumiki wa ku Kaesareya: 21:8-14

V. Ulendo wotsiriza wa ku Yerusalemu ndi kwa Aroma: 21:15-28:31

- A. Yerusalemu: 21:15-23:32
  - 1. Kusintha kupita ku Yerusalemu: 21:15-17
  - 2. Mphekesera zosutsana ndi Paulo: 21:18-30
    - a. Kuti anaphwanya chilamulo cha Mose: 21:18-26
    - b. Kuti anadetsa malo oyera: 21:27-30
  - 3. Zimene Paulo adachita: 21:23-26
  - 4. Kupulumuka kwa Paulo: 21:30-32
  - 5. Zimene Paulo adayankha: 21:33-23:10
    - a. Khamu la Chiyuda: 22:1-23
    - b. Kenturiyo wa Chiroma: 22:24-26
    - c. Kapitao wamkuru: 22:26-30
    - d. Bwalo la akuru: 23:1-10
      - (1) Chivomerezo cha Paulo: 23:1
      - (2) Kukumana ndi Mkulu wansembe: 23:2-5
      - (3) Kugawanika kwa bwalo: 23:6-10
  - 6. Chivumbulutso kwa Paulo: 23:11
  - 7. Chiwembu chofuna kupha Paulo: 23:12-15
  - 8. Kupulumuka kwa Paulo: 23:16-32
    - a. Chiwembu chiululika: 23:16-22
    - b. Kalata: 23:25-30
    - c. Kuthawa: 23-32

- B. Ku Kaesareya: 23:33-26:32
  - 1. Pa maso pa Felike: 23:33-24:27
    - a. Chitsutso cha Tertulo: 24:1-9
    - b. Yankho la Paulo: 24:10-21
    - c. Yankho la Felike: 24:22-27
  - 2. Pamaso pa Festo: 25:1-12
  - 3. Felike ndi Agripa: 25:13-27
  - 4. Pamaso pa Agripa: 26:1-32
    - a. Paulo adzilankhulira yekha: 26:1-23
    - b. Kuitanira ku chipulumutso: 26:24-29
    - c. Chigamulo: 26:30-32
- C. Ulendo wa kwa Aroma: 27:17-28:31
  - 1. Mafunde: 27:1-44
  - 2. Njoka: 28:1-6
  - 3. Machiritso: 28:7-10
  - 4. Ulendo upitilira: 28:11-15
- D. Kwa Aroma: 28:16-31
  - 1. Mkumano ndi Ayuda: 28:16-29
  - 2. Utumiki: 28:30-31

## CHAPUTALA CHA 3

### MAFANIZO A KUCHULUKITSA

ZOLINGA:

Pakutha pa chaputachi muyenera:

- Kulemba Vesi Lotsogolera kuchokera pantima.
- Kupereka tanthauzo la mawu oti “fanizo.
- Kulongosola chifukwa chimene Yesu amagwiritsa ntchito mafanizo.
- Kuzindikira mfundo za kuchulukitsa mu mafanizo amene Yesu amaphunzitsa.

**VESI LOTSOGOLERA:**

**Ndipo ndi mafanizo otere ambiri analankhula nao mau, monga anakhoza kumva; (Marko 4:33).**

### MAWU OYAMBA

Phunziroli likukhazikika pa mfundo za kuchulukana molingana ndi mmene Yesu anaphunzitsira pa utumiki wake. Fanizo ndi nkhani imene imakamba zitsanzo zochokera ku dziko limene timakhala pofuna kuonetsera choonadi ku uzimu.

Tanthauzo lenileni la mawu oti “fanizo” ndi “kuika pambali, kufanizira.” Mu mafanizo, Yesu amafanizira zitsanzo za kudziko ndi choonzdi cha uzimu. Fanizo ndi nkhani yochitika kudziko imene ili ndi tanthauzo ku uzimu.

### CHIFUKWA CHIYANI MAFANIZO

Ophunzira ake nthawi ina anamufunsa Yesu chifukwa chimene amagwiritsa ntchito mafanizo pofuna kuphunzitsa choonadi cha uzimu.

**Ndipo ophunzirawo anadza, nati kwa Iye, Cifukwa canji muphiphiritira iwo m'mafanizo? (Mateyu 13:10).**

Yesu anayankha:

**Ndipo Iye anayankha nati, Cifukwa kwapatsidwa kwa inu kudziwa zinsinsi za Ufumu wa Kumwamba, koma sikunapatsidwa kwa iwo (Mateyu 13:11).**

Kumvetsetsa choonadi ku uzimu chimene chaphunzitsidwa mu fanizo zinapatsidwa kwa ophunzira chifukwa anali ndi maganizo a uzimu. Amene analibe maganizo a uzimu mkumamva mafanizo amalephera kumvetsetsa. Choonadi chauzimu chimveka ndi maganizo a uzimu:



**Koma munthu wa cibadwidwe ca umunthu salandira za Mzimu wa Mulungu: pakuti aziyesa zopusa; ndipo sakhoza kuzizindikira, cifukwa ziyesedwa mwauzimu (I Akorinto 2:14).**

Munthu wa maganizo a uzimu ndi amene wabadwanso mwatsopano ku uzimu. Amene ali ndi maganizo a uzimu amamvetsa mfundo zimene zimachokera mmaganizo. Amene ndi anthupi, a maganizo a uchimo sangamvetse.

### **UTHENGA WABWINO WA UFUMU**

Pamene Yesu anatuma akuphuzira ake kupita kudziko lonse kukalalikira uthenga wabwino, Anati kwa iwo...

**Ndipo uthenga uwu wabwino wa Ufumu udzalalikidwa pa dziko lonse lapansi, ukhale mboni kwa anthu a mitundu yonse; ndipo pomwepo cidzafika cimariziro (Mateyu 24:14).**

Uthenga wabwino umene mukuyenera kufalitsa kudziko lapansi ndi uthenga wabwino wa ufumu. Ndi uthenga umene ndi wa kubadwa, moyo ndi utumiki wa Yesu. Komanso ndi uthenga wa imfa ya machimo a anthu onse ndi kuuka kwake kuchokera ku imfa. Mukuyenera kuuza anthu za mmene anthu za mmene angalowere mu ufumu wa Mulungu kudzera mu kubadwanso ku uzimu ndi kuwaphuzitsa mmene angakhalire moyo watsopano wa ufumu.....

### **MAFANIZO A KUCHULUKANA**

Yesu anaphuzitsa mafanizo ambiri okhudza ufumu wa Mulungu. Ena mwa iwo anali mafanizo a mmene ufumu ungafalikire ku dziko lonse lapansi. Mafanizo ali mmusiwa okhudza kukula kwa Ufumu amaululu mfundo za kuchulukana. Onani ndi kuwerenga mafanizowa Mbaibulo lanu:

**Nkhosa yosochera:** Mateyu 18:12-14; Luka 15:4-7

**Ndalama yotaika:** Luka 15:8-10

**Mwana olowerera:** Luka 15:11-32

Mafanizowa amaululu chidwi cha Mulungu pa otaika ndi change chowafuna kuti abwerere mu Ufumu wa Mulungu. Sizitengera chifukwa chimene anataikira. Nkhosa zinasochera kutali. Ndalama inataika chifukwa cha kusasamala. Mwana anasochera chifukwa cha kugalukira kwake. Mukuyenera kuchita mmene mungathere kuti mupeze otayika mu uchimo. Pitani kumene amapezeke, osadikiraiwo kuti akupezeni. Mulungu sakhudzidwa ndi mmene anataikira, komatu kuti apezeke basi.

**Phwando lalikulu lopanda kanthu:** Luka 14:15-23

Kuchulukana kusathe chufukwa choti ena akana atatha kuyitamidwa ku uthenga wabwino. Mukuyenera kuwafuna iwo amene ali ndi njala ya uzimu, ndi kwabweretsa ku phwando lokonzedwa ndi Ambuye.

**Mkuyu wosabala:** Luka 13:6-9

Yesu anawauza fanizo la mkuyu wosabala. Mtengo wamkuyu ndi chizindikiro chooneka cha mtundu Israyeli. Mulungu anakweza Israyeli ngati mtundu umene kudzera mwa iye adzaululu Ufumu wa Mulungu ku dziko. Mulungu anayetsesa kupeza “mtengo” wa Israyeli kuti ukabale “zipatso” pakati pa mitundu yosadziwa Mulungu pakugawana nawo chidziwitso cha Mulungu woona. Mulungu sakondwera ndi mitengo imene sibala zipatso.

**Matalente:** Mateyu 25:14-30; Luka 19:11-27

**Munthu wa pa ulendo wautali:** Marko 13:34-37

**Akapolo:** Mateyu 24:43-51; Luke 12:39-46

**Akapolo oyang'anira:** Luka 12:36-38

**Woyang'anira wokhulupirika:** Mateyu 25:14-30

Mafanizo a “akapolowa” amaika chidwi pa mdindo woyang'anira wamzeru pa uthenga wa Ufumu umene waperekedwa kwa okhulupirira. Wokhulupirira aliyense papatsidwa “matalente” kapena kuthekera kwapaderadera koti agwiritse ntchito polalikira uthenga wabwino. Kaya kuthekera kwanu nkochepe kapena kwakukulu, mukuyenera kuchulukitsa zimene Mulungu wakupatsani.

Kapolo aliyense akuyenera kuchuluka. Pamene Yesu adzabwerera ku dziko lapansi, iwo amene agwiritsa ntchito mphoto zawo moyenera adzapatsidwa mphoto (Luka 16:10-12). Iwo amene sakuchulukana amayesedwa osakhulupirika:

**Pakuti Mwana wa munthu adzabwera mu ulemerero wa Atate wace, pamodzi ndi angelo ace; ndipo pomwepo Iye adzabwezera kwa anthu onse monga macitidwe ao (Mateyu 16:27).**

Yesu amadziwa mfundo ya muyeso pa kuchulukana:

**Koma iye amene sanacidziwa, ndipo anazicita zoyenera mikwapulo, adzakwapulidwa pang'ono. Ndipo kwa munthu ali yense adampatsa zambiri, kwa iye adzafuna zambiri; ndipo amene anamuikizira zambiri, adzamuuzza abwezere zoposa (Luka 12:48).**

Ufumu wa Mulungu umafalikira pakugwiritsa ntchito luso la uzimu lopatsidwa ndi Mulungu. Ngati mugwiritsa ntchito zimene Mulungu wakupatsani, luso lanu lidzachuluka. Ndipo ngati simuligwiritsa ntchito adzkulandani.

**Wofetsa:** Mateyu 13:3-8; Marko 4:3-8; Luka 8:5-8

Uthenga wa Ufumu umafalikira pofesa mbewu ya Mau a Mulungu. Sipangakhale kuchulukana popanda Mau a Mulungu. Zipatso zimatengera moyo umene uli mu mbewu (amene ndiwo Mau a Mulungu) ndi mmene nthaka ikuchitira (ndi mmene munthu achitira akamva Mau a Mulungu). Pamakhalamachitidwe osiyana pamene mbewu ya Mau ikufetsedwa.

Udindo wanu ndi kungofetsa. Pamene mufetsa mbewu ya Mau a Mulungu, nthaka idzakonzeka ndi kupereka zokolola. Nthaka ina imalephera kupereka zochuluka. Ngakhale Yesu anakumana ndi nthaka yokanika pa nthawi ya utumiki wake.

**Ndipo kumeneko sanakhoza Iye kucita zamphamvu konse, koma kuti anaika manja ace pa anthu odwala owerengeka, nawaciritsa.**

**Ndipo anazizwa cifukwa ca kusakhulupirira kwao (Marko 6:5-6).**

**Nansongole ndi Tirigu:** Mateyu 13:24-30

Pamene mukuchulukitsa Ufumu wa Mulungu pa kuonjezereka kwa okhulupirira atsopano, Satana nayenso amayesera kugonjetsa ntchitoyo. Adzadzala anthu amene adzakhala ngati Nansongole pakati pa mbewu zabwino za Ufumu wa Mulungu.

Anthu ena amene amavomereza kukhala okhulupirira ndi kuyamba kubwera mu mpingo mu njira yochulukitsa, nthawi zina sakhala oona mtima. Amakhala nansongole odzalidwa ndi Satana.

Yesu safuna muwononge nthawi yanu kusiyanitsa pakati pa nansongole ndi tirigu. Pitolirani kudzala mbewu ndi kuchulukana. Pa tsiku lokolola pamene Yesu adzabwera, nansongole adzasiyanitsidwa kuchokera ku zokololazo.

**Nkhoka yoponyedwa mnyanja:** Mateyu 13:47-50.

Yesu anafanizira kukula kwa Ufumu wa Mulungu ndi nkhoa yaikulu imene iponyedwa mnyanja. Nsomba zamitundu yonse zimalowamo, koma pamene nkhoa iponyedwa kumtunda nsombazo zimasiyanitsidwa ndi zinthu zina zimene sizabwino.

Ufumu udzakoka anthu a mitundu yonse. Ambiri adzalowamo. Ena adzakhala oona mtima ena ayi. Pa tsiku lomaliza la chiweruzo pamene Mulungu adzakoka nkhoka, “nsomba” zabwino ndi zoipa zizasiyanitsidwa. Inu simunaitanidwe kusiyantsa koma kusodza.

**Mbewu ya Mpiru:** Mateyu 13:31-32; Marko 4:31-32; Luka 13:19

Ufumu wa Mulungu udzacheluka ngati mbewu ya mpiru. Mbewu ya mpiri ndi yaing’ono, koma imakula mkukhala yokhwima. Ufumu wa Mulungu padziko umakhala ndi chiyamba chaching’ono. Pamene Yesu anabwerera kumwamba atatha utumiki padziko, anasiya gulu la anthu lochepa kulalikira uthenga wabwino. Okhulupirira ochepawa anachulukana kufikira zikwi la omutsatira Iye ku mitundu yonse ya anthu.

**Chotupitsa Mkate:** Mateyu 13:33; Luka 13:21

Monga chotupitsa mkate mu choikiramo, Ufumu wa Mulungu udzachelukitsidwa kufikira dziko lonse. Momwemonso chotupitsa, mphamvu ya Ufumu wa Mulungu siili kunja koma ili mkati.

**Mpesa ndi Nthambi zake:** Yohane 15:1-16

Fanizoli limafotokoza ubale wa pakati pa Yesu ndi kubala zipatso. Yesu ndi mpesa wa uzimu ndipo ife ndizo nthambi. Simungabale chipatso mwa inu nokha. Mungathe kuchulukana ngati mukhala mwa olumikizika ku moyo wa wochokera ku nthambi, ndiye Yesu. Yesu akufuna kusanza moyo wanu pochotsa chilichonse chimene sichibala chipatso ndi cholinga chakuti inu mukabale chipatso cha uzimu chokhalitsa.

**Zokolola:** Mateyu 9:37-38; Luka 10:2

Mu fanizo ili, munda ukuimira dziko. Zokolola ndi khamu la anthu amene akonzeka kulandira uthenga wabwino. Zokolola zochuluka zikudikira kuti zikoledwe ndi ogwira ntchito a Mulungu.

## **MFUNDO ZINA ZA KUCHULUKITSA**

Yesu anaphunzitsa mfundo zina zochulukitsa mwachidule:

**Kuunika kwa Dziko:** Mateyu 5:14-16; Luka 8:16

Ufumu wa Mulungu udzacheluka ngati wokhulupirira akuoneka ngati kuwala kochokera ku mzinda umene uli pamwamba kuonekera kutali. Tikyenera kubweretsa kuunika kwa dziko (Yesu) ku dziko limene lili mu mdima wa uzimu. Ufumu udzacheluka pamene anthu abwera ku kuwala.

**Mchere wa dziko:** Luka 14:34

Mu nthawi ya Mbaibulo, mchere umathiridwa pa nyama kuti isaonongeke. Okhulupirira ali ngati “mchere” wothiridwa pa dziko ndi uthenga wa kuteteza (chipulumutso). Ufumu udzachuluka anthu apulumuke ku “chivundi” (imfa ya uzimu) ya tchimo.

**Chuma cha kumwamba:** Mateyu 6:19-21; Luka 12:15

Okhulupirira sakuyenera kukhala ndi chidwi ndi kudzychulukitsira chuma cha dziko lapansi. Tayitanikwa ku chichulukitso cha uzimu. Pamene mukugawana uthenga wabwino, mumachulukitsa chuma cha chanu cha uzimu kumwamba.

**Chipata chotakata:** Mateyu 7:13

Simungapereke chiweruzo choyenera poyang’ana chiwerengero. Njira yak u Gehena ili yotakata ndipo ambiri amapita kumeneko koma njira yaku moyo wosatha amapitako ndi ochepa.

**Ntchito Zambiri:** Mateyu 7:22

Ambiri adzachita ntchito zodabwitsa. Moti padzakhala kukula ndi kuchuluka. Komatu kuchita zodabwitsa zambiri sikofanana ndi kuchita chifuniro ndi kukwaniritsa cholinga cha Mulungu. Zodabwitsa za Mulungu zikuyenera kuchitidwa ndi anthu Ake mu njira Yake.

**Zochepa ndi Zambiri:** Mateyu 10:42; Mateyu 14:15-21

Chilichonse chochitika mu dzina la Yesu, ngakhale choneka chochepa, ndi chofunikira. Chozizwa cha mikate ndi nsomba chimaonetsera mmene Mulungu amachulukitsira ndi kugwiritsa ntchito zochepe zimene tingapereke.

**Kukula kumafuna Kusintha:** Marko 2:21-22; 7:13

Kukula kwatsopano kumafuna kusintha. Simungasunge chatsopano mu chotengera cha makhalidwe a zakale ndi a uchimo. Kuthekera kwa mphamvu ya Mau a Mulungu kumalepheretsedwa ndi anthu amene amakakamira makhalidwe akale ndi kukana kusintha.

**Kupeza pa Kutaya:** Marko 8:34-37; 10:29-30

**Kulandira pa Kupereka:** Luka 6:38

Mfundo za dziko lapansi zimaphunzitsa kuti mumapeza pofuna zambiri. Yesu anaphunzitsa kuti mumapeza chilichonse pamene mutaya chilichonse. Chimene chimaoneka chotayika mu dziko mumachipeza mu dziko la uzimu.

**Imfa imabweretsa Moyo:** Yohane 12:24

Kudzera mu imfa ya Yesu, ambiri analandira moyo. Pofuna kuchulukitsa, mbewu iyenera kufa. Kudzera mu imfa moyo unabwera. Kuti mukhale ophunzira weniweni mukuyenera kufa ku zokhumba za thupi. Mukuyenera “kufa” ku uchimo. Mukuyenera kukaniza njira zanu potsata Yesu.

**Mpingo wa pa thanthwe:** Mateyu 16:18

Ufumu wa Mulungu unakhazikika pa thanthwe Yesu Khristu. Palibe kukula popanda Iye. Yesu anati, “Ndizamanga mpingo wanga.” Ndipo anati palibe munthu amene abwera kwa Ite ngati Atate samuitana (Yohane 6:44).

Chitsutso chimayenera kukhalako, koma “makomo a imfa” sangakhoze kugonjetsa cholinga cha Mulungu pofuna kukulitsa Ufumu wake.

**...Ici sicitheka ndi anthu, koma zinthu zonse zitheka ndi Mulungu (Mateyu 19:26).**

**...Zinthu zonse zitheka ndi iye wakukhulupirira (Marko 9:23).**

## **MFUNDO YAIKULU YA KUCHULUKITSA**

Mfundo yaikulu ya kuchulukitsa imene Yesu anaphunzitsa inaperekedwa Mmau Ake otsiriza kwa ophunzira ake. Lamulo lake linaulula cholinga chake chachikulu polalikira uthenga wabwino ndi kuchulukitsa atsopano ndi ophunzira:

**Cifukwa cace mukani, phunzitsani anthu a mitundu yonse, ndi kuwabatiza iwo m'dzina la Atate, ndi la Mwana, ndi la Mzimu Woyera:**

**ndi kuwaphunzitsa, asunge zinthu zonse zimene ndinakulamulirani inu; ndipo onani, Ine ndiri pamodzi ndi inu masiku onse, kufikira cimariziro ca nthawi ya panso pano (Mateyu 28:19-20).**

**Ndipo ananena nao, mukani ku dziko lonse lapansi, lalikirani Uthenga Wabwino kwa olengedwa onse (Marko 16:15).**

**Ndipo anati kwa iwo, Kotero kwalembedwa, kuti Kristu amve zowawa, nauke kwa akufa tsiku lacityatu;**

**Ndi kuti kulalikiidwe m'dzina lace kulapa ndi kukhululukidwa kwa macimo kwa mitundu yonse, kuyambira ku Yerusalemu.**

**Inu ndinu mboni za izi (Luka 24:46-48).**

**Komatu mudzalandira mphamvu, Mzimu Woyera atadza pa inu: ndipo mudzakhala mboni zanga m'Yerusalemu, ndi m'Yudeya lonse, ndi m'Samariya, ndi kufikira malekezere ace a dziko (Machitidwe 1:8).**

### **CHIDULE**

Ziphunzitsa za Yesu zimaonetsera kuti Iye sakondwera ndi:

- Kusodza opanga kugwira.
- Phwando lopanda kanthu.
- Kufesa opanda kulolola.
- Mtengo wosabala zipatso.
- Nkhosa yotaika imene sibwerera mnkhola.
- Ndalama yotaika imene sinapezeke.
- Mwana wolowelera amene sanapezeke.
- Kapolo wosabala zipatso.
- Nthaka ya uzimu yosachita bwino.
- Zokolola zakupsa zimene sizinakololedwe

Atate athu amene safuna kuti ngakhale mmodzi atayike, amakondwera ndi zotsatira kudzera mu kuchulukana kwa uzimu:

**Comweco siciri cifuniro ca Atate wanu wa Kumwamba kuti mmodzi wa ang'ono awa atayike (Mateyu 18:14).**

**Ambuye sazengereza nalo lonjezano, monga ena aciyesa cizengerezo; komatu aleza mtima kwa inu, wosafuna kuti ena aonongeke, koma kuti onse afike kukulapa (II Petro 3:9).**

## MAYESO ODZIYETSA NOKHA

1. Lembani Vesi Lotsogolera kuchokera pantima.

---

---

---

2. Perekani tanthauzo la mawu oti “fanizo.”

---

---

3. Kodi ndi chifukwa chiyani Yesu amaphunzitsa ophunzira ake mu mafanizo?

---

---

4. Pa pepala lapadera, longosolani mwachidule mfundo za kuchulukana mu fanizo lililonse pansipa:

Phwando la pa gome lopanda kanthu:

Mtengo wamkuyu wosabala:

Nkhosa yosochera, ndalama ndi mwana:

Mafanizo a kapolo:

Wofesa:

Nansongole ndi Tirigu:

Nkhoka:

Mbewu ya mpiru:

Chotupisa mkate:

Mpesa ndi nthambi zake:

(Mayankho a mafunsowa akupezeka kumapeto kwenikweni kwa bukuli).



## KUPITILIZA KUPHUNZIRA

1. Kuyambira zaka 12 kufikira pamene Yesu amayamba utumiki, Baibulo silimapereka tsatanetsatane wa zimene zinachitika mmoyo wake mu nthawi imeneyi. Ndi vesi limodzi lokha limene limaulula za kukula kwa ku uzimu mu nthawi imeneyi.

**Ndipo mwanayo anakula nalimbika, nalikudzala ndi nzeru; ndi cisomo ca Mulungu cinali pa iye (Luka 2:40).**

Kuti ukhale wamphamvu, kukula kwa ku uzimu kukuyenera kubwera poyamba utumiki usanayambe.

2. Pamene nthawi imayandikira kumapeto, Satana adzagwiritsa ntchito mfundo zake zochulukitsa. Werengani mavesiwa:

-Aneneri onyenga adzauka: Mateyu 24:11

-Anthu ambiri adzanyengedwa: Mateyu 24:11

-Uchimo udzachuluka: Mateyu 24:12

-Ambiri adzataya choonadi cha uthenga wabwino: II Atesalonika 2:3

-Mazunzo a okhulupirira adzachuluka: Mateyu 24:9-10

-Chodetsa ndi nkhani zopanda pake zidzachuluka: II Timoteo 2:16

## CHAPUTALA CHA 4

### CHIMODZI KUPHATIKIZA CHIMODZI ZIMAKHALA ZOPITILIRA ZIWIRI

#### ZOLINGA:

Pakutha pa chaputalachi muyenera:

- Kulemba Vesi Lotsogolera kuchokera pantima.
- Kupereka tanthauzo la mawu oti “umboni.”
- Kupereka tanthauzo la mawu oti “otumikira.”
- Kupereka tanthauzo la mawu oti “mkulu wampingo”
- Kulongosola tanthauzo la mawu oti “maitanidwe” a otumikira.
- Kuolongosola dongosolo la Mulungu lochulukitsa pofalitsa uthenga wabwino.
- Kutchula anthu awiri a Mchipangano Chatsopano ngati chitsanzo cha kuchulukitsa.
- Kulongosola mmene mungachulukire ku uzimu.
- Kuyamba kuchulukana ku uzimu.

#### VESI LOTSOGOLERA:

**Ndipo zimene wazimva kwa ine mwa mboni zambiri, zomwezi uikize kwa anthu okhulupirika, amene adzadziwa kuphunzitsa enanso (II Timoteo 2:2).**

#### MAWU OYAMBA

Kukula kwa munthu kumayamba ndi selo imodzi ya moyo. Ndipo seloyo imayamba kuchulukana kwambiri kufikira kuti munthu amapezeka kuti wapangidwa. Atatha kubadwa, ntchitoyo imapitilira mwa mwana. Maselo a munthu amapitilira kuchulukana ndi kuyamba kukula. Izi zili chomwechonso ndi ndi kudziko la uzimu. Munthu aliyense amene wakumana ndi moyo watsopano mwa Yesu ali chomwechonso ndi selo ya munthu. Wokhulupirira aliyense ayenera kubereka ku uzimu. Uthenga wabwino umalalikidwa pamene okhulupirira amachulukana mu njira imeneyi.

Chaputala ichi chikuulula za udindo wanu ngati munthu ku moyo wanu wa uzimu. Muphunzira dongosolo la Mulungu kuchulukana ku uzimu limene ndi “1 kuphatikiza 1 zimakhala zoposa ziwiri.

## ZOLEPHERETSA

Vuto limene Yesu anali nawo kwa okhulupirira linali kufikira dziko lonse lapansi ndi uthenga wabwino (Mateyu 28:19; Machitidwe 1:8). Lero tikukhala mu dziko limene likukula. Zikwi za anthu akubadwa tsiku ndi tsiku. Chiwerengero cha dziko chikukula kwambiri.

Pali anthu ambiri amene sanafikilidwe ndi uthenga wabwino mdzikoli ndipo ambiri sanamvepo za Yesu. Magulu a anthu amenewa ndi ankhaninkhani amene sanafikilidwe ndi uthenga wabwino. Midzi komanso komanso madera ambiri alibe mipingo. Maiko ambiri kulibe azibusa ambiri ophunzitsidwa ku mipingo imene ilipo.

Kodi tingapambane bwanji ndi vutoli pamene Yesu akuti tifikire dziko lonse ndi uthenga wabwino?

## DONGOSOLO LA MULUNGU

Mulungu ali ndi dongosolo lapaderadera lofuna kufikira dziko lapansi ndi uthenga wabwino. Mwachidule, Yesu anawauza ophunzira ake kuti...

**Komatu mudzalandira mphamvu, Mzimu Woyera atadza pa inu: ndipo mudzakhala mboni zanga m'Yerusalemu, ndi m'Yudeya lonse, ndi m'Samariya, ndi kufikira malekezero ace a dziko (Machitidwe 1:8).**

Dongosolo la Mulungu ndi ili: Mzimu Woyera ndi mphamvu ya umulungu yopezeka kuseli kwa kuchulukana, Yesu ndiye mwini nkhanu wa uthenga, ndipo dziko lonse lidzakhala lolandira uthenga wabwino.

Ophunzira ndi mnthumwi za kuchulukana. Njira za Mulungu kwa ophunzira ndi kuchitira “umboni” wa uthenga wabwino. Choncho kuchitira “umboni” ndiko kunena zimene waona, wamva, kapena kukumana nazo. Mu bwalo la milandu, mboni ndiye amene amavomereza za chinthu kapena munthu. Monga mboni, mukuyenera kuchitira umboni za Yesu ndi cholinga chake cha chipulumutso kwa anthu onse. Pali mitundu iwiri ya maumboni opezeka mbwalo la milandu la malamulo. Umboni woyamba ndi wolankhula zokhuza nkhanu. Umboni wina ndi otsimikizira.

Mzimu Woyera amakuthandizani kuchitira umboni kaya wolankhula kudzera mu kuonetsera mphamvu ya Mulungu.

## KUGAWANA PAKATI PA AKULU A MPINGO NDI ATUMIKI

Dongosolo la Mulungu kwa okhulupirira aliyense ndi lochitira umboni wa uthenga wabwino. Mpingo woyamba unakula pamene amatsatira dongosololi. Wokhulupirira aliyense amagawana uthenga wabwino ndipo anali wochitachita ku uzimu. Makomo awo amakhala malo ochulukiranapo. Mpingo unakula ndi kuchulukana pamene okhulupirira amachitira umboni wa uthenga wabwino.

Pamene mpingo ukukula, Mulungu anaitana anthu ena kuti azitumikira nthawi yawo yonse monga abusa, alaliki, aneneri, aphunzitsi ndi atumwi. Kwa nthawi yaitali, okhulupirira anakhala gawo limodzi la magulu awiri mu mpingo. Amakhala akulu ampingo kapena atumiki wamba.

Atumikiwa amakhala gulu limodzi la anthu wosankhidwa ndi Mulungu. Tanthauzo lake ndi lakuti anthu onse a Mulungu. Choncho atumiki amenewa amadziwidwa ngati anhtu amene satumikira nthawi yawo yonse mu mpingo ayi.

Kenako pali akulu a mpingo amene anaphunzira bwino pa ntchito yawo ya utumiki mu mpingo. Awa kwa iwo utumiki umakhala ngati ntchito yawo ya nthawi yonse ku mpingo. Akhoza kusankhidwa kapena osasankhidwa ndi mpingo.

Kwa nthawi yaitali, mu mbiri ya mpingo, kusiyana pakati pa atumiki ndi atumiki wamba kunayamba. Moti atumiki wamva ansiya kukhala ochulukana mu mpingo. Anayamba kusiyira ntchito yofalitsa uthenga ku dziko kwa atumiki omwe anali ndi nthawi yonse yotumikira.

Palibe mtumiki wophunzira amene akhoza kukwaniritsa ntchito yonse yonse imene mpingo unatumidwa kuti ukachite. Ichi ndi chifukwa chimodzi chimene sitinafikire dziko lapansi ndi uthenga wabwino. Okhulupirira apereka udindo wawo kwa atumiki. Baibulo limaphunzitsa za kugawana kwa ntchito mu mpingo, koma munthu wina aliyense akuyenera kukangalika kufalisa uthenga wabwino. Onani Machitidwe 6:1-6.

Pamene mpingo wa ku Yerusalemu imachulukana, zinayamba kufunikira kuti agawane ntchito kuti afikire zosowa zonse za mu mpingo. Atsogoleri anadzipereka okha ku Mau a Mulungu ndi kupemphero. Atumiki wamba amagwira ntchito monga kutumikira amasiye ndi ntchito zina zotumukira. Koma ngakhale okhulupirira amatumikira mosiyanasiyana mu mpingo, onse anakangalika kufalisa uthenga wabwino.

Stefano anali mmodzi mwa atumiki wamba amene anasankhidwa kugwira ntchito ina, koma anachitira umboni wamphamvu wauthenga wabwino. (Machitidwe 6:8-11). Filipino anali mtumiki wambanso amene anasankhidwa kuti atumikire zinthu zina. Anagawana uthenga wabwino ndi a Samariya (Machitidwe 8:5-12).

Pamene chizunzo chinabwera ku Yerusalemu ndipo okhulupirira mkubalalikana mmizinda anapitilira kukhala mboni za uthenga wabwino.

**Pamenepo ndipo iwo akubalalitsidwa anapitapita nalalikira mauwo (Machitidwe 8:4).**

Kwa okhulupirira enieni sipakhala kugawana pakati pa opatulika ndi a kudziko chifukwa Yesu ndi Ambuye wa onse.

## MAITANIDWE A ATUMIKI WAMBA

Ngati mukufuna mumvetsetse maitanidwe a uzimu a mtumiki wamba, mubwerere ku Chipangano Chakale. Dongosolo la Mulungu linali kwa mtundu wonse wa Israyeli kuti ukhale “ansembe” kapena “atumiki.”

**Ndipo ndidzakuyesani ufumu wanga wa ansembe, ndi mtundu wopatulika (Eksodo 19:6)**

Monga ansembe, munthu aliyense wa Israyeli anali mboni wa Mulungu woona kwa osakhulupirira.

Kukhazikitsidwa kwa udindo wa unsembe sikunasinthe ndondomeko ya Mulungu pa Israyeli. Unsembe unali ngati ntchito ya “utumiki” wa utsogoleri wa masiku a lero. Koma mtundu wonse umatumikirabe ngati atumiki a uthenga wa Mulungu mitundu yosadziwa Mulungu.

Mu Chipangano Chatsopano, okhulupirira apatsidwa maitanidwe ofanana. Akutchedwa ansembe kapena atumiki a uthenga wabwino:

**Koma inu ndinu mbadwa yosankhika, ansembe acifumu, mtundu woyera mtima, anthu a mw ni wace, kotero kuti mukalakire zoposazo za iye amene anakuitanani muturuke mundima, mulowe kuunika kwace kodabwitsa (II Petro 2:9).**

Kuitanidwa kwa okhulupirira ndiko kuti akachitire umboni wa Mulungu amene anawatulutsa mu mdima wa uzimu ndi kulowa mu “kuwala” kwa Yesu Khristu (Yohane 9:5).

Okhulupirira amaudzidwa kuti “ayende moyenera molingana ndi maitanidwe awo amene alimo” (Aefeso 4:1). Pali maitanidwe amodzi ndiwo kuchitira umboni wa uthenga wabwino. Imeneyi ndi ntchito ya okhulupirira onse. Munthu wina aliyense adzayankhapo pa za mmene anachitira ku maitanidwe ake.

Maitanidwe amenewa samakhazikika chifukwa cha maphunziro kapena kuthekera kwa kudziko. Mulungu amagwiritsa ntchito anthu wamba ndi cholinga chakuti Iye yekhayo alandire ulemerero.

**Pakuti penyani maitanidwe anu, abale, kuti saitaniidwa ambiri anzeru, monga mwa thupi; ambiri amphamvu, mfulu zambiri, iai;**

**Koma Mulungu anasankhula zopusa za dziko lapansi, kuti akacititse manyazi anzeru; ndipo zofoka za dziko lapansi Mulungu anazisankhula, kuti akacititse manyazi zamphamvu;**

**Ndipo zopanda pace za dziko lapansi, ndi zonyozeka, anazisankhula Mulungu, ndi zinthu zoti kulibe; kuti akathere zinthu zoti ziriko; kuti thupi liri lonse lisadzitamande pamaso pa Mulungu (I Akorinto 1:2-29).**

## MACHITIDWE A KUCHULUKANA

Dongosolo la Mulungu la kuchulukana ndi lofanana ndi la kudziko la uzimu. Paulo anamuza Timoteo mawu awa mwachidule:

**Ndipo zimene wazimva kwa ine mwa mboni zambiri, zomwezi uikize kwa anthu okhulupirika, amene adzadziwa kuphunzitsa enanso (II Timoteo 2:2).**

Paulo anamuza Timoteo kuti asankhe anthu okhulupirika ndi kuwapereka ku zinthu zimene anaphunzitsidwa ndi Paulo. Anthu okhulupirika amenewa akuyenera kukhala ndi kuthekera kophunzitsa ena. Kupyolera mu dongosolo limeneli la kuchulukana, uthenga wabwino ungafikire ku dziko lapansi.

Pofuna kuona mmene dongosolo la Mulungu la kuchulukana mmene limagwirira ntchito, werengani tchati mmusimu. Tchatili likuonetsa nthawi ya pachaka imene munthu angatembenuze munthu wina ndi kumuphunzitsa kukhala mkhristu wodalilika. Mu zoonza zake zikhoza kutenga nthawi kapena ayi potengera munthu amene achitayo. Choncho sizotheka kukhazikika pa malire a nthawi. Koma ngati mkhristu akhoza kufikira munthu mmodzi ndi kumuphunzitsa pa chaka ndipo nayenso aphunzitsa wina pa chaka, dziko likhoza kufikilidwa ndi uthenga wabwino.

## TIYAMBE BWANJI

Chipangano chatsopano chimaulula uthenga wabwino unafalikira mmadera oyandikana. Kutanthauza kuti mukhoza kufalisa uthenga mosavuta pogwiritsa ntchito magulu a anzanu, achibale, ndi ogwira nawo ntchito limodzi.

Mwachitsanzo, Yesu anaitani nsodzi mmodzi wotchedwa Andreya. Iyeyi anagawana uthenga ndi mbale wake Petro. Ndipo anagawana ndi asodzi anzawo. Posakhalitsa gulu la anthu onse la asodzi linamtsata Yesu.

Mmoyo wathu wa tsiku ndi tsiku atumiki osaitanidwa sikuti angokhala okongoletsa mpingo kapena kumene amakhala ayi. Iwonso ndi akazembe a Ufumu kwa anzawo, achibale komanso ogwira nawo ntchito limodzi. Kaya ndi kusukulu, kuntchito, kubanja, mmudzi, tikhoza kuchitanso utumiki.

Luka 16:19-31 amakmba nkhani ya mwini chuma amene anapita ku Gehena. Munthuyi anafunitsitsa atabwerera kuti akalalkire kwa a pabanja pake koma nthawi inamuthera. Musadikire kufikira nthawi yofalisa uthenga ndi anzanu ikuthereni.

## **MPHATSO ZA MZIMU NDI KUCHULUKANA**

Umboni weniweni wa ubatizo wa Mzimu Woyera ndiko kukhala wamphamvu pochitira umboni wa uthenga wabwino. Mphamvu ya Mzimu Woyera imapangitsa akhristu kuchulukana ku uzimu (Machitidwe 1:8).

Njira imodzi imene Mzimu Woyera amapatsa mphamvu wokhulupirira ndi kudzera mu mphatso za uzimu. Okhulupirira aliyense anapatsidwa mphatso za uzimu zomukuonzekeretsa kuchita utumiki kwa ena. Mphatsozi ndi kuthekera kwa uzimu kopatsidwa ndi Mzimu Woyera.

Ngati simudziwa mphatso za uzimu zimene Mulungu wakupatsani, funsani a Harvestime International Institute akupatseni phunziro la “*Utumiki wa Mzimu Woyera.*” Phunziroli limakamba za mphatso za uzimu.

## **KUKULA KWA UFUMU**

Wokhulupirira aliyense akuyenera kukhala wochitachita. Koma kuchulukana chabe kwa okhulupirira sikukwanira. Wokhulupirira ayenera kudzipereka pa mpingo umene ali ndi cholinga chokhala pa umodzi woona ndi okhulupirira ena. Mpingi uyeneranso kuchulukana pawokha. Mpingo uyenera kumakula mwa okha ku uzimu ndi kupitilira kukula, mmalire, ndi makulidwe ena. Mwaonanso udindo wanu wochukitsa ngati munthu. Mu chaputala chikubwerachi, muphunzira za mmene mungachulukire ngati gulu pakati pa mpingo.

## MAYESO ODZIYESA NOKHA

1. Lembani Vesi Lotsogolera kuchokera pantima.

---

---

2. Perekani tanthauzo la mawu oti “mboni.”

---

3. Perekani tanthauzo la mawu oti “atumiki wamba.”

---

4. Perekani tanthauzo la mawu oti “atumiki oitanidwa.”

---

5. Fotokoza “maitanidwe” a atumiki wamba.”

---

6. Kodi dongosolo la Mulungu la kuchulukitsa pa kulalikita uthenga wabwino ndi chani?

---

7. Ndi anthu ati awiri mu Chipangano Chatsopano amene anali chitsanzo cha kuchulukana ku uzimu?

---

---

8. Ndi njira iti yabwino yoyamba kuchulukana ku uzimu?

---

(Mayankho a mafunsowa akupezeka kumapeto kwenkweni kwa bukuli).



## KUPITILIZA KUPHUNZIRA

1. Mu chaputala chimene chikuthachi ndi mwaphunzira za mafanizo a kuchulukana. Onaninso mafanizo otsatirawa kawiri. Mu fanizo lililonse aliyense anali ndi udindo wochulukana mokhulupirika.

-Matalente: Mateyu 25:14-30; Luka 19:11-27

-Munthu wa paulendo wautali: Marko 13:34-37

-Akapolo: Mateyu 24:43-52; Luka 12:39-46

-Akapolo woyang'anira: Luka 12:36-38

-Woyang'anira wokhulupirika: Mateyu 25:14-20

2. Werengani kukambirana kwa pakati pa Yesu ndi Petro mu buku la Yohane 21:15-22. Mu Machitidwe 10:22 werengani mawu a Yesu amene analankhula kwa Paulo pa nthawi imene amatembenuka mtima.

Chidwi chanu chisakhale poti kaya ena akukwaniritsa udindo wawo wolalikira uthenga kapena ayi. Simukuyenera kufunsa ngati Petro, “Kodi munthuyu adzatani?” Chidwi chanu chikhale ngati cha Paulo, “Kodi ndidzatani Ambuye?”

## CHAPUTALA CHA 5

### MAWU OYAMBA A KUKULA KWA MPINGO

#### ZOLINGA:

Pakutha pa chaputalachi muyenera:

- Kulemba Vesi Lotsogolera kuchokra pantima.
- Kudziwa mpingo weniweni.
- Kulongosola mmene mpingo unayambira.
- Kulemba zitsanzo za Mpingo mu Baibulo.
- Kudziwa cholinga cha Mpingo Mbaibulo.
- Kudziwa mitundu inayi ya kukula kwa Mpingo.
- Kulemba chidule cha utumiki wa Mzimu Woyera pa kukula kwa Mpingo.

#### VESI LOTSOGOLREA:

**Ndiponso Ine ndinena kwa iwe, kuti iwe ndiwe Petro, ndipo pa thanthwe ili ndidzakhazika Mpingo wanga; ndipo makomo a dziko la akufa sadzaulaka uwo (Mateyu 16:18).**

### MAWU OYAMBA

Mu chaputala chomaliza mwaphunzira za udindo wa wokhulupirira aliyense wochulukana ku uzimu pofalisa uthenga wabwino. Mulungu ali ndi dongosolo lapaderadera mwa okhulupirira amene angofika kwa Iye. Akuyenera kukhala gawo limodzi la chiyanjano cha okhulupirira anzawo mu Mpingo. Okhulupirira ayenera kuberekana aliyense mumpingo, pakutero mpingo umachulukana.

Chaputala ichi chikuonetsera dongosolo la Mulungu ku Mpingo ngati malo ochulukiranapo ku uzimu. Machaputala anayi otsatira akufotokoza za mitundu ya kukula kwa mpingo.

### MPINGO

Tikamakamba za “Mpingo” sitikamba za bungwe kapena mpingo opangidwa ndi anthu.

Mawu okuti “Mpingo” amatanthauza “oitaniidwa.” Tikamakamba za Mpingo, timakamba za chiyanjano cha dziko lapansi cha iwo amene ndi okhulupirira owona amene ayitanidwa kuchoka ku dziko lapansi kulowa mu Ufumu wa Mulungu.

Chifukwa cha cholinga cha utumiki, chiyanjano chimenechi cha dziko lapansi cha okhulupirira chagawidwa mmangulu awo amene amasonkhana. Maguluwa amenewa amatchedwa Mpingo. Ena mwa magulu amenewa amakhala oyima pawokha. Pamene ena amasonkhana ndi mabungwe monga Assemblies of God, Baptist ndi Methodist komanso ena.

Munthu sumakhala gawo la Mpingo woona pokhala limodzi ndi bungwe koma pokhala wobadwa mwatsopano ndi kulowa mu Ufumu wa Mulungu. Izi zimachitika zimachitka povomereza ndi kulapa machimo ndi kulandira Yesu ngati Ambuye ndi mpulumutsi wa moyo wanu. Mutatha kukhala wokhulupirira, dongosolo la Mulungu pa moyo wanu ndilo kukhala mmodzi wa anthu wokhulupirira mu chiyanjano chimene ndi Mpingo.

### **MMENE MPINGO UMayambira**

Mu Chipangano Chakale mtunda wa ana a Israyeli unasankhidwa ngati gulu la anthu limene kudzera mwa iwo Mulungu adzadzizululu yekha kwamitundi una ya anthu. Kwa nthawi yaitali Israyeli analephera udindowu.

Mu nthawi ya Chipangano Chatsopano pamene Yesu anabwera padziko lapansi, Israyeli anamkana ngati Mesiya. Chifukwa cha ichi, Mulungu anadzutsa gulu lina la anthu limene anasankha kudzionetsa ku dziko. Gulu limeneli likutchedwa Mpingo.

Kutchulidwa koyamba kwa “Mpingo” ndi pamene Yesu analongosola za mmene Mpingo ungamangidwire.

**Ndiponso Ine ndinena kwa iwe, kuti iwe ndiwe Petro, ndipo pa thanthwe ili ndidzakhazika Mpingo wanga; ndipo makomo a dziko la akufa sadzaulaka uwo (Mateyu 16:18).**

Mu ndime imeneyi Yesu anaulula kuti Petro adzakhala mmodzi wa miyala ya maziko a uzimu a Mpingo woyamba. Izi zikutanthauza kuti adzakhala ofunika mmakulidwe ndi maumbidwe ake. Tanthauzo la Petro ndiye kuti “thanthwe kapena mwala.”

Yesu ananena yekha kuti kwa Iye yekha, “...pa thanthwe ILI ndidzamanga Mpingo wanga.” Amaonetsera kuti Mpingo udzakhazikika pa Iye. Adzakhala thanthwe limene Mpingo udmangidwa. Padzakhala miyala ina yaing’ono (anthu ngati Petro). Koma zoonza zake, okhulupirira amatchedwa “miyala yamoyo” amene ali gawo limodzi la Mpingo:

**Inunso ngati miyala yamoyo mumangidwa nyumba ya uzimu, kun mukhale ansembe oyera mtima, akupereka nsembe zauzimu, zolandiridwa ndi Mulungu mwa Yesu Kristu (I Petro 2:5).**

Maziko a “miyala ya moyo” ndi “Thanthwe.” Thanthwelo ndiye Yesu ndipo limalongosola malire a Mpingo. Mpingo sukhalam pingo woona pokhapokha wamangidwa pa Yesu Khristu.

Kwa zaka zambiri Mpingo yambiri yosiyana papanga zolinga za mabungwe komanso mautumiki. Ngati ali akhazikikadi pa maziko a Yesu, ndiye kuti ali gawo limodzi la chiyanjano cha okhulupirira cha pa dziko lapansi:

**Thupi limodzi ndi Mzimu mmodzi, monganso anakuitanani m'ciyembekezo cimodzi ca maitanidwe anu;**

**Ambuye mmodzi, cikhulupiriro cimodzi, ubatizo umodzi.**

**Mulungu mmodzi ndi Atate wa onse amene ali pamwamba pa onse, ndi mwa onse, ndi m'kati mwa zonse (Aefeso 4:4-6).**

Yesu ananena kuti “makoma a imfa” sadzaulaka mpingo woona. Izi zikutanthauza kuti Mpingo udzakumana ndi chitsutso chachikulu cha Satana, koma sudzagonjetsedwa.

Buku la Machitidwe limakamba za chitutso choyamba cha mpingo (Machitidwe 8). Kuyambira mu mbiri kufikra pano, mpingo wakhala ukulandira chitsutso chachikulu, koma udzakhalabe ndipo udzapitilira kukhalapobe. Udzakwaniritsa zolinga za Mulungu.

### **MMENE MPINGO UMAKHALIRA**

Baibulo limagwiritsa zitsanzo zambiri polongosola mpingo. Zitsanzosi zimaululu zambiri zokhuza maziko ndi cholinga cha mpingo. Onani zitsanzo za Mbaibulo zotsatirazi zokhudza Mpingo:

Munthu watsopano: Aefeso 2:14-15

Thupi la Khristu: Aefeso 1:22-23; 5:30; I Akorinto 12:27

Kachisi kapena nyumba ya Mulungu: Aefeso 2:21-22; I Akorinto 3:9,16; I Timoteo 3:15; I Petro 2:5

Ansemble achifumu: I Petro 2:5,9; Chibvumbulutso 1:6; 5:10

Mkwati wa Khristu: II Akorinto 11:2; Mateyu 25:6; Aefeso 5:22-32

Okhala mnyumba ya Mulungu: Aefeso 2:19

Nkhosa za Mulungu: Yohane 10:1-29; I Petro 5:3-4; Ahebri 13:20; Machitidwe 20:28

Pali mpingo umodzi koma Mbaibulo ukudziwika ndi magawo ambiri. Ukutchedwa:

Mpingo wa Mulungu: Machitidwe 20:28; I Akorinto 1:2; 10:32; 11:22; 15:9; I Timoteo 3:5; I

Atesalonika 2:14

Mpingo wa Mulungu wamoyo: I Timoteo 3:15

Mpingo wa Khristu: Aroma 16:16

Mpingo wa obadwa oyamba: Ahebri 12:23

Mpingo wa oyera mtima: I Akorinto 14:33

Anthu a Mulungu: Ahebri 4:9; I Petro 2:9-10

### **CHOLINGA CHA MPINGO MOLINGANA NDI MALEMBA**

Pali zolinga zambiri za Mpingo molingana ndi mmene Baibulo limatiuzira:

#### **MALAMBIRO A MULUNGU:**

Cholinga chachikulu chimene muntu analengedwera ndicho kulambira Mulungu. Kulambira ndi cholinga chachikulu cha Mpingo. Onani mavesiwa:

I Petro 2:5,9; I Akorinto 14:26-27; Yohane 4:23-24; Aefeso 2:19-22.

#### **KUTUMIKIRA MU MPINGO:**

Mamembala a mu Mpingo akuyenera kutumikirana zosowa za wina ndi mzake:

-Zikhoza kukhala zosowa za kuthupi: Machitidwe 11:27-30; 6:1-6.

-Mamembala ayenera kugawana mwa ufulu zinthuzawo: Machitidwe 2:44; 4:32, 34,37.

-Mamembala ayeneranso kusamalirana pa zosowa za ku uzimu mu thupi la Khristu: Yohane 15:1-7; Aroma 15:1-15; I Akorinto 3:9; Agalatiya 6:1; Akolose 2:16-23; I Atesalonika 2:7-16.

#### **CHIYANJANO:**

-Chiyanjano cha Mpingo chakhazikika pa umodzi wa mwa Khristu: Aefeso 4:4-6

-Mpingo umakhala umodzi mwa Khristu: Aefeso 2:11-18. Membala aliyense ndi wofanana pamoso pa Ambuye: Aefeso 2:19-20.

-Mpingo ukuyenera kukhala gulu la chiyanjano mmawu, mpemphero, ndi mu ntchito: Machitidwe 2:41-47; 4:24,32-33; Aefeso 2:20-22; I Yohane.

-Chiyanjano chawo chikuyenera chikhale ndi cholinga chimodzi, maganizo amodzi, moyo umodzi ndi mtima umodzi: Machitidwe 1:14; 2:46; 4:24,32; 5:12; 15:25

Chiyanjano sikuyenera chikhale kwa mpingo umodzi wokha ayi, komanso pakati pa mipingo ina. Werengani mavesiwa amene akuonetsera ubale umenewu pakati pa mipingo:

-Amadziwa kuti ali amodzi mwa Khristu ndipo alumikizidwa pamodzi: Machitidwe 15:1; Aroma 15:26-27

-Amalankhulana pafupipafupi ndi wina: Aroma 16:16; I Akorinto 16:19-20; Afilipi 4:23

-Amathandizana wina ndi mzake: Aroma 15:26; I Akorinto 16:1-3.

-Anathandizira ntchito ya atumwi mmadera ena: Afilipi 4:15-16

-Anagawana makalata a atumwi: Akolose 4:16.

-Amatumizirana nthumwi wina ndi mzake: Machitidwe 11:22,23,27; 15:1,2; I Akorinto 16:3,4

-Amalimbikizana wina ndi mzake pa chikhulupiriro: II Akorinto 1:24; 9:2; I Atesalonika 1:7-10; 2:14

-Amalumikizana pa nkhani ya ulaliki: I Atesalonika 1:8

## **UTUMWI:**

Mpingo cholinga chake ndiko kuchita utumwi osangoti kulambira komanso chiyanjano. Cholinga cha ana a Israyeli mu Chipangano Chakale ndi Mpingo mu Chipangano Chatsopano kunali kuulula Mulungu ku dziko lapansi.

Mu Chipangano Chakale, Israyeli anayenera kukhala mboni ku maiko osadziwa Mulungu. Chimene Mulungu amafuna chinali choti maikowa afike poona Mulungu ndi mphamvu yake kwa Israyeli. Mu Chipangano Chatsopano, cholingancha Mulungu chinali china. Chollinga chake chinali kuti mpingo upite ku maiko ngati mboni. Utumwi weniweni wa mpingo ukupezeka mu Aefeso:

**Kuti mu Eklesia azindikiritse tsopano kwa akulu ndi maulamuliro m'zakumwamba nzeru ya mitundu mitundu ya Mulungu,**

**monga mwa citsimikizo mtima ca nthawi za nthawi, cimene anacita mwa Kristu Yesu Ambuye wathu (Aefeso 3:10-11).**

**Anatizindikiritse ife cinsinsi ca cifuniro cace, monga kunamkomera ndi monga anatsimikiza mtima kale mwa iye,**

**kuti tikakonzedwe a makwaniridwe a nyengozo, akasonkhanitse pamodzi zonse mwa Kristu, za kumwamba, ndi za padziko (Aefeso 1:9-10).**

Chidule cha utumwi wa mpingo ndi ichi:

1. Mpingo ukuyenera kuonetsera Yesu ku dziko lapansi ngati Ambuye ndi Mpulumutsi. Mpingo ukuyenera kutsogolera anthu ku ubale wabwino ndi Yesu kuti athe kukhululukidwa machimo awo ndi kuyambanso moyo watsopano.
2. Kupyolera mu chiphunzitso ndi ulaliki wa ubatizo wa mmadzi, mpingo ukuyenera kukhazikitsa okhulupirra mu chiphunzitso, mfundo ndi makhalidwe a chikhristu. Akuyenera kuphunzitsa anthu ongotembenuka kumene kuti “asunge zinthu zonse” zimene analamulilidwa mmawu a Mulungu.
3. Mpingo ukuyenera kupanga dongosolo la okhulupirra atsopano kukhala ofunikira mu chijanano cha mpingo.
4. Mipingo yokhazikikayi ikuyenera kubwereza ndondomekoyi kuti akhale ndi okhulupirira ambiri ndi chijanano chochuluka.

Phunzirani zambiri zokhuza utumwi wa mpingo mmavesi awa:

Kufalisa uthenga wabwino kudziko lapansi: Mateyu 5:13-14; 28:18-20; Marko 16:15-16; Luka 24:45-49; Yohane 20:19-23; Machitidwe 1:8.

Kukhala mchere ndi kuunika kwa dziko lapansi: Mateyu 5:13-16; Afilipi 2:14-16; I Yohane 4:1.

Kuphunzitsa okhulupirita atsopano: Mateyu 28:19-20; Machitidwe 20:27-28; Aefeso 4:11-16; I Petro 5:1-3.

## MITUNDU YA KUKULA KWA MPINGO

Ngati mpingo ukukwaniritsa cholinga chake cha mmalemba, mitundu inayi yampingo imapezeka:

### **KUKULA KWA MKATI:**

Kukula kwa mkati ndi kukula kwa uzimu kwa anthu a mumpingo.

### **KUKULA KOCHULUKA:**

Uku ndi kukula kwa mpingo mu chiwerengero kumene kumachitika pamene ntchito yolalikira uthenga yachitika ndi mpingo. Okhulupirira achilendo amapezeka mkukhala gawo limodzi la thupi la Khristu.

### **KUKULA MMADERA:**

Mpingo umakula mmadera pamene wayambitsa mpingo wina mudera lina la anthu achikhaidwe chofanana.

### **KUKULA KOLUMIKIZANA:**

Uku ndi kukula kwa mpingo pamene wayamba kugawana uthenga kupitilira malire ndi anthu a dera lina osiyana mtundu, chikhalidwe.

## MZIMU WOYERA NDI KUKULA KWA MPINGO

Mzimu Woyera ndi mphamvu ya uzimu imene imapangitsa kukula kwa konse kwa mpingo kwa mitundu inayi:

**Komatu mudzalandira mphamvu, Mzimu Woyera atadza pa inu: ndipo mudzakhala mboni zanga m'Yerusalemu, ndi m'Yudeya lonse, ndi m'Samariya, ndi kufikira malekezere ace a dziko. (Machitidwe 1:8).**

Vesi limeneli limatiuza za mmene Mzimu Woyera amapangira:

**Kukula kwa mkati:** ophunzira alandira mphamvu ya Mzimu Woyera. Izi ziwapangisa iwo kuti akachitire umboni mwamphamvu.

**Kukula kochulukuka:** Mpingo udzachulukuka ku Yerusalemu.



**Kukula mmadera: mpingo udzadzala mipingo ina kumadera a zikhalidwe zofanana.**

**Kukula kolumikizana:** Mpingo udzalumikizitsa kusiyana kwa zikhalidwe pofuna kufikira ena monga Samariya ndi “malekezere a dziko lapansi.”

Baibulo limaphunzitsa kuti Mzimu Woyera ali ndi mautumiki ambiri. Anali wochitachita pa kulengedwa kwa dziko, amauzira mawu Mulungu. Analinso wochitachita mu nthawi ya utumiki wa Yesu panso pano, ndipo anagwira ntchito zambiri mmaalo mwa okhulupirira.

Mzimu Woyera amaulula choonadi cha uthenga wabwino ndi kuwokokera anthu kwa Mulungu kuti apulumuke. Mzimu Woyera alinso ndi utumiki wokhudza Satana. Amaberetsa mphamvy ya uzimu imene imaika malire pa mphamvu ya Satana (Yesaya 49:19). Mautumiki ake onse akupezeka mu maphunziro a Harvestime International Institute otchedwa “*Utumiki wa Mzimu Woyera.*”

Mzimu Woyera alinso ndi utumiki wapaderadera wokhudza kukula ndi kuumba mpingo:

#### **MZIMU WOYERA ANAUMBA MPINGO:**

**Pa tsiku la pentekosite pa Machitidwe 2:1-4 Mzimu Woyera anapanga Mpingo. Baibulo limaphunzitsa kuti Mpingo malo opezeka Mulungu omangidwa ndi Mzimu Woyera.**

**Pamenepo ndipo simulinso alendo ndi ogonera, komatu muli a mudzi womwewo wa oyer mtima ndi a banja la Mulungu**

**omangika pa maziko a atumwi ndi aneneri, pali Kristu Yesu mwini, mwala wa pangondya;**

**mwa iye cimango conse, columikizika pamodzi bwino, cikula, cikhale kacisi wopatulika mwa Ambuye;**

**cimene inunso mumangidwamo pamodzi, mukhale cokhalamo Mulungu mwa Mzimu  
(Aefeso 2:19).**

#### **MZIMU AMAKHUDZA MALAMBIRO**

**Kulambira kwa Mpingo kukuyenera kukhudzidwa ndi Mzimu Woyera:**

**Koma ikudza nthawi, ndipo tsopano iripo, imene olambira oona adzalambira Atate mumzimu ndi m'coonadi; pakuti Atate afuna otere akhale olambira ace.**

**Mulungu ndiye mzimu; ndipo omlambira iye ayenera kumlambira mumzimu ndi m'coonadi (Yohane 4:23-24).**

**Pakuti ife ndife mdulidwe, akutumikira popembedza ndi Mzimu wa Mulungu, nadzitamandira mwa Yesu Kristu, osakhulupirira m'thupi (Afilipi 3:3).**

#### **MZIMU WOYERA ANATSOGOLERA NTCHITO YA UTUMWI:**

**Izi zikuoneka mu ntchito ya utumwi ya mpingo woyamba:**

**Ndipo Mzimu anati kwa Filipino, Yandikira, nudziphatike ku gareta uyu (Machitidwe 8:29).**

**Ndipo anapita pa dziko la Frugiya ndi Galatiya, atawaletsa Mzimu Woyera kuti asalalikire mau m'Asiya; pamene anafika kundunji kwa Musiya,**

**Anayesa kunka ku Bituniya; ndipo Mzimu wa Yesu sanawaleza**

**Pamene anaona masomphenyawo, pomwepo tinayesa kuturukirakunka ku Makedoniya, poganizira kuti Mulungu anaitanira ife kulalikira Uthenga Wabwino kwa iwo (Machitidwe 16:6,7,10).**

**Ndipo pa kutumikira Ambuye iwowa, ndi kusala cakudya, Mzimu Woyera anati, Mundipatulire Ine Bamaba ndi Saulo ku nchito imene odinawaitanirako**

**Pamenepo iwo, otumidwa ndi Mzimu Woyera, anatsikira ku Selukeya; ndipo pocokerapo anapita m'ngalawa ku Kupro (Machitidwe 13:2,4).**

#### **MZIMU WOYERA ANASANKHA ATUMIKI:**

**Mipingo ina imasankha atumiki otumikira mu mpingo. Anthu ambiri amapita ku sukulu za koleji kapena ku seminale kukaphunzitsidwa ngati atumiki. Koma choyenera chimene malemba amanena ndi chakuti atumiki ayenera kuitanidwa ndi kusankhidwa ndi Mzimu Woyera:**

**Tadzicenjerani nokha, ndi gulu lonse, pamenepo Mzimu Woyera anakuikani oyang'anira, kuti muwete Eklesia wa Mulungu, umene anaugula ndi mwazi wa iye yekha (Machitidwe 20:28).**

#### **MZIMU AMADZODZA ALALIKI:**

**Paulo analemba kale: Ndipo mau anga ndi kulalikira kwanga sanakhala ndi mau okopa a nzeru, koma m'cionetso ca Mzimu ndi ca mphamvu (I Akorinto 2:4).**

#### **MZIMU WOYERA AMATSOGOLERA ZIGANIZO:**

**Machitidwe chaputala cha 15 amakamba za mkumano wa atsogoleri umene amakambirana mavuto osiyanasiyana amene mpingo umakumana nawo. Chiganizo chawo chomaliza amatsogolera ndi Mzimu Woyera:**

**Pakuti cinakomer a Mzimu Woyera ndi ife, kuti tisasenzetse inu cothodwetsa cacikuru cina coposa izi zoyenerazi (Machitidwe 15:28).**

#### **MZIMU AMABATIZA MPINGO NDI MPHAMVU:**

**Buku la Machitidwe limayamba ndi nkhani yaikulu kwambiri:**

Ubatizo umenewu unali wamphamvu pa kukula kwa mpingo mkati, chiwerengero, mmadera, mmalire kumene kukupezeka mbuku la Machitidwe.

**Ndipo pakufika tsiku la Pentekoste, anali onse pamodzi pa malo amodzi.**

**Ndipo mwadzidzidzi anamveka mau ocokera Kumwamba ngati mkokomo wa mphepo yolimba, nadzaza nyumba yonse imene analikukhalamo.**

**Ndipo anaonekera kwa iwo malilime ogawanikana, onga amoto; ndipo unakhala pa iwo onse wayekha wayekha.**

**Ndipo anadzazidwa onse ndi Mzimu Woyera, nayamba kulankhula ndi malilime ena, monga Mzimu anawalankhulitsa (Machitidwe 2:1-4).**

## MAYESO ODZIYETSA NOKHA

1. Lembani Vesi Lotsogolera kuchokera pantima.

---

---

2. Kodi Mpingo woona ndi wandani?

---

---

3. Kodi Mpingo unayamba bwanji?

---

---

4. Pali zitsanzo zambiri za Mbaibulo zimene zimakamba za Mpingo. Lembani zitsanzo zitatu zokha.

---

---

5. Tchulani zolinga zinayi za Mpingo zimene mwaphunzira mu phunziroli.

---

---

---

6. Tchulani ndipo longosolani mwachidule mitundu inayi ya Mpingo.

---

---

---

7. Chaputalach chakambapo za zolinga 7 za Mzimu Woyera mogwirizana ndi kukula ndi mapangidwe a Mpingo. Kodi mungatchule zingati?

---

---

---

---

(Mayankho a mafunsowa akupezeka kumapeto kwenikweni kwa bukuli)

## KUPITILIZA KUPHUNZIRA

1. Izi ndi zina mwa zotitsogolera zimene tingaziwire Mpingo wona. Ndi Mpingo umene:
  - umakhala wolondola mchiphunzitso. Ziphunzitso zonse zimakhazikika mu Mau olembedwa ndi Mulungu.
  - umakhala ndi mamembala obadwa mwatsopano: miyoyo ya mamembalayo imakhala yosinthika ndi mphamvu ya Mulungu.
  - wolambira: umalambira Mulungu mmodzi woonayo Atate, Mwana ndi Mzimu Woyera.
  - olalikira. Umakhala wochitachita mu utumwi ofikira dziko lapansi ndi uthenga wabwino.
2. Izi ndi zina zotitsogolera kudziwa Mpingo wonama. Ndi Mpingo umene:
  - umakhala wonama mchiphunzitso chake: Amasindika mawu ochepa okha ochokera Mbaibulo ndi kuchotsako ena. Samatenga Mau a Mulungu mmene alili. Amavomereza ziphunzitso za munthu zimene zimatsutsana ndi Mau a Mulungu.
  - ogawikana: amakhala ndi magawano a mu Mpingo ndipo amalakalaka kuyambitsa kuyambitsa mipatuko mu thupi la Khristu. Onani Aroma 16:17-18; Acts 20:29,30; Aefeso 4.
  - ulamuliro: mpingo wonama umayesera kulamulira miyoyo ndi ntchito za mamembala mu njira yowalamulira.
  - umakhala ndi mamembala osabadwanso: anthu amapitilira kukhala mmakhalidwe akale a uchimo.

## CHAPUTALA CHA 6

### KUKULA KWA MKATI

#### ZOLINGA:

Pakutha pa chaputalachi muyenera:

- Kulemba Vesi Lotsogolera kuchokera pantima.
- Kulongosola za kukula kwa “mkati” kwa Mpingo.
- Kupereka tanthauzo la “kukula mu uzimu.”
- Kuzindikira zizindikiro za kukula mu uzimu.
- Kulongosola utumiki wa Mzimu Woyera mogwirizana ndi kukula kwa Mpingo.
- Kuzindikira nyengo za kakulidwe mu dziko lapansi molingana ndi kudziko la ku uzimu.

#### VESI LOTSOGOLERA:

**Pakuti kunamkomera Atate kuti mwa iye cidzalo conse cikhaliye (Akolose 1:19).**

### MAWU OYAMBA

Mu chaputala chomaliza munaphunzira kuti pali mitundi inayi ya kukula kwa dongosolo la Mulungu pa kuchuluka kwa Mpingo. Mpingo ukuyenera kuchulukana mkati, muchiwerengero, mmadera komanso mmalire. Phunziro ili tikhala tikukamba za kukula mkati kwa Mpingo.

### KUKULA KWA MKATI

Tikamakamba za “kukula mkati” kwa Mpingo, timakamba za kukula ndi kuumbika kwa mamembala. Mpingo umakula mu uzimu molingana ndi kukula kwa munthu kwa yekha.

Mpingo sukungoyenera kukula kokha mu chiwerengero kudzera ku mmadera, kuchuluka kwa anthu kapena mmalire, ukuyeneranso kukula mmachitidwe. Kukula mmachitidwe ndiye kuti ndi kukula mkati ndi kukula ku uzimu. Paulo anakamba za izi pofanizira za kukula mkati mu thupi:

**Pakuti kunamkomera Atate kuti mwa iye cidzalo conse cikhaliye (Akolose 1:19).**

Ndiye kuti “kuchuluka kwa Mulungu” ndiye kuti ndi kukula kwa kuuzimu. Pamene mamembala akukula mu uzimu, mpingo umakumanandi kukula kwa mkati. Moti thupi lonse la Khristu limakula ndi kuchuluka kwa chidziwitso cha Mulungu.

Kukula kwa ku uzimu ndi kuchuluka kwa kukhwima ku uzimu kumene kumatsatira ku kuumba moyo wa mkhristu wa okhulupirira. Ndi kukula kwa chidziwitso cha Yesu:

**Koma kulani n'cisomo ndi cizindikiritso ca Ambure wathu ndi Mpulumutsi Yesu Khristu (II Petro 3:18)**

Uku ndi kukula mwa Khristu:

**Koma ndi kucita zoonu mwa cikondi tikakule m'zinthu zonse, kufikira iye amene ali mutu ndiye Kristu (Aefeso 4:15)**

Kukula mu uzimu kumatanthauza kuchepetsa umwini ndi kukulitsa moyo wa Khristu mwa iwe:  
**Iyeyo ayenera kukula koma ine ndicepe (Yohane 3:30)**

Kukula mu uzimu sikumabwera nthawi imodzi chifukwa cha kukhala nthawi yaitali ya mkhristu. Ndi zotsatira za kukula kwa moyo wa chikhristu mwa okhulupirira.

Zizindikiro za kukula mu uzimu ndi:

1. Kuchuluka kwa chidziwitso cha uzimu
2. Kugwiritsa ntchito bwino chidziwitsocho pa moyo ndi utumiki.
3. Kukhala ndi kuya kwa zinthu za uzimu.
4. Kukhala ndi chikondi chachikulu pa Mulungu ndi anthu ena.
5. Kuumbika kwa moyo wa chikhristu mmakhalidwe a uzimu (zipatso za uzimu).
6. Kukula kwa khumbo ndi kuthekera kugawana uthenga wabwino ndi anthu ena.
7. Kukula ndi kugwiritsa ntchito mpatso za uzimu.

Kukula ndi zotsatira za moyo. Ngati pali moyo wa uzimu mu mpingo, kukula kwa mkati kuzabweretsa kukula mu chiwerengero, mmadera, ngakhale kukula mmalire.

## **MZIMU WOYERA NDI KUKULA KWA MKATI**

Mu chaputala chathachi munaphunzira za utumiki wa Mzimu Woyera ku mpingo. Mzimu Woyera:

- amapanga Mpingo.
- amatakasa Mpingo.
- amatsogolera ntchito ya umishoni.
- amasankha atumiki.
- amadzodza alaliki ache.
- amatsogolera ziganizo.

-amabatiza ndi mphamvu.

Kuonjezera zku mautumuki mu mpingo, Mzimu Woyera ali ndi ntchito zina mogwirizana ndi makulidwe a mkati a mpingo. Izi ndi monga:

### **KUTSUTSA UCHIMO:**

Kukula mu uzimu kumatchingidwa ndi uchimo. Motero Mzimu Woyera amatsutsa tchimo kwa okhulupirira:

**Ndipo atadza Iyeyo, adzatsutsa dziko lapansi za macimo, ndi za cilungamo, ndi za ciweruziro;**

**za macimo, cifukwa sakhulupirira Ine;**

**za cilungamo, cifukwa ndinka kwa Atate, ndipo simundionanso;**

**za ciweruziro, cifukwa mkuru wa dziko ili lapansi waweruzidwa (Yohane 16:8-11).**

Pamene Mzimu Woyera akutsutsa za uchimo, pamenepo ndiye kuti tikhoza kutsatira lamulo...

**Ngati tibvomereza macimo athu, ali wokhulupirika ndi wolungama iye, kuti atikhululukire macimo athu, ndi kutisambitsa kuticotsera cosalungama ciri conse (I Yohane 1:9).**

### **KUKONZEDWANSO:**

Uku kumatanthauza “kusinthika.” Mzimu Woyera amasintha moyo wa okhulupirira. Kusintha uku kumabweretsa kukula kwa mkati:

**Zosati zocokera m'nchito za m'cilungamo, zimene tidazicita ife, komatu monga mwa cifundo cace anatipulumutsa ife, mwa kutsuka kwa kubadwanso ndi makonzedwe a Mzimu Woyera (Tito 3:5).**

### **CHIYERETSO:**

Chiyeretso ndi “kupatulikira Mulungu.” Kupatulikaku kumabweretsa kukula ku uzimu:

**Koma tiyenera ife tiziyamika Mulungu nthawi zonse cifukwa: ca inu, abale okondedwa ndi Ambuye, kuti Mulungu anakusankhani inu kuyambira paciyambi,**



**mulandire cipulumutso mwa ciyeretso ca Mzimu ndi cikhulupiriro ca coonadi (II Atesalonika 2:13).**

### **KUKHALA NAYE:**

Mzimu Woyera amakhala mmoyo wa wa okhulupirira. Cholinga cha chimenechi ndi kulimbikitsa chikhalidwe chatsopano chimene chinabwera chifukwa cha chipulumutso:

**Kapena simudziwa kuti thupi lanu liri kacisi wa Mzimu Woyera, amene ali mwa inu, amene muli naye kwa Mulungu? Ndipo simukhala a inu nokha (I A korinto 6:19).**

**Kodi simudziwa kuti muli Kacisi wa Mulungu, ndi kuti Mzimu wa Mulungu agonera mwa inu? (I Akorinto 3:16).**

**Cifukwa cace ngati munthu ali yense ali mwa Kristu ali wolengedwa watsopano; zinthu zakale zapita, taonani, zakhala zatsopano (II Akorinto 5:17).**

**Koma ndinena, Muyendeyende ndi Mzimu, ndipo musafitse cilakolako ca thupi.**

**Pakuti thupi lilakalaka potsutsana naye Mzimu, ndi Mzimu potsutsana nalo thupi; pakuti izi sizilingana; kuti zimene muzifuna musazicite.**

**Ngati Mzimu akutsogolerani, simuli omvera lamulo (Agalatiya 5:16-18).**

### **KULIMBIKITSA:**

Kulimbikitsa ndi kukula zimayendera limodzi. Umakhala wamphamvu pamene ukukula. Zimatengera mphamvu kuti munthu ukule. Kukula kwa mkati kumabwera kudzera mu kulimbikitsidwa kwa Mzimu Woyera:

**Kuti monga mwa cuma ca ulemerero wace akulimbikitseni inu ndi mphamvu mwa Mzimu wace, m'kati mwanu (Aefeso 3:16).**

### **UMODZI:**

Umodzi umabweretsa kukula mkati kwa Mpingo:

**Koma iye wophatikidwa ndi Ambuye ali mzimu umodzi (I Akorinto 6:17).**

**Pakuti monga thupi liri limodzi, nilikhala nazo ziwalo zambiri; koma ziwalo zonse za thupilo, pokhala zambiri, ziri thupi limodzi; momwemonso Kristu.**

**Pakutinso mwa Mzimu mmodzi ife tonse tinabatizidwa kulowa m'thupi limodzi, ngakhale Ayuda, ngakhale Ahelene, ngakhale akapolo, ngakhale mfulu; ndipo tonse tinamwetsedwa Mzimu mmodzi (I Akorinto 12:12-13).**

#### **KUPEMBEDZERA:**

Kupembedzera kwa Mzimu Woyera kumamanga moyo wa wokhulupirira ku uzimu:

**Ndipo momwemonso Mzimu athandiza kufoka kwathu; pakuti cimene tizipempha monga ciyenera, sitidziwa; koma Mzimu mwiniatipempherera ndi zobuula zosatheka kuneneka (Aroma 8:36).**

**Koma inu, okonedwa, podzimangirira nokha pa cikhulupiriro canu coyeretsetsa, ndi 4 kupemphera mu Mzimu Woyera (Yuda 20).**

**Mwa pemphero lonse ndi pembedzero mupemphere nthawi yonse mwa Mzimu, ndipo poezera pamenepo cicezerere ndi kupembedzera oyera mtima onse (Aefeso 6:18).**

#### **CHITSOGOZO:**

Mzimu Woyera amatsogoza okhulupirira ku choonadi chonse cha Mau a Mulungu chimene chimabweretsa kukula kwa mu uzimu:

**Koma atadza Iyeyo, Mzimu wa coonadi, adzatsogolera inu m'coonadi conse; pakuti sadzalankhula za iye mwini; koma zinthu ziri zonse adzazimva, adzazilankhula; ndipo zinthu zirinkudza adzakulalikirani (Yohane 16:13).**

**Pakuti onse amene atsogozedwa ndi Mzimu wa Mulungu, amenewo ali ana a Mulungu (Aroma 16:14).**

#### **MAVUMBULUTSO:**

Mzimu Woyera amavumbulutsa choonadi cha Mau a Mulungu kwa okhulupirira chimene chimabweretsa kukula mu uzimu:

**Koma kwa ife Mulungu anati onetsera izi mwa Mzimu; pakuti Mzimu asanthula zonse, zakuya za Mulungu zomwe (I Akorinto 2:10).**

#### **CHIKONDI:**

Anthu amakulu mu uzimu pamene akuonetsera chikondi:

**Ndipo ciyembekezo sicicititsa manyazi; cifukwa cikondi ca Mulungu cinatsanulidwa m'mitima mwathu mwa Mzimu Woyera, amene wapatsidwa kwa ife (Aroma 5:5).**

#### **KUFANANA:**

Mzimu Woyera amakhala pa yotifanizira ife ndi Yesu mkati mwathu:

**Koma ife tonse ndi nkhope yosaphimbika popenyenera monga mwa kalirole ulemerero wa Ambuye, tisandulika m'cithunzihunzi comweci kucokera kuulenerero kumka kuulemerero, monga ngati kucokera kwa Ambuye Mzimu (II Akorinto 3:18).**

#### **KUPHUNZITSA:**

Timakula ku uzimu pamene tikukula mu chidziwitso cha Mulungu cha Mulungu. Mzimu Woyera ndi mphunzitsi wathu.

**Ndipo inu, kudzoza kumene munalandira kucokera kwa iye, kukhala mwa inu, ndipo simusowa kuti wina akuphunzitseni; koma 9 monga kudzoza kwace kukuphunzitsani za zinthu zonse, ndipo kuli koono, sikuli bodza ai, ndipo monga kudaphunzitsa inu, mukhale mwa iye (I Yohane 2:27).**

#### **CHITSIMIKIZO:**

Kukaika kumatchinga kukula kwa uzimu. Mzimu Woyera amachotsa kukaika paukutipatsa chitsimikizo cha chipulumutso:

**Mzimu yekha acita umboni pamodzi ndi mzimu wathu, kuti tiri ana a Mulungu (Aroma 8:16).**

**Ndipo 6 munthu amene asunga malamulo ace akhala mwa iye, ndi iye mwa munthuyo. Ndipo 7 m'menemo tizindikira kuti akhala mwa ife, kucokera mwa Mzimu amene anatipatsa ife (I Yohane 3:24).**

## **UFULU:**

Zotchinga zimaika malire pa kukula. Mzimu Woyera amapatsa ufulu pa uchimo ndi zikhulupiriro za anthu:

**Pakuti cilamulo ca mzimu wa moyo mwa Kristu Yesu candimasula ine ku lamulo la ucimo ndi la imfa (Aroma 8:2)**

**Koma Ambuye ndiye Mzimuyo; ndipo pamene pali Mzimu wa Ambuye pali ufulu (II Akorinto 3:17).**

## **KUTONTHOZA:**

Nkhawa ndi kufooketsedwa kumatchinga kukula kwa moyo wa uzimu. Mzimu Woyera amapereka chitonthozo:

**...ndipo unayenda m'kuopa kwa Ambuye ndi m'cithonhozo ca Mzimu Woyera, nucuruka (Machitidwe 9:31).**

**Ndiye Mzimu wa coonadi; amene dziko lapansi silingathe kumlandira, pakuti silimuona iye, kapena kumzindikira iye. Inu mumzindikira iye; cifukwa akhala ndi inu nadzakhala mwa inu...**

**Koma Nkhosweyo, Mzimu Woyera, amene Atate adzamtuma m'dzina langa, Iyeyo adzaphunzitsa Inu zonse, nadzakumbutsa inu zinthu zonse zimene ndinanena kwa inu (Yohane 14:17,26).**

## **KUDZUTSA:**

Umodzi mwa mautumiki a Mzimu Woyera mmoyo wa Yesu unali kudzutsa Iye kwa akufa.

**Koma ngati Mzimu wa iye amene adaukitsa Yesu kwa akufa akhalabe mwa inu, iye amene adaukitsa Kristu Yesu kwa akufa adzapatsanso moyo matupi anu akufa, mwa Mzimu wace wakukhala mwa inu (Aroma 8:11).**

Ngati simukukula ku moyo wanu wa uzimu, ndiye kuti mumakhala “wakufa” ku uzimu. Kukula kumatha. Pakuti ndi mphamvu ya Mzimu Woyera imene imadzutsa inu moyo wanu wa uzimu.

## **KUONETSERA MPHAMVU:**

Paulo anati:

**Ndipo mau anga ndi kulalikira kwanga sanakhala ndi mau okopa a nzeru, koma m'cionetso ca Mzimu ndi ca mphamvu;**

**kuti cikhulupiriro canu cisakhale m'nzeru ya anthu, koma mu mphamvu ya Mulungu (I Akorinto 2:4-5).**

Chionetsero cha mphamvu ya Mzimu Woyera chimakulitsa chikhulupiriro chanu mwa Mulungu.

#### **MPHAMVU YA KUCHITIRA UMBONI:**

Mphamvu yapadera ya kuchitira umboni ndi chizindikiro kuti munthu wabatizidwa mwa Mzimu Woyera:

**Komatu mudzalandira mphamvu, Mzimu Woyera atadza pa inu: ndipo mudzakhala mboni zanga m'Yerusalemu, ndi m'Yudeya lonse, ndi m'Samariya, ndi kufikira malekezere ace a dziko (Machitidwe 1:8).**

Akhristu okhwima mu uzimu adzachelukana pochitira umboni wa uthenga wabwino.

#### **KUBATIZA:**

Mpingo umakula mkati kudzera mu ubatizo wa Mzimu Woyera:

**Ndipo anadzazidwa onse ndi Mzimu Woyera, nayamba kulankhula ndi malilime ena, monga Mzimu anawalankhulitsa (Machitidwe 2:4).**

Ubatizo wa Mzimu Woyera kukula kwa mphatso za Mzimu ndi zipatso mmoyo wa okhulupirira.

#### **KUPEREKA MPHATSO ZA MZIMU:**

Mphatso za mzimu ndi zofunikira pa kukula kwa Mpingo chifukwa “zimalimbikitsa” wokhulupirira. Moti “kulimbikitsa” kumatanthauza “kumanga ndi kukweza kukula kwa moyo wa uzimu.” (Muphunzira za mphatso za mzimu muphunziro likubwerali).

#### **KUKWEZA CHIPATSO ZA UZIMU:**

Chipatso cha Mzimu ndi chikhalidwe cha Mzimu choululidwa mmoyo wa okhulupirira. Zimenezi zimatanthauza makhalidwe a uzimu amene ndi zizindikiro mu moyo wa okhulupirira.

Chipatso cha Mzimu ndi chizindikiro cha kukula mu uzimu. Monga chipatso cha dziko lapansi, ndi zotsatira za makhalidwe a uzimu amene ndi zotsatira za moyowu. Monga chipatso chimatenga nthawi kuti chikule mu dziko lapansi, chipatso cha mzimu chimatenganso nthawi kuti chikule. Zimenezi ndi zotsatira za kukula kwa mkati kwa moyo wa okhulupirira.

Izi ndi zipatso Mzimu Woyera:

**Koma cipatso ca Mzimu ndico cikondi, cimwemwe, mtendere, kuleza mtima, cifundo, kukoma mtima, icikhulupiriro, cifatso, ciletso; pokana zimenezi palibe lamulo (Agalatiya 5:22-23).**

Mulungu amafuna inu kuti mukule mu:

Chikondi: chikondi cholama, chisamaliro, ndi kukhuzidwa

Chimwemwe: chisangalalo, kukondwa, kunyadira zimane sizimadalira zochitikaza moyo.

Mtendere: bata, chiyanjano, kudekha, kupanda nkhwana ndi madandaulo, maudani.

Kuleza mtima: kudikira-kuthekera kopilira mu nyengo yowawa, chipiliro.

Kufatsa: ulemu kwa anthu ena, kupanda nkhanza, kudekha.

Ubwino: machitidwe a chiyero ndi chilungamo.

Chikhulupiriro: maganizo okhala ndi kudalira pa Mulungu.

Kudekha: kukhala ndi kuthekera koletsa mphamvu.

Kukhazikika: maganizo abwino, ntchito zabwino, kudziletsa.

## **ZOPANGITSA KUKULA**

Mu dzikoli lapansi pali zinthu zimene zimapangitsa kukula kwa zipatso. Zinthu za chilengedwe zimenezi zimafanana ndi za uzimu zofunika kukula kwa moyo wobereka chipatso. Izi ndi zina zimene zimafanana:

### **MOYO:**

Kukula mkosatheka popanda moyo. Kukula kwa chipatso kumayamba kuchokera ku mbewu.

Pamayenera kukhala moyo mu mbewu, kupanda kutero zingakule. Pakufanizira fanizo la ofesa, “mbewu” ndiye mau a Mulungu. Kukula kumabwera kudzera mbewu ya Mau a Mulungu.

**Lirani monga makanda alero mkaka woyenera, wopanda cinyengo, kuti mukakule nao kufikira cipulumutso (I Petro 2:2).**

Yesu anali ndi chionetsero cha Mau a Mulungu, mbewu, ndipo mwa Iye munali moyo:

**Mwa iye munali moyo; ndi moyowu unali kuunika kwa anthu (Yohane 1:4).**

**Pakuti monga Atate ali ndi moyo mwa iye yekha, momwemonso anapatsa kwa Mwana kukhala ndi moyo mwa iye yekha (Yohane 5:26).**

Yesu anadza kudzafeso mbewu ya moyo yopangitsa moyo wauzimu kukula.

**Siikudza mbala, koma kuti ikabe, ndi kupha, ndi kuononga, Ndadza Ine kuti akhale ndi moyo, ndi kukhala nao wocuruka (Yohane 10:10).**

### **NTHAKA YABWINO:**

Mbewu ya Mau a Mulungu imayenera kukhalandi nthaka yabwino kuti ikule bwinobwino. Werengani fanizo la wofesa mu Marko 4. Mbewu yokhayo imene yagwera panthaka yabwino imabweretsa kukula kwa ku uzimu:

**Ndipo iwo ofesedwa pa nthaka yabwino ndiwo oterewa akumva mau, nawalandira, nabala zipatso zakupindula makumi atatu, ndi makumi asanu ndi limodzi, ndi makumi khumi (Marko 4:20).**

Mukuyenera kukonzekeretsa “nthaka” ya mtima wanu ndi maganizo anu kuti mulandire Mau a Mulungu.

### **MADZI:**

Madzi ndi wofunika pa kukula kwa zinthu mu dzikoli. Mulungu analonjeza:

**Pakuti ndidzathira madzi pa dziko limene liribe madzi, ndi mitsinje pa nthaka youma (Yesaya 44:3).**

Kutsanulira kumeneku ndi kudzodza kwa Mzimu Woyera kwa madzi amene ndi chizindikiro:

**Iye wokhulupirira Ine, monga cilembo cinati, Mitsinje ya madzi amoyo idzayenda, kuturuka m'kati mwace (Yohane 7:38).**

Madzi a Mzimu Woyera amapangitsa mbewu ya Mawu a Mulungu kuzika mizu mmitima ya anthu amene ndi okufa mu uzimu:

**Pakuti akaulikha mtengo pali ciyembekezo kuti udzaphukanso, Ndi kuti nthambi yace yanthete siidzasowa.**

**Ngakhale muzu wace wakalamba m'nthaka, Ndi tsinde lace likufa pansu;**

**Koma pa mnunkho wa madzi udzaphuka, Nudzaswa nthambi ngati womera (Yobu 14:7-9).**

**KUWALA:**

Uku ndi kuyankha kuwala kumene kumapangisa kukula mu dziko lapansi. Kukula ku uzimu kumayamba polandira kuwala kwa uzimu. Kuwalaku ndi Yesu.

**Mwa iye munali moyo; ndi moyowu unali kuunika kwa anthu (Yohane 1:4).**

**Ine ndine kuunika kwa dziko lapansi; iye wonditsata ine sadzayenda mumdima, koma adzakhala nako kuunika kwa moyo (Yohane 8:12).**

**MPWEYA:**

Mpweya umabwera kuchokera ku chilengedwe cha zomera mulengalenga. Mpweya ndi wofunika pa kukula. Mu Baibulo Mzimu Woyera amafanizidwa ngati mpweya kapena mphepo.

**Mphepo iomba pomwe ifuna, ndipo ukumva mau ace, komavsudziwa, kumene icokera, ndi kumene imuka; coteru ali yense wobadwa mwa Mzimu (Yohane 3:8).**

Mzimu Woyera amapumwira mmoyo wa mbewu ya Mau a Mulungu. Kukula ku uzimu ndi zipatso zimakhala zotsatira.

**MPATA:**

Mu fanizo la ofesa, kulimbirana mpata kumapangisa kuti mbewu zina zife:

**Ndipo iye amene afesedwa kuminga, uyu ndiye wakumva mau; ndipo kulabadira kwa dziko lapansi, ndi cinyengo ca cuma citsamwitsa mau, ndipo akhala wopanda cipatso (Mateyu 13:22).**

Mpikisano wa zinthu za dziko zimatsamwitsa mbewu ya Mau a Mulungu ndi kulepheretsa kukula kwa uzimu.

**MPUMULO:**

Nthawi ya mpumulo (yotchedwa yongokhala) imakhala nyengo yapadera ya kubwerezeka kwa zomera mu dziko lapansi. Imeneyi ndi nthawi ya mpumulo wa zomera ndi nyengo imene ndi



yachisanu ya kukula kwambiri. Mu nthawi yongokhala, zomera zimaoneka ngati zafa. Koma zimakhala zisanafe. Mbewu ya moyo imakhala ili mkati.

Nthawi zina munthu kapena mpingo umatha kuoneka ngati sukukula mu uzimu. Koma ngati mbewu ya Mau a Mulungu yadzalidwa bwino, kukula kwa mkati kudzachitika (Masalmo 1).

Monga ngati mdziko, kungokhala mu uzimu kumabwera pambuyo pa kukula kwambiri ndi kuumbika. Dikirani modekha pa kukula kwa mkati ndi kuchuluka ku zipatso za mzimu:

**Taonani, wolima munda alindira cipatso cofunikatu ca dziko, ndi kuleza mtima naco kufikira cikalandira mvula ya myundo ndi masika (Yakobo 5:7).**

#### **MIZU YAKE:**

Mizu ndi yofunikira kulimbisa ndi kupereka zofunika ku mtengo. Masalmo 1 amatuiza za mmene mizu ilili mmoyo wa uzimu:

**Wodala munthuyo wosayenda mu uphungu wa oipawosakhala pansu pa bwalo la onyoza.**

**Komatu m'cilamulo ca Yehova muli cikondwerero cace;**

**Ndipo m'cilamulo cace amalingima usana ndi usiku.**

**Ndiye akunga mtengo wooka pa mitsinje ya madzi; Wakupatsa cipatso cace pa nyengo yace,**

**Tsamba lace lomwe losafota; Ndipo zonse azicita apindula nazo (Masalmo1:1-3).**

#### **IMFA:**

Nthawi yonse imene mudzala mbewu kti ibereke, zingakhale ndi moyo ngati siyamba yafa kaye:

**Indetu, indetu, ndinena ndi inu, Ngati mbeu ya tirigu siigwa m'nthaka, nifa, ikhala pa yokha iyo; koma ngati ifa, ibala cipatso cambiri (Yohane 12:24).**

**Wopusa iwe, cimene ucifesa wekha sicikhalitsidwanso camoyo, ngati sicifa (I Akorinto 15:36).**

Moyo wa uzimu umadalira kufa kwa zinthu zina za dziko lapansi. Umafuna kufa ku tchimo, zokhumba za dziko, ndi zosangalasa. Kufa ku za dziko kumasatira kukula kwa moyo wachipatso wofanana ndi Khristu mmoyo wanu.

## **KULUMIKIZIKA KU MPESA:**

Kuti mubale chipatso mu dziko lapansi nthambi iyenera kulumikizika ku mtengo. Ngati nthambi yadulidwa ku mtengo umene umapereka moyo ndiye kuti idzafa.

Yesu ndiye mpesa ndipo ife ndi nthambi. Choncho kuti ife tikabale chipatso cha uzimu tiyenera kusungabe ubale wathu ndi Iye:

**Ine ndine mpesa weniweni, ndipo Atate wanga ndiye wam'munda.**

**Nthambi iri yonse ya mwa Ine yosabala cipatso, aicotsa; ndi iri y'onse yakubala cipatso, aisadza, kuti ikabale cipatso cocuruka.**

**Mwakhala okonzeka tsopano inu cifukwa ca mau amene ndalankhula ndi inu,**

**Khalani mwa Ine, ndi Ine mwa inu. Monga nthambi siingathe kubala cipatso pa yokha, ngati siikhala mwampesa; motere mulibe inunso ngati simukhala mwa Ine.**

**Ine ndine mpesa, inu ndinu nthambi zace: wakukhala mwa Ine, ndi Ine mwa iye, ameneyo abala cipatso cambiri; pakuti kopanda Ine simungathe kucita kanthu (Yohane 15:1-5).**

## **KUTSAZA:**

Kutsaza ndi kofunikira mu dziko lapansi ngati tikufuna kuti zomera zikhale zoberekana zipatso. Pamene mlimi atsanza mtengo amadula nthambi zosafunika ndi cholinga chopanga mtengowo kuti ubale zipatso zambiri. Amachotsa chilichonse chimene chimatchinga makulidwe a mtengo.

Kutsanza ndi kofunikanso ku dziko la uzimu. Kutsanza ku uzimu ndi kukonzedwa ndi Mulungu. Baibulo limatchula kuti chilango. Pamene Mulungu “atsanza” amachotsa chilichonse chimene chilepheretsa kukula moyo wanu wa uzimu. Machitidwewa ndi ofunika ngati mufuna kuti mubale chipatso:

**Nthambi iri yonse ya mwa Ine yosabala cipatso, aicotsa; ndi iri y'onse yakubala cipatso, aisadza, kuti ikabale cipatso cocuruka (Yohane 15:2).**

Nthawi zina simukolola zotsatira za kutsanza chifukwa mumloza chala Satana pamene ali Mulungu kubweretsa zinthu mmoyo wanu kuti akukonzeni (kutsanza). Cholinga cha kukonza kwa Mulungu chikupezeka pa Hoseya 6:1:

Tiyeni, tibwerere kunka kwa Yehova; pakuti wang'amba, nadzatipoletsera; wakantha, nadzatimanga (Hoseya 6:1).

Chilango cha kutsanza chimatsatira kubwerera kwa Mulungu. Pokhapo pamene tabwerera kwa Iye pamenepo mudzakhala ochitachita ku uzimu ndi kubala chipatso cha Mzimu Woyera.

### **NYENGO:**

Nyengo ndi yofunika pa kukula kwa chipatso. Mu dziko lathuli zipatso za mitundu yambiri zimakula mu nyengo imene imatetezedwa. Zimakula mnyumba zotchedwa “nyumba zotentha” pamene pamakhala kutentha kwapadera. Zimatetezedwa ku nyengo imene ili pa dziko.

Mukatenga “nyumba yotentha” mkudzala ndi kuchotsa, mwamsanga chidzafa chifukwa chakhala pa nyengo yotetezedwa. Sichingalimbe ndi nyengo imene ilipo mdziko. Kulankhula ku uzimu, simufunika “nyumba yotentha” akhristu amene amaoneka abwino mu nyengo inayake koma amafota akapezana ndi zenizeni za dziko.

## MAYESO ODIYETSA NOKHA

1. Lembani Vesi Lotsogolera kuchokera pantima.

---

---

---

2. Kodi timatanthauza chani tikamakamba za kukula kwa mkati kwa Mpingo?

---

---

---

3. Kodi kukula mu uzimu ndi chiyani?

---

---

4. Lembani zizindikiro 7 za kukula mu uzimu.

---

---

---

---

5. Mwaphunzira njira zambiri za mmene Mzimu Woyera amakhudzira kukula mkati kwa mpingo. Lembani zimene mungathe:

---

---

---

6. Mwaphunziranso za nyengo za kakulidwe ka moyo wa uzimu zimene ndi zofanana ndi za mdziko lapansi. Lembani zimene mungathe.

---

---

(Mayankho a mafunsowa akupezeka kumapeto kwenikweni kwa bukuli)

## KUPITILIZA KUPHUNZIRA

1. Pamene mtengo wayandikira kufa mu dzikoli, umayenera kuti utsitsimudwe. Momwemonso Mpingo ukayandikira kufa, chitsitsimutso chimafunika. Kutsitsimula ndiye kuti “kukhala ndi moyo kawiri.” Werengani mawuwa:

Kulirira chitsitsimutso: Masalmo 85:6      Dongosolo la Mulungu la chitsitsimutso: II Mbiri 7:14

Werengani mavesiwa amene akukamba za chitsitsimutso mu chipangano chatsopano. Kodi ndi zinthu ziti zimene zinabweretsa chitsitsimutso? Nanga zotsatira za chitsitsimutso zinali chiyani?

Chitsitsimutso ku Sinai:                      Eksodo 32:1-35; 33:1:23  
Chitsitsimutso mu nthawi ya Samueli:      I Samueli 7:1-17  
Chitsitsimutso pa phiri la Karimeli:      I Mafumu 18:1-46  
Chitsitsimutso ku Ninevi:                  Buku la Yona  
Chitsitsimutso mu nthawi ya Asa:      II Mbiri 15  
Chitsitsimutso mu nthawi ya Hezekiya:      II Mbiri 29:1-36; 30:1-27; 31:1-21  
Chitsitsimutso mu nthawi ya Yosiyah:      II Mbiri 34:1-33; 35:1-19  
Chitsitsimutso utatha ukapolo:          Nehemiya 8:1-18

2. Muchaputala chomalizachi mwaphunzira kuti mpingo umafanizidwa ndi nyumba ya uzimu yomangidwa pa maziko a Yesu Khristu. Kukula kwa mkati kwa uzimu ndi njira yomanga pa maziko amenewa. Werengani magawowa:

## KUKULA PA KUMANGA

### MFUNDO ZIKULUZIKULU:

A. Kodi mukumanga chiyani ku uzimu?

1. Inu ndiye mamangidwe:

**Inunso ngati miyala yamoyo mumangidwa nyumba ya uzimu... (I Petro 2:5)**

2. Inu ndi mamangidwe a muyaya:

**Pakuti tidziwa kuti ngati nyumba ya panso pano ya msasa wathu ipasuka, tiri naco cimango ca kwa Mulungu, ndiyo nyumba yosamangidwa ndi manja, yosatha, m'Mwamba (II Akorinto 5:1)**

3. Mpingo ndi mamangidwe:

**...Omangika pa maziko a atumwi ndi aneneri, pali Kristu Yesu mwini, mwala wa pangondya; mwa iye cimango conse, columikizika pamodzi bwino, cikula, cikhale kacisi wopatulika mwa Ambuye; cimene inunso mumangidwamo pamodzi, mukhale cokhalamo Mulungu mwa Mzimu (Aefeso 2:20-22)**

B. Pali awiri amene akutenga nawo gawo:

1. Mulungu

...Koma wodzimanga zonse ndiye Mulungu. (Ahebri 3:4).

Akapanda kumanga nyumba Yehova, Akuimanga agwiritsa nchito cabe;  
Akapanda kusunga mudzi Yehoya (Masalmo 127 :1)

...Ndipo pa thanthwe ili ndidzakhazika Mpingo wanga; ndipo makomo a dziko la akufa sadzaulaka uwo (Mateyu 16:18)

2. Munthu: Munthu, mu ubale ndi Mulungu, akuyenera kumanga:

Pakuti ife ndife anchito anzace a Mulungu; cilimo ca Mulungu, cimango ca Mulungu ndi inu (I Akorinto 3:9)

podzimangirira nokha pa cikhulupiriro canu coyeretsetsa (Yuda 20)

Ndipo iwo amene adzakhala a iwe adzamanga malo akale abwinja; udzautsa maziko a mibadwo yambiri; udzachedwa Wokonza pogumuka, Wakubwezera njira zakukhalamo (Yesaya 58:12)

### **MUSANAYAMBE KUMANGA:**

Musanayambe kumanga muyenera:

1. Muwerengere mtengo wake:

Pakuti ndani wa inu amene akafuna kumanga nsanja yaitali, sathanga wakhala pansu, nawerengera mtengo wace, aone ngati ali nazo zakuimariza? 29Kuti kungacitike, pamene atakhazika pansu miyala ya ku maziko ace, osakhoza kuimariza, anthu onse akuyang'ana adzayamba kumseka iye, 30ndi kunena kuti, Munthu uyu anayamba kumanga, koma sanathe kumariza (Luka 14:28-30)

2. Khalani otsimikizika:

Ndipo a Solomo anati alimangire dzina la Yehova nyumba... (II Mbiri 2:1)

3. Khalani ndi malingaliro abwino:

Taonani, nditi ndilimangire dzina la Yehova Mulungu wanga nyumba, kumpatulira iyo, ndi kufukiza pamaso pace zonunkhira za pfungo lokoma (II Mbiri 2:4)

4. Kukonzeka:

Pakuti Ezara adaikiratu mtima wace kucifuna cilamulo ca Yehova, ndi kucicita, ndi kuphunzitsa m'Israyeli malemba ndi maweruzo... (Ezara 7:10)

Ndipo 4 kapolo uyo, wodziwa cifuniro ca mbuye wace, ndipo sanakonza, ndi kusacita zonga za cifuniro caceco, (Luka 12:47)

### **TIMANGE BWANJI:**

1. Mangani pa maziko abwino:

**Munthu wamzeru amamanga pa maziko a Mau a Mulungu...amene simagwa chifukwa imakhala pa thanthwe (Mateyu 7:24-27)**

Maziko abwino ndiye Yesu ndi Mau ake:

**omangika pa maziko a atumwi ndi aneneri, pali Kristu Yesu mwini, mwala wa pangondya (Aefeso 2:20)**

**Ozika mizu ndi omangirika mwa iye, ndi okhazikika m'cikhulupiriro, monga munaphunzitsidwa, ndi kucurukitsa ciyamiko (Akolose 2:7)**

Musamalitse mmene mukumangirapa mazikowa:

**Monga mwa cisomo ca Mulungu cidapatsidwa kwa ine, ngati mwini mamangidwe waluso, ndinaika maziko, koma wina amangapo. Koma yense ayang'anire umo amangira pamenepo. 11Pakuti palibe munthu akhoza kuika maziko ena, koma amene aikidwako, ndiwo Yesu Kristu.**

**Koma ngati wina amanga pa mazikowo, golidi, siliva, miyala va mtengo wace, mtengo, maudzu, dziputu,**

**nchito ya yense idzaonetsedwa; pakuti tsikulo lidzaisonyeza, cifukwa kuti yabvumbuluka m'moto; ndipo mota wokha udzayesera nchito ya yense ikhala yotani (I Akorinto 3:10-13)**

2. Mangani molingana ndi dongosolo:

Mamangidwe ena aliwonse a Mbaibulo, pamakhala dongosolo la Mulungu. Onani Genesis 6: Eksodo 25:1 Mbiri 22. Anthu anamvera dongosolo la Mulungu:

**Cotero anacita Nowa, monga mwa zonse anamlamulira iye Mulungu, momwemo anacita (Genesis 6:22)**

Dongosolo linali losiyana, koma chomwechonso zinali ndi Mose, Davide, Solomoni, Ezarandi Nehemiya molingana ndi mmene Ambuye anawalamulira.

**Conseci, anati Davide, anandidziwitsa ndi kucilemba kucokera kwa dzanja la Yehova; ndizo nchito zonse za cifaniziro ici (I Mbiri 28:19)**

Ngati simukusatira dongosolo la Mulungu la moyo wanu pa Mau a Mulungu, simudzapambana:

**Pakuti sasamala nchito za Yehova, Kapena macitidwe a manja ace, Adzawapasula, osawamanganso (Masalmo 28:5)**

3. Mangani molingana ndi kuthekera kwanu:

Pa zokhudza mamangidwe mu nthawi ya Chipangano Chakale, anthu anapereka molingana ndi kutherekerera kwawo:

**Monga momwe anakhoza anapereka ku Cuma... (Ezara 2:69)**

4. Mangani mofuna:

Funani kukula mu uzimu:

**Anapereka caufulu kwa nyumba ya Mulungu cakulimika pakuzika pace (Ezara 2:68).**



5. Mangani mu mphamvu za Ambuye:

**...Motero ndinalimbika mtima, monga umo dzanja la Yehova Mulungu wanga linakhala pa ine (Ezara 7:28)**

6. Mangani mu Umodzi:

**...Popeza mitima ya anthu inalunjika kunchito (Nehemiya 4:6)**

7. Mangani Mwanzeru:

**Nzeru imangitsa nyumba; Luntha liikhazikitsa (Miyambo 24:3)**

**Mkazi yense wanzeru amanga banja lace; Koma wopusa alipasula ndi manja ace (Miyambo 14:1)**

**Nzeru yamanga nyumba yace, Yasema zoimiritsa zace zisanu ndi ziwiri (Miyambo 9:1)**

Mulungu adzakupatsa luntha:

**Ndipo ndamdzaza nd mzimu wa Mulungu, ndi luso, ndi nzeru, ndi cidziwitso, ndi m'nchito ziri zonse (Eksodo 31:3,6)**

**Nampatsa mfumu Davide mwana waluso, wodziwa nzeru ndi waluntha, ammagire Yehova nyumba, ndiponso nyumba ya ufumu wace (II Mbiri 2:12)**

Mwini luntha ndi Mulungu:

**Koma wina wa inu ikamsowa nzeru, apemphe kwa Mulungu, amene apatsa kwa onse modzala manja, niwosatonza; ndipo adzampatsa iye (Yakobo 1:5)**

## CHAPUTALA CHA 7

### KUKULA MU CHIWERENGERO

#### ZOLINGA:

Pakutha pa chaputalachi muyenera:

- Kulemba Vesi Lotsogolera kuchokera pamtima.
- Kulongosola tanthauzo la kukula mu chiwerengero.
- Kulemba chidule cha kukula mu chiwerengero kwa mpingo woyamba wa ku Yerusalemu.
- Lembani chidule cha njira za kukula kwa mpingo mu chipangano chatsopano.

#### VESI LOTSOGOLERA

**Ndipo mau a Mulungu anakula; ndipo ciwerengero ca akuphunzira cidacurukatu ku Yerusalemu (Machitidwe 6:7)**

#### MAWU OYAMBA

Mu thupi lathuli, ziwalo zambiri zalumikizika ndi mutu. Ntchito zonse za thupi zimabwera chifukwa zimachokera ku mutu. Yesu ndi mutu amene amapereka chitsogozo cha thupi lake la uzimu, ndiye mpingo. Yesu anati, “ndizamanga mpingo wanga” (Mateyu 16:18). Mu Baibulo, njira zake zofuna kukwaniritsa cholinga chake zaululika.

Njira zochulukitsa mpingo zikuyenera kuti zikhazikike pa zimene zinaphunzitsidwa ndi kuonetsedwa Mmau a Mulungu. Ngati ziwalo za thupi la Khristu, okhulupirira akuyenera kuchitapo kanthu pa zitsogozo zimene zimachokera ku mutu, ndiye Ambuye Yesu. Chaputala ichi ndi chimodzi mwa machaputala atatu amene amaika chidwi pa kukula kwa mamembala mu mpingo. Phunziro ili likukamba zambiri za kukula mu chiwerengero.

### KUKULA MU CHIWERENGERO

Kukula mu chiwerengero kumachitika pamene okhulupirira atembenuza munthu kupita kwa Khristu ndikumutengera ki chiyanjano cha mpingo. Zotsatira za izi ndi kukula kwa mpingo mu chiwerengero. Kukula mu chiwerengero kukuyenera kuloza ku kuchulukitsa Ufumu wa Mulungu.

Ngati mpingo wachiwiri unaonjezeka ndi anthu 100 kuchokera ku mpingo wina pa ma thiransifa, pamenepo kukula mu chiwerengero sikunachitike. Pakhala pali kuchulukika kwa mamembala ku

mpingo wachiwiri koma chiwerengero mu ufumu sichinachitike. Kukula kwa ufumu kumachitika pamene membala watsopano akutengedwera kwa Yesu ndi kuphunzitsidwa kukhala membala odalilika mu thupi la Khristu.

## **ZIMENE CHIPANGANO CHATSOPANO CHIMANENA**

Buku la Machitidwe limakamba za kukula kwa mpingo woyamba ku Yerusalemu mu chiwerengero. Izi ndi chidule cha mmene zinakhalira:

### **KAKULIDWE KAKE:**

**Ndipo m' masiku awa anaimirira Petro pakati pa abale, nati (gulu la anthu losonkhana pamalo pomwe ndilo ngati zana limodzi ndi makumi awiri) (Machitidwe 1:15)**

Mpingo unayamba mu chipinda cha pamwamba ndi gulu lochepa la ophunzira okwana 120. Pa tsiku la Pentekosite, anthu okwanira 3,000 anaonjezereka ku mpingo:

**Pamenepo iwo amene analandira mau ace anabatizidwa; ndipo anaonjezedwa tsiku lomwelo anthu ngati zikwi zitatu (Machitidwe 2:41).**

Itatha Pentekosite, kukula mu chiwerengero kumachitika tsiku ndi tsiku:

Chiwerengero cha anthu ku Yerusalemu chinakwera mkufika 5,000. Chiwerengerochi panalibe akazi ndi ana amene analinso gawo limodzi la mpingo:

**Koma ambiri a iwo amene adamva mau anakhulupira; ndipo ciwerengero ca amuna cinali ngati zikwi zisanu (Machitidwe 4:4)**

Kumapeto kwake, khamu la athu linaonjezereka:

**Ndipo makamaka anaonjezedwa kwa Ambuye okhulupirira ambiri, ndiwo amuna ndi akazi (Machitidwe 5:14)**

Ngakhale iwo amene amatsutsa mpingo anazizwa ndi kukulaku:

**Koma m'mene anamva mau awa mdindo wa Kacisi ndi ansembe akulu anathedwa nzeru ndi iwo aja, kuti ici cidzatani (Machitidwe 5:24)**

Mawu oti anaonjezedwa anagwiritsidwa ntchito polongosola kukula ku chiwerengero cha mpingo. Mwamsanga kukula kuja kunakhala kwakukulu moti mawu oti kukuchuka anagwira ntchito.

**Ndipo mau a Mulungu anakula; ndipo ciwerengero ca akuphunzira cidacurukatu ku Yerusalemu (Machitidwe 6:7)**

Kuchokera pa nthawi imeneyi, buku la Machitidwe limatsindika za kuchuluka kwa mipingo komanso mamembala a mpingo wa ku Yerusalemu. Mipingo yatsopano inadzalidwa mmalo onse a anthu a mitundu amene ndi odziwika mdziko osachepera za 40. Mwachitsanzo, ku Samariya...

**Koma pamene anakhulupirira Filipino wakulalikira Uthenga Wabwinowa Ufumu wa Mulungu ndi dzina la Yesu Kristu, anabatizidwa, amuna ndi akazi (Machitidwe 8:12)**

Mipingo yaku Yudeya, Galileya, Ludda, Sarona ndi Yopa inakula mu chiwerengero cha anthu:

**Pamenepo ndipo Mpingo wa m'Yudeya Ionse ndi Galileya ndi Samariya unali nao mtendere, nukhazikika; ndipo unayenda m'kuopa kwa Ambuye ndi m'cithonhozo ca Mzimu Woyera, nucuruka (Machitidwe 9:31)**

**Ndipo anamuona iye onse akukhala ku Luda ndi ku Sarona, natembenukira kwa Ambuye amenewa (Machitidwe 9:35,42)**

Anthu “ambiri anaonjezereka” ku mpingo kudzera mu utumiki wa Myuda mmodzi wotembenuka:

**Cifukwa anali munthu wabwino, ndi wodzala ndi Mzimu Woyera ndi cikhulupiriro: ndipo khamu lalikuru lidaonjezeka kwa Ambuye (Machitidwe 11:24)**

Mavesi atatu akukamba za chiwerengero chachikulu chimene chinaonjezereka ku Antioki:

**Ndipo dzanja la Ambuye linali nao; ndi unyinji wakukhulupira unatembenukira kwa Ambuye.**

**ndipo m'mene anampeza, anadza naye ku Antiokeya. Ndipo kunali, kuti caka conse anasonkhana pamodzi mu Mpingo, naphunzitsa anthu aunyinji; ndipo ophunzira anayamba kuchedwa Akristu ku Antiokeya (Machitidwe 11:21, 24,26).**

Pamene Mau a Ambuye amapitilira kulalikidwa ndi kuchuluka, okhulupirira atsopano amaonjezereka ku mpingo:

**Koma mau a Mulungu anakula, nacurukitsa (Machitidwe 12:24)**

**KUCHULUKA KUPITILIRA:**

Ndime zotsatirazi ndi chidule chabe cha kukula kwa mpingo kumadera ena:

**Ndipo mau a Ambuye anabukitsidwa m'dziko lonse. Koma Ayuda anakakamiza akazi opembedza ndi omveka, ndi akulu a mudziwo (Machitidwe 13:49-50)**

**Cotero mau a Ambuye anacuruka mwamphamvu nalakika (Machitidwe 19:20)**

**KUKULA KU IKONIYO**

**Ndipo kunali pa Ikoniyo kuti analowa pamodzi m'sunagoge wa Ayuda, nalankhula kotero, kuti khamu lalikuru la Ayuda ndi Ahelene anakhulupira (Machitidwe 14:1)**

**KUKULA KU DEBE**

Ku Debe, ophunzira anatsimikizidwa, kulimbikitsidwa ndi kukhala pamodzi ndi Paulo (Onani Machitidwe 14:20-21)

**KUKULA KU AGALATIYA:**

**Kotero Mipingoyo inalimbikitsidwa m'cikhulupiriro, nacuruka m'ciwerengo cao tsiku ndi tsiku (Machitidwe 16:5)**

**KUKULA KU FILIPO:**

**Ndipo anatimva mkazi wina dzina lace Lidiya, wakugulitsa cibakuwa, wa ku mudzi wa Tiyatira, amene anapembedza Mulungu; mtima wace Ambuye anatsegula, kuti amvere zimene anazinena Paulo (Machitidwe 16:14)**

**KUKULA KU ATESALONIKA:**

**Ndipo ena a iwo anakopedwa, nadziphatika kwa Paulo ndi Sila; ndi Ahelene akupembedza aunyinji ndithu, ndi akazi akuru osati owerengeka (Machitidwe 17:4)**

## **KUKULA KU BEREYA:**

**Ndipo ambiri a iwo anakhulupira; ndi akazi a Cihelene omveka, ndi amuna, osati owerengeka (Machitidwe 17:12)**

## **KUKULA KU AKORINTO:**

Ambuye anati “Ndili ndi anthu ambiri mu mzindawu” (Onani Machitidwe 18:8-11). Buku la Machitidwe limatha ndi Paulo akadali kukulitsabe mpingo, ngakhale anali wa mndende kwa Aroma:

**Ndipo anakhala zaka ziwiri zamphumphu m'nyumba yace yobwereka, nalandira onse akufika kwa iye,**

**ndi kulalikira Ufumu wa Mulungu, ndi kuphunzitsa za Ambuye Yesu Kristu ndi kulimbika konse, wosamletsa munthu (Machitidwe 28:30-31)**

Paulo nalemba **kuti zikwi za Ayuda ambiri anabwera kwa Yesu nakhala gawo la mipingo:**

**Ndipo pamene anazimva, analemekeza Mulungu; nati kwa iye, Uona, mbale, kuti ambirimбири mwa Ayuda akhulupira; ndipo ali naco cangu onsewa, ca pa cilamulo (Machitidwe 21:20)**

## **MMENE MPINGO UMAKULIRA**

Pali njira zambiri zimene mpingo oyamba unakulira:

## **MASOMPHENYA A UZIMU:**

**Popanda masomphenya anthu amatayika. (Miyambo 29:18)**

Popanda masomphenya a uzimu, anthu amafa ku uzimu. Mpingo woyamba unali ndi masomphenya a uzimu. Anali masomphenya amene Yesu anapereka kwa ophunzira ake pamene anawauza kuti....

**Onani ndinena kwa inu, Kwezani maso anu, nimuyang'ane m'minda, kuti mwayera kale kufikira kumweta (Yohane 4:35)**

Masomphenya a uzimu amalumikiza anthu pa cholinga. Masomphenya amatsogolera anthu kuchitukuko cha machitidwe. Machitidwe monga kumvetsa cholinga, ndi kuwaniritsa cholingacho komanso njira za kauniuni poonetsetsa kuti cholinga chikukwaniritsidwa.

Masomphenya amatsogolera kukhudzikwa. Pamene Yesu anaona khamu la anthu anakhudzika. Chinali chikatundu cholemera molingana ndi chidziwitso cha chosowa chawo. Masomphenya ndi kutukula kwa maonedwe a zinthu molingana ndi Baibulo, kumaliwona dziko molingana ndi mmene Mulungu amalionera ndi kuvomereza pa zimenezo.

Mpingo woyamba unatenga masomphenya ochulukitsa mpingo kuchokera ku Yerusalemu kupita ku Yudeya, Samariya ndi malekedzero onse a dziko lapansi. Anali masomphenya ophunzitsidwa ndi atsogolera awo (Machitidwe 1:8). Pamene anthu ali ndi masomphenya a uzimu chiyembekezo chimachotsa ulesi ndi umodzi wawo umachotsa mpikisano.

### **MALO NDI NTHAWI ZOLANDILIKA:**

Yesu anaphunzitsa kuti malo ena adzalandilidwa kuposa ena:

Awa amene, khumi ndi awiriwa, Yesu anawatumiza, nawalangiza ndi kuti,

**Musapite ku njira ya kwa anthu akunja, ndi m'mudzi wa Asamariya musamalowamo:**

**koma makamaka mupite ku nkhosa zosokera za banja la Israyeli**

**Ndipo yemwe sadzakulandirani inu, kapena kusamva mau anu, pamene mulikuturuka m'nyumbayo, kapena m'mudzimo, sansani pfumbi m'mapazi anu (Mateyu 10:5-6,14)**

Madera ena komanso magulu ena amalandira uthenga mu nthawi zina kuposa ena. Mpingo woyamba unagwira ntchito pa zokolola za uzimu zimene zimalandira uthengawo. Pamene Paulo anakanidwa ku Sunagoge, anaphunzitsa kwina (Machitidwe 9:20-31). Pamene amafuna kupita ku M' Asiya mu nthawi yoyamba, Mzimu Woyera anamuletsa (Machitidwe 16:6). Anadzapita nthawi ina imene analandira uthenga.

Kukula ku chiwerengero kumachitika pamene taika chidwi pa zokolola za mmunda mu nyengo yake. Izi sizitanthauza kuti mumasiya minda imene sinakonzekere ayi. Mumapitilizabe kufesa mau a Mulungu, kudikira, kupemphera kuti Mulungu awapangise kulandira uthenga.

### **NDONDOMEKO YA “PITANI OSATI “BWERANI”**

Mpingo woyamba umagwiritsa ntchito njira “yopita” osati njira “yobwera” ya Chipangano Chakale mu nthawi ya Israyeli.

Mu nthawi ya Chipangano Chakale mitundu ya anthu imayenera kubwera kwa Israyeli kudzalandira vumbulutso la Mulungu. Koma mu Chipangano Chatsopano lamulo ndi lakuti “pitani kudziko lonse lapansi.” Mu Chipangano Chatsopano okhulupirira amatsatira njira imeneyi. samangokhala pansu kudikirira anthu kuti awapeza kumene iwo akukhala.

## **WOKHULUPIRIRA ALIYENSE ACHULUKITSE”**

Wokhulupirira aliyense wa mpingo woyamba amachuluka pobweretsa okhulupirira atsopano:

### **Pamenepo ndipo iwo akubalalitsidwa anapitapita nalalikira mauwo (Machitidwe 8:4)**

Mpingo ukuyenera kutumiza anthu (MUN ndi akazi) mmagawo onse a moyo. Anthu amene amakhala ndi mwa chikhulupiro osti kumangoyankhula. Anthu amene miyoyo yawo inasintha ndi uthenga wabwino. Msilikali sapambana ku nkondo pamene wangokhala ku malo amaphunziro. Wokolola sangokhala mu nkhoke ndipo nsodzi sangokhala kumtunda kumadikira.

## **MAUBALE A ANTHU:**

Mu nthawi ya Chipangano Chatsopano uthenga wabwino unafala mwamsanga mmalo amene anthu anali pa ubale wa mbanja, ndi anzawo. Mwachitsanzo, Yesu anaitana Andreyu kuti amtsate. Mwamsanga Andreyu anayamba kugawana uthenga wabwino kwa apabanja ake. Ndipo anambweretsera Petro kwa Yesu.

Werengani ndimezi zimene zikuonetsera za mmene uthenga unafalikira pakati pa maubale a anthu:

- Zakeyu ndi banja lake: Luka 19
- Banja la mkulu wa ku Kapanawo: Yohane 4:53
- Abale ndi abwenzi a Koneliyo: Machitidwe 10:24,44
- Anthu awiri mnyumba ya Filipo: Machitidwe 16:15 ndi 27-34
- Banja la atsogoleri a Sunagoge: Machitidwe 18:8
- Stefano ndi a mnyumba mwake: I Akorinto 1:16
- Amnyumba mwa of Aristobulo ndi Nakiso: Romans 16:10-11
- Onesifolo ndi banja lake: II Timoteo 1:16
- Filemoni ndi banja lake: Filemoni 1

## **NJIRA ZA YESU**



Mu buku lonse la Machitidwe, mpingo woyamba unagwiritsa ntchito njira zimene Yesu anaphunzitsa ndi kuonetsera. Analalikira uthenga, kuphunzitsa mau, kubatiza atsopano, ndi kuphunzitsa ophunzira (Mateyu 28:19-20).

Pemphero ndi kuwerenga Mau zinali zofunika kwambiri pa kukula kwa mpingo mu chiwerengero (Machitidwe 6:4).

Kuphatikiza Mau a Mulungu ndi kuonetsera mphamvu zinachulukitsanso mpingo. Pamene anthu amachiritsidwa, zozizwa zimachitikanso, ziwanda zimathawa ndipo ambiri amabwera kwa Ambuye.

(Kuonetsera mphamvu kunali kofunika moti a Harvestime International Institute ali ndi phunziro lotchedwa “*Mfundo Zamphamvu*”).

### **MAGULU A CHIPANGANO CHATSOPANO:**

Magulu anali ofunika mu Chipangano Chatsopano pa kukula mu chiwerengero. Mu Machitidwe 6:1-7 pamene vuto labwera, gulu lapadera linapangidwa kuthetsa vutoli. Paulo anaphunzitsa zagulu lapadera la ophunzira pa sukulu ya mdera (Machitidwe 19:9). Mwanthawi, Paulo amaphunzitsa gulu lapadera la Ayuda ndi a mitundu (Machitidwe 13:42). Magulu ochepa amakumana mnyumba (Machitidwe 12).

Mipingo yambiri yapanga dongosolo la anthu amumpingo mwawo kuhkala magulu a ang’ono kuti akwaniritse cholinga chimene sichingakwaniritsidwe ndi bwino ndi mikumano yaikulu ya mpingo wonse. Magulu ang’ono amakhala pa ubale, oyendayenda ndi omasuka kutumikira zosowa za anthu.

### **UTUMIKI WA MZIMU WOYERA:**

Mzimu Woyera ndi mphamvu imene imatsutsa anthu ochimwa ndi kuwakopa kuti alandire uthenga wabwino. Zotsatira za izi ndi kukhala ndi okhulupirira atsopano amene amakulitsa mpingo.

**Ndipo atadza Iyeyo, adzatsutsa dziko lapansi za macimo, ndi za cilungamo, ndi za ciweruziro;**

**za macimo, cifukwa sakhulupirira Ine;**

**za cilungamo, cifukwa ndinka kwa Atate, ndipo simundionanso; 11za ciweruziro, cifukwa mkuru wa dziko ili lapansi waweruzidwa (Yohane 16:8-11).**

## **MPHATSO ZA MZIMU:**

Kukula kwa munthu kumafuna kukula kwa gawo lolimba pofuna kulimbisa ndi kuthandiza kuchulukana nkwa ma selo. Kuti thupi la Khristu likule, gawolinso ndi lofunika. Yesu ananena kuti zokolola zapsa, koma ogwira ntchito ochepa. Ngati ogwira ntchito achepa, ndiye kuti tigwirizane kuti ticolole zokolola.

Pa cholinga ichi, Mzimu Woyera amapereka mphatso ndi mautumiki osiyana mu mpingo ndi cholinga chogwira ntchito ya utumiki. Mphatso za Mzimu ndi kuthekera kwa uzimu kopatsidwa ndi Mzimu Woyera kopangitsa ntchito ya utumiki. Mukhoza kuwerenga mavesi awa:

**Aroma 12:1-8, I Akorinto 12:1-31, Aefeso 4:1-16, I Petro 4:7-11**

Mulungu ali ndi malo mu mpingo amene ali wokhulupirira:

**Koma tsopano, Mulungu anaika ziwalo zonsezo m'thupi, monga anafuna (I Akorinto 12:18)**

Membala aliyense ali ndi malo amene Mulungu anamusankhira. Amapatsidwa mphamvu kuti akwaniritse cholinga mu mpingo kudzera mu mphatso za Mzimu Woyera. Pamene okhulupirira akupezeka pa malo amene Mulungu wamusankhira ndi kuyamba kugwiritsa mphatso yake, mpingo umayamba kuyenda bwino. Mulungu amaufanizira ngati mmene thupi la munthu limagwirira ntchito pamene chiwalo chilichonse chimachita ntchito yake. (I Akorinto 12:1-31).

Munthu aliyense ndi wofunika pa ntchito ya utumiki, monganso mmene lilili thupi lathu:

**Ndipo dise silingathe kunena kwa dzanja, Sindikufuna iwe, kapenanso mutu kwa mapazi, Sindikufunani inu. 22Koma makamakatu ziwalo zoyesedwa zofoka m'thupi, zifunika (I Akorinto 12:21-22).**

Harvestime International Institute mu phunziro lawo amalitcha “*Utumiki wa Mzimu Woyera*” limapereka tsatanetsatane wa mphatso za uzimu. Pa chifukwa ichi, chidule chokha chaperekedwa:

### **Mphatso zapadera za utsogoleri:**

Pali ma udindo a utsogoleri amene Mulungu amawaika ndi kuwasankha ena mu mpingo:

**Ndipo Iye anapatsa ena akhale atumwi; ndi enaaneneri; ndi ena alaliki; ndi ena abusa, ndi ena aphunzitsi (Aefeso 4:11)**

Atsogoleri apadera operekedwa ndi Mulungu ndi monga:

### **Atumwi:**

Mtumwi ndi amene ali ndi kuthekera kwapadera kutukula mpingo watsopano mmadera komanso mu zikhalidwe osiyanasiyana ndipo amayang'anira mipingo ngati woyang'anira. Mtumwi ndiye kuti “wotumidwa” amene watumidwa ndi mphamvu yonse komanso ulamuliro wochita mmalo mwa wina.” Mtumwi ali ndi ulamuliro wapadera kapena kuthekera kofalisa uthenga wabwino kumadera ambiri ku dziko lapansi popanga okhulupirira. Masiku ano mpingo ukuwatchula atumwi ngati wodzala mipingo.

### **Aneneri:**

Pali magawo awiri a uneneri. Loyamba ndi mphatso yapadera yokhala mneneri. Ina ndi mphatso yolankhula uneneri. Mwachidule, uneneri ndi kulankhula pansu pa kuuzilidwa ndi Mulungu. Ndi kuthekera kwapadera kolandira ndi kulankhula uthenga wa Mulungu kwa anthu ake. Munthu amene ali mneneri ali ndi mphatso ya utsogoleri yapadera ya uneneri komanso mphatso yolankhula uneneri.

### **Alaliki:**

Mlaliki ali ndi kuthekera kwa kogawana ndi uthenga wabwino ndi anthu osakhulupirira ndi cholinga kuti anthuwa akhale mu thupi la Yesu. Tanthauzo la “mlaliki” ndi amene amagawa uthenga wabwino.

### **Abusa:**

Abusa ndi atsogoleri amene amakhala nthawi yaitali yoyang'anira moyo wa uzimu wa gulu la okhulupirira.

### **Aphunzitsi:**

Aphunzitsi ali ndi kuthekera kolankhula Mau a Mulungu cholinga choti adziwitse anthu ndi kugwiritsa ntchito zimene aphunzirazo. Mphunzitsi ndi amene ali ndi mphatso yophunzitsa komanso amakhala atsogoleri a mu mpingo.

Mphatso zisanu za utsogolerizi zimagwira ntchito pamodzi ndi cholinga chokulitsa mpingo. Atumwi amakulitsa mpingo polalikira uthenga wabwino ku madera osiyanasiyana ndi kukhala ndi okhulupirira atsopano. Mulungu amachita zozizwa ndi zodabwitsa pofuna kuthandiza kukula kwa uthenga wabwino. Atumwi amapereka utsogoleri wapadera ku mpingo umene awudzutsa.

Udindo wenweni wa iwo amene ali ndi mphatso ndi kuthandiza okhulupirira ena kuzindikira ndi kugwiritsa ntchito mphatso zawo za uzimu (Aefeso 4:11-16). Ntchito ya utumiki imafuna kuchitachita kwa onse. Pamene thupi la Khristu siligwira ntchito moyenera, mamembala ofooka amatengedwa ndi mosavuta ndi ziphunzitsa zonama (Aefeso 4:14).

Ichi ndi chidule cha mphatso za uzimu zopatsidwa kwa okhulupirira:

### **Mphatso zolankhula:**

Mphatso izi zimatchedwa “zolankhula” chifukwa zimakhudza kulankhula momveka (mokweza). Mphatsozi ndi monga uneneri, kuphunzitsa, chilimbikitso, mawu a nzeru (kuthekera kolandira chidziwitso cha mmene zinthu zikhalire), mawu a chidziwitso (kuthekera komvetsa zinthu zimene ena sadziwa ndipo sangamvetse ngakhale kutha kugawira kwa ena.

### **Mphatso zotumikira:**

Mphatso izi zimatumikira mpingo pothandiza ndondomeko, dongosolo ndi chithandizo cha ku uzimu kapena kuthupi.

Kutumira: kuthekera kogwira ntchito ya Ambuye, kumasula ena ndi zina.

Thandizo: kuthandiza ena mu ntchito za Ambuye powachulukitsa kuti azichita bwino.

Utsogoleri: kuthekera kokhala ndi zolinga zogwirizana ndi Mulungu ndi kuuza ena za izi. Munthu amene ali ndi mphatso imeneyi amalimbikitsa ndi kutsogolera ena kuwaniritsa cholinga cha Mulungu ku ulemmero wa dzina lake.

Dongosolo: mphatsoyi imatchedwa “maboma” Mbaibulo. Munthu amene ali ndi mphatsoyi amakhala ndi kuthekera kotsogolera, kulongosola, ndi kupanga ziganizo mmalo mwa ena.

Kupereka: kuthekera kwapadera kopereka zinthu, ndalama, nthawi, mphamvu ndi luso ku ntchito ya Mulungu.

Kuonetsa chifundo: chifundo chapadera ndi kuthekera kothandiza iwo akuvutika.

Kuzindikira mizimi: kuthekera kokhalandi kawuniwuni wa anthu, ziphunzitsa ndi nyengo ndi kutsimikiza ngati zikuchokera kwa Mulungu kapena Satana.

Chikhulupiriro: munthu wa chikhulupiriro amakhala ndi kuthekera kokhulupirira zinthu pa kulimba mtima ndi kudalira Mulungu mu nyengo zovuta.

Kuchereza alendo: kuthekera kopereka chakudya ndi malo ndi zinthu zina kwa iwo amene ali ndi zosowa.

### **Mphatso za zozizwa:**

Izi ndi zozizwa za umulungu za mphamvu ya Mulungu kudzera mwa okhulupirira pofuna kuwaniritsa Mau a Mulungu.

Malilime: kuthekera kolandira ndi kulankhula uthenga wa Mulungu kupita kwa anthu mwa ziyankhulo zachilendo.

Kumasulira: kuthekera kodziwitsa uthenga mu chilankhulo chomveka cha amene alankhula ndi malilime ena.

Zozizwa: kudzera mwa munthu amene ali ndi mphatso ya kuchita zodabwitsa za Mulungu amachita mwamphamvu ya Mulungu kuposa ya chilengedwe.

Machiritso: munthu ameneyi amakhala ndi kuthekera kolola mphamvu ya Mulungu kuwombola moyo posagwiritsa ntchito njira zachilengedwe.

## **MAUTSOGOLERI ENA A MBAIBULO**

Okhulupirira amene ali ndi mphatso zapadera si omwewa amene ali ndi utsogoleri mu Mbaibulo kuti atumikire mu mpingo. Palinso ma udindi ena monga akulu a mpingo, oyanga'anira amene akupezeka mu Chipangano Chatsopano. Maudindo amenewa ndi ofunikiranso pa kukula kwa mpingo.

Maudindo amenewa ndi osiyana ndi mphatso za utsogoleri zimene mwaphunzira. Awa ndi maudindo apadera amene anakhazikitsidwa ndi mpingo wakale othandizira kukula kwa mpingo mu chiwerengero. Mukhoza kuwerenga Machitidwe 6:1-7 za mmene analili mu mpingo woyamba.

Zimene mpingo wakale umachita zinali cholinga cha Mulungu kuti zikhale chitsanzo chatu. Maudindowa akhoza kugwiranso ntchito lero lino. Cholinga cha maudindo amenewa ndi kuthandiza iwo amene ali ndi mautumiki a mphatso zapadera monga za atumwi, aneneri, alaliki, abusa ndi aphunzitsi.

Dziwani: mawu oti “akulu a mpingo” anayamba kugwiritsidwa ntchito mu Eksodo 3:16 pofuna kunena za Israyeli. Pali mavesi ambiri amakamba za akulu a Israyeli mu Baibulo. Akuluwa ndi osiyana ndi amene anali ndi utsogoleri wa mpingo woyamba.

## **ZOWAYENEREZA A BISHOPO NDI AKULU A MPINGO**

Werengani mavesi ndipo phunzirani zina mwa zinthu zimene atumiki akuyenera kukhala:

I Timoteo 3:2-12, Tito 1:6-9 ndi Aroma 16:2

## MAYESO ODZIYETSA NOKHA

1. Lembani Vesi Lotsogolera kuchokera pamtima.

---

---

---

2. Kodi chimachitika ndi chiyani pamene mpingo ukukula mu chiwerengero?

---

---

---

3. Lembani chidule cha mmene mpingo woyamba unakulira ku Yerusalemu.

---

---

---

---

4. Pansipa pali njira za kukula kwa mpingo mu Chipangano Chatsopano. Lembani mwachidule pa pepala lina za mmene zinagwirira ntchito kuti mpingo ukule ku Yerusalemu.

- Masomphenya a uzimu
- Nthawi ndi malo amene uthenga wabwino umalandilidwa
- "Pitani" osati "bwerani" ngati njira
- Okhulupirira aliyense achulukane
- Maubale
- Njira za Yesu
- Magulu
- Khomu lililonse
- Utumiki wa Mzimu Woyera
- Mphatso ndi maudindo a uzimu

(Mayankho a mafunsowa akupezeka kumapeto kwenikweni kwa bukuli).

## KUPITILIZA KUPHUNZIRA

1. Pa nkhani ya kukula kwa mpingo mu chiwerengero pali zinthu zitatu zofunika. Mzimu wa Mulungu (Machitidwe 1-11, Mau a Mulungu (Machitidwe 12:20) ndi munthu wa Mulungu (Machitidwe 21-28).
2. Magulu a padera a uthumi anali amodzi amene amene anabweretsa kukula kwa mpingo wakale. Awa ndi ena mwa magulu a padera a utumiki amene mukhoza kumawapempherera mu mpingo mwanu:
  - Kuphunzitsa obadwa mwatsopano
  - Akazi atsopano ndi oyembekezera
  - Ana
  - Achinyamata
  - Achikulire
  - Mabanja atsopano
  - Osakwatiwa / osakwatira
  - Utumiki wa iwo amene ali mu msinga za mowa, fodya, mankhwala ozunguza bongo.
  - Utumiki wa abambo
  - Utumiki wa amayi
  - Amasiye, osiidwa banja
  - Olumala
3. Magulu onse amene ali mu mpingo amafuna mtsogoleri. Onetsetsani kuti mtsogoleri amene akutsogolera ali ndi zomuyenerereza kukhala mtsogoleri molingana ndi Baibulo.
4. Kafukufuku wa kukula kwa mpingo anachitika ku Amerika ndipo anapeza zinthu zimene zimakuluitsa mpingo mu chiwerengero. Zina mwa izo ndi izi:

Utsogoleri wa uzimu wamphamvu  
Ulaliki wa kathithi  
Kuonetsera mphamvu za Mzimu woyera  
Maziko a chuma amphamvu  
Mphatso ndi zipatso za Mzimu  
Pemphero  
Mautumiki osiyanasiyana  
Kugwiritsa ntchito Baibulo  
Kukamba za Yesu yekha basi.

## CHAPUTALA CHA 8

### KUKULA MMADERA

#### ZOLINGA:

Pakutha pa chaputalachi muyenera:

- Kulemba Vesi Lotsogolera kuchokera pamtima.
- Kupereka tanthauzo la “kukula mmadera”
- Kupereka tanthauzo la “kudzala mpingo”
- Kuomba mkota pa kukula mmadera kwa mpingo wa chipangano chatsopano.
- Longosolani za mmene mpingo umachulukira kudzera mmadera.
- Kudziwa njira zinayi zimene mpingo ungayambire
- Kudziwa mitundu itatu ya kukula mmadera kwa mpingo.
- Lembani zimene Baibulo limafuna posankha madera amene mungadzaleko mipingo
- Longosolani uthenga umene ungayambitse mpingo.

#### VESI LOTSOGOLERA:

**Kotero Mipingoyo inalimbikitsidwa m'cikhulupiriro, nacuruka m'ciwerengo cao tsiku ndi tsiku (Machitidwe 16:5)**

### MAWU OYAMBA

Ophunzira analamulidwa ndi Yesu kuti akhale mboni ku Yerusalemu, Yudeya, Samariya ndi malekedzero a dziko lapansi (Machitidwe 1:8).

Monga mwaphunzira chaputala changothachi, mpingo wa ku Yerusalemu unachuluka kwambiri. Gawo lina mu dongosolo la Mulungu linali kukulitsa mmadera. Mpingo wa ku Yerusalemu unayenera kuyambitsa mipingo ina mu mizinda ya Ayuda.

### KUKULA MMADERA

Kukula mmadera kumayamba pamene mpingo wayambitsa mpingo wina mu dera la anthu a chikhalidwe chofanana. Mpingo watsopanowo umakhala wina wochokera ku mpingo “waukulu” monga ngati mwana akakhala ndi makolo ake mdzikoli.

Ngati mpingo “waukuluwo” uli wokhwima mu uzimu, mpingo watsopanowo udzakulanso momwemo. Ngati pali mavuto mu mpingo “waukulu” mpingo watsopanowo udzakhalanso ndi ndi mavutowo. Izi ndi chifukwa chake mkofunika kwa mpingo kuti uyambe wakula mkati usanayambe kuganiza zoyambitsa mpingo kwina.

Mawu oti “Kudzala mpingo” ndi mawu amene timagwiritsa nchito pokamba za kukula mmadera ndi kubweretsa kukula kwa mpingo. Mawuwa amagwiritsidwa ntchito chifukwa mmodzi



“amadzala” mpingo watsopano ngati mlimi adzala mbewu munthaka. Mu dothi la nthaka, mbewu idzakula ngati yatsopano monga ngati “makolo” amene mbewuyo inachokera.

Mawu oti “kudzala” amafunika chifukwa sizikwanira pa “kulongosola” mpingo umene suyenera mu chikhalidwe cha anthu. Sizikwanira “kungoyambitsa” mpingo mkuwusiya kuti uzivutika. Umayenera “kudzalidwa” zimene zikutanthauza kuti umaikizidwa, kukulitsidwa ndi kupitilira moyo wa uzimu.

## **KUKULA KWA MPINGO MMADERA MCHIPANGANO CHATSOPANO**

Kuchuluka kumachitika pogawana. Ndipo kugawana ndi njira yoyamba yofunika imene Mulungu amachulukitsira. Ngati mwadala sitikusankha kugawana ndi kuchulukana, Mulungu adzalola zinthu zina zipangise. Machitidwe 8 amakamba za chizunzo chachikulu pa okhulupirira ku Yerusalemu. Chizunzochi chinabweretsa kugawana ku mpingo wa ku Yerusalemu pakuti anthu anathawa kupita ku mizinda ina.

Pamene anthu amathawa ku Yerusalemu, “kumene amapitako amalalikira Mau” (Machitidwe 8:4). Obadwa mwatsopano amapezeka ndipo mipingo yatsopano imadzalidwa. Mipingo imrneyi imakulitsa mpingo “waukulu” wa ku Yerusalemu.

Mpingo wa Chipangano Chatsopano sunakule mmadera podzala mipingo ina yokha ayi, komanso unalumikiza danga loyambitsa mipingo yambiri mu madera ena. Muphunzira izi mu phunziro la “kukula kwa mpingo kolumikiza maiko” mu chaputala chikubwerachi. Mbiri ya kukula kwa mpingo mmadera mu buku la Machitidwe inayamba ku Yerusalemu, Yudeya, Galileya, Ludda, Sarone ndi Ku Yopa. Awa anali madera a chikhalidwe cha Ayuda. Si munthu wokhulupirira payekha amene akachuluka ku uzimu, koma mipingo inachulukanso mu chiwerengero pamene mpingo wa ku Yerusalemu umakula pochitira umboni mderalo...Machitidwe 16:5

## **MMENE MIPINGO INAKULIRA MMADERA**

Pali njira zimene mpingo watsopano umayambira:

1. Mpingo wina umayambitsa mpingo umzake.
2. Mipingo kugwirizana kuyambitsa mpingo wina.
3. Mpingo waukulu kugawana kupanga mipingo iwiri kapena yoposera apo.
4. Wokhulupirira mmodzi akhoza kukuyambitsa mpingo. Amene ali ndi mphatso ya uzimu ya utumwi angatero mosavuta. Munthu ameneyi nthawi zina amatchedwa “wodzala mpingo.”

Muzonse izi, kuchulukana kumachitika kudzera mu kufalisa uthenga pokhala ndi okhulupirira atsopano.

## **MITUNDU YA KUKULA KWA MPINGO MMADERA**

Mipingo yatsopano imakhala ndi makulidwe osiyana a mmadera:

### **1. MIPINGO KUMATUMIKIRA KU MADERA:**

Iyi ndi mipingo yokhazikitsidwa ndi cholinga chotumikira ku madera, mmidzi, kapena mu mzinda. Izi zikhoza kukhala zotsatira za ulaliki umene waitana gulu la anthu okhulupirira mdera. Ikhoza kukhazikitsidwa kuti itumikire anthu amene sanafikilidwe ndi uthenga kapena ku malo kumene uthenga sulandilidwa.

### **2. MIPINGO YOTUMIKIRA KU MAGULU A MITUNDU YA ANTHU:**

Chiyanjano cha mautumiki awa amtumikira ku magulu a anthu amene ali ndi zikhaliidwe, ziyankhulo komanso mitundu yofanana. Mwachitsanzo mpingo ukhoza kuyamba kwa anthu amene amalankhula Spanish koma sangamve chingerezi ngati “chiyankhulo” chawo choyamba.

### **3. MIPINGO YOKHALA NDI CHOLINGA CHAPADERADERA:**

Mpingo ukhoza kukhazikitsidwa ndi cholinga chapedera: Mwachitsanzo, mpingo ukhoza kudzalidwe kufupi ndi malo amene ophunzira amachitirako maphunziro kuti azitumikira ophunzira.

### **ZOFUNIKA TIKAMAYAMBA KUKULITSA MPINGO MMADERA**

Baibulo limaphunzitsa zinthu zimene ndi zofunikira pokulitsa mpingo polalikira uthenga wabwino pamene tikufuna kukhazikitsa mipingo. Zofunikirazo ndi izi:

#### **OSAFIKILIDWA:**

Chinthu choyambirira ndi anthu osafikilidwa. Paulo anati:

**Pakuti, amene ali yense adzaitana pa dzina la Ambuye adzapulumuka.**

**Ndipo iwo adzaitana bwanji pa iye amene sanamkhulupirira? ndipo adzakhulupirira bwanji iye amene sanamva za iye? ndipo adzamva bwanji wopanda wolalikira (Aroma 10:13-14)**

Kumalo kumene kulibe umboni wa uthenga wabwino kukuyeneran kukhala koyamba. Werengani fanizo la nkhoa mu Luka 15:3-7. Chinthu choyamba chinali pa nkhoa yotaika, osati pa zomwe zinali nkhoa.

#### **OLANDIRA:**

Mwaphunzira mu phunziro lotsiriza za kufumikira kwa kulalikira kwa munda wa uzimu umene uthenga umalandirika. Yesu anaphunzitsa mu Mateyu 10:13-15; Luka 8:5-15) ndi Paulo analankhulanso (Machitidwe 13:42-51). Yesu ndi Paulo sanakane za malo osalandilika. Anapitilira kulalikira uthenga kwa iwo ndikuchenjeza za chiwereuzo cha Mulungu. Koma anayambirira kwa anthu amene amalandira uthenga.

## **KUYAMBA MIZINDA, KENAKO MADERA A KUMUDZI:**

Iyi inali njira imene Paulo anagwiritsa ntchito imene muphunzira zambiri mukafika mu chaputala chikubwerachi. Mizinda ili ndi chiwerengero chambiri cha anthu. Anthu ambiri amapita ku kukachita malonda ku mizinda. Anapitilira kulalikira uthenga ndi kuchenjeza za chiwereuzo cha Mulungu. Pamene mukufikira anthu ambiri mi mizinda, iwowa amabwerera ku midzi kumakagawira anthu uthenga wabwino ndi kudzala mipingo yatsopano.

Kaya ndi zokhuza za kusintha kwa zikhalidwe, machitidwe a moyo, malamulo, kusintha kumeneku kumayamba ku mizinda kenako kumudzi. Pamene mwafikira mizinda ndi uthenga wabwino, umafalikira kumalo konse kwa deralo mpakana ku midzi.

## **UTHENGA**

Uthenga wa iwo amene amadzala mipingo ndi wakuti:

### **UTHENGA WA MBAIBULO:**

Mipingo yatsopano inabadwa chifukwa cha iwo amene sanatembenuke mtima atatha kumva uthenga wabwino ndi kulandira Yesu kukhala Mbuye ndi mpulumutsi wa moyo wawo. Pamene kulalikira kuli kochokera Mbaibulo, kumakhala ndi ulamuliro wa Mulungu. Omvera amadziwa ndi kuchitapo kanthu pa za mphamvu ya Mau a Mulungu.

### **WOKAMBA ZA MKRISTU:**

Yesu ndiye mwini wa uthenga umene umachulukitsa mipingo. Anthu akuyenera kudziwa Yesu ndi ndani, kufunikira kwa utumuki wake wa padziko lapansi, imfa yake, ndi kuuka kwake kwa akufa. Akuyenera kuphunzitsaidwa za mmene angachitire ndi kulandira uthenga wabwino wa chipulumutso ndi moyo wosatha.

### **UTHENGA WOKHAZIKIKA PA CHOSOWA:**

Anthu amachitapo kanthu pa uthenga umene ukukumana ndi chosowa chawo. Chitsanzo cha ichi ndi Yesu ndi mkazi pa chitsime (Yohane 4). Uthenga wake ukhakhazikika pa pa chosowa chake pa madzi akumwa.

### **MMENE TIGZDZALIRE MPINGO WATSOPANO:**

Maphunziro ambiri a Harvestime International Institute amakamba zambiri za mmene tingadzalire mpingo watsopano. Ngati mukuphunzira phunziroli la Harvestime Institute mu ndondomeko yawo, phunziro limene mukuphunzirali lili gawo limodzi la mapgunziro a Mfundo za Baibulo za kuchulukitsa.

Pofuna kudzala ndi kulongosola mipingo, mukuyenera kuphunzira maphunzirowa. Pakadali pano yambani kupemphera chitsogozo cha Mulungu cha kumene akufuna iye kuti mukule. Ngati muli

mbusa wa mpingo, musadwabwe pa nkhani yoti muchulukane. Mwaphunzira kale kuti kuchuluka ndi chifuniro cha Mulungu.

Pemphero lanu likhale pa kumene mukufuna kudzala mpingo watsopano ndi nthawi imene muchite chifukwa nthawi ndi malo ndi zofunika pa zokolola za uzimu. Mukuyenera kuchulukana ku malo oyenera komanso pa nthawi yabwino.

## **MIPINGO YATSOPANO IKUYENERA KUKULA**

Monga mwana akabadwa mdzikoli, mpingo watsopano ukuyenera kudalira “kholo” la mpingo pa kukula kwake. Koma pamene mpingo watsopano ukukula, ukuyenera kukhala osiyana, thupi la okhulupirira lochitachita, ndi kuthekera kwa kuchulukana ku uzimu pa kuberekana. Ichi ndi chitsanzo cha mipingo imene Paulo anadzala.

Mpingo wadera ukuyenera kukula kuchokera mu mfundo za Mmalemba zimene zimakamba za “Kukula kwa Mpingo mu chiwerengero.” Kutu ukule bwino mpingo uliwonse watsopano ukuyenera:

### **1. KUMVETSA CHOLINGA CHAKE:**

Madongosolo onse a mu mpingo akuyenera kugwirizana ndi zolinga za Mpingo. Harvestime International Institute ali ndi phunziro la “Dongosolo pa Zolinga” limene limalongosola izi mwatsatane.

### **2. KUMVETSA MFUNDO ZA MMBAIBULO ZA DONGOSOLO:**

Izi ndi monga mphatso za uzim ndi mautumiki a mumpingo ndi mpaphunziro a okhulupirira atsopano kuti akhala atsogoleri a ku uzimu otha kugwiritsa ntchito mphatso zawo. Harvestime International Institute ali ndi phunziro la “Dongosolo la Mfundo za Mbaibulo” ndi “Dongosolo pa Zolinga” amene adzakuthandizani pophunzira.

### **3. KUMVETSA ZOMUYENEREZA MTSOGOLERI ZA MBAIBULO:**

Harvestime International Institute ali ndi phunziro la “Dongosolo la Mfundo za Mbaibulo” limene lingakuthandizeni pa maphunziro anu.

### **4. KUPHUNZITSIDWA MAZIKO A CHIKHULUPIRIRO:**

Maphunziro a Harvestime mu bukhu la “Kukhala Wachiwiri” a Harvestime International Institute azakuthandizani kukwaniritsa zolinga zanu.

### **5. KHAZIKIKANI PA MAFUNSO ENIENI:**

Mafunsowa ali ndi zinthu monga:

- Kupanga chiphunzitso chimene alendo adzadziwa zikhulipiro zanu za mpingo za Mbaibulo.
- Malamulo amene boma limafuna pa za mpingo watsopano.
- Dongosolo la mpingo lokhuza utsogoleri, mautumiki, ndi ndondomeko za chuma cha mpingo.
- Malo ndi umwini wake wa katundu wa mpingo.
- Ubale wake wa “likulu” la mpingo ndi mipingo yatsopano.

## MAYESO ODZIYETSA NOKHA

1. Lembaini Vesi Lotsogera kuchokera pamtima.

---

---

2. Kodi kukula kwa mpingo “mmadera ndi chiyani?

---

---

3. Kodi “kudzala mpingo” kumatanthauza chiyani?

---

---

4. Lembani chidule cha kukula kwa mpingo woyamba mmadera ku Yerusalemu.

---

---

5. Lembani njira zinayi zimene mpingo watsopano ungayambire.

---

---

---

---

6. Lembani mitundu itatu ya kukula mmadera kwa mpingo.

---

---

7. Ndi mfundo ziti zoyamba zimene Baibulo limanena posankha madera oyambitsako mipingo?

---

---

8. Kodi ndi mtundu uti wa uthenga umene umayambitsa mpingo watsopano?

---

---

(Mayankho a mafunsowa akupezeka kumapeto kwenikweni kwa bukuli)

## KUPITILIZA KUPHUNZIRA

Popitiliza kuphunzira za mmene mungadzalire mpingo onani maphunziro awa a Harvestime International Institute:

*Dongosolo la mpingo la Mbaibulo* lidzakutsogolerani posankha ndi kupanga atsogoleri a mpingo.

*Kusanthula Malo* lidzakuthandizani kudziwa malo amene uthenga wabwino ungafikeko ndi kudzalako mpingo.

*Dongosolo la Zolinga* lidzakuphunzitsani kukhazikitsa cholinga, kupanda zochita ndi kulongosola mpingo.

*Ndondomeko Zolimbikitsa* zidzkuthandizani kulimbikitsa chiyanjano cha mpingo pa ulaliki.

*Chotupisa ngati Ulaliki* lidzabweretsa okhulupirira atsopano pa mpingo.

## CHAPUTALA CHA 9

### KUKULA POLUMIKIZA

#### ZOLINGA:

Pakutha pa chaputalachi muyenera:

- Kulemba Vesi Lotsogolera kuchokera pamtima.
- Kulongosola tanthauza la “kukula polumikiza” mipingo.
- Kupereka Vesi la Mbaibulo la dongosolo ma Mulungu la “kukula polumikiza” mipingo.
- Kudziwa Vesi Lotsogolera la mtsogoleri wa mu Chipangano Chatsopano pa nkhani ya “kukula polumikiza”
- Kulemba chidule cha njira zimene Paulo anagwiritsa ntchito pokulitsa uthenga wabwino mmadera a zikhalidwe zina.

#### VESI LOTSOGOLERA:

**... Kukawatsegulira maso ao, kuti atembenuke kucokera kumtima, kulinga kukuunika, ndi kucokera ulamuliro wa Satana kulinga kwa Mulungu, kuti alandire iwo cikhululukiro ca macimo, ndi colowa mwa iwo akuyeretsedwa ndi cikhulupiriro ca mwa Ine (Machitidwe 26:18)**

#### MAWU OTSOGOLERA

Chaputala chomwe mwamalizirachi chikukamba za kukula kwa mpingo mmadera kumene kumachitika podzala mipingo yatsopano mu madera ofanana chikhalidwe. Zikuyenera kukhala limodzi ndi phunziro la kukula kwa mpingo polumikiza.

Mfundo zomwezo zofunikira pa kukula kwa mpingo mmadera zikugwiranso ntchito pa kukula kwa mpingo polumikiza. Izi zikutanthauza kuti chilichonse chakambidwa mu phunziro lathali, ndi chofunikanso mu phunziro lino. Koma kukulitsa polumikiza kumafuna njira zina zimene ndi za chaputalachi basi.

#### KUKULA POLUMIKIZA

Kukula polumikiza kumachitika pamene mpingo uzikulitsa mmadera a dziko, chiyankhulo, malire a mitundu podzala mpingo watsopano mu zikhalidwe zatsopano za anthu. Mawu oti “kulumikiza” akugwiritsidwa ntchito chifukwa pamene ntchito ikuchitika “mlato” umaikidwa kuchokera ku chikhalidwe china kupita ku chikhalidwe china polafalitsa uthenga. Njira zatsopano za mayendedwe ndi zolumikizana zatukula kwambiri machitidwe a mpingo okula polumikiza ngakhale ku malo akutali.



## KUKULA KOLUMIKIZA MCHIPANGANO CHATSOPANO

Kukula kolumikiza madera kunali gawo limodzi la dongosolo la Ambuye Yesu pofuna kufalitsa uthenga wabwino mdziko lonse lapansi. Ophunzira amayenera kuyamba kuchitira umboni mmadera a zikhalidwe zawo ku Yerusalemu keneko kukula popita ku madera ena ofanana nawo zikhalidwe kukudzala mipingo.

Kenako, ophunzira amayenera kulumikiza maiko, zilankhulo ndi malire pofalisa uthenga wabwino mu zikhalidwe zosiyana ndi zawo monga Samariya ndi “malekezero onse a dziko lapansi” (Machitidwe 1:8). Ophunzira mwachangu anakwaniritsa lamuloli pochulukana pakati pa anthu a zikhalidwe zawo (Machitidwe 2).

Kukula ku madera ena a zikhalidwe zawo kunabwera chifukwa cha chizunzo:

**... Koma pamene atumwi a ku Yerusalemu anamva kuti Samariya adalandira mau a Mulungu, anawatumizira Petro ndi Yohane; (Machitidwe 8:14).**

Filipo koyamba analumikiza kusiyana kwa zikhalidwe pa chitsitsimutso cha ku Samariya pa Machitidwe 8. Petro ndi Yohane anapitiliza utumiki mu dera lomwelo.

Mtumwi Petro anali ndi vuto polandira ntchito yotumidwa wa anthu osiyana zikhalidwe. Anali mu Yuda wachipembedzo ndipo mwa kanthawi anali ndi malire polumikizana ndi Amitundu (anthu amene sanali Ayuda). Mulungu analankhula kwa Petro mmasomphenya pa Machitidwe 10 ndipo Petro anatengera uthenga wabwino kwa amitundu ku Kaesareya.

Kukula kolumikiza mu Chipangano Chatsopano kukuonetsedwa bwino ndi utumiki wa mtumwi Paulo. Mulungu akuitana Paulo ku utumiki umenewu. Paulo anali mu Yuda, koma Mulungu anamuuza kuti anali:

**Koma Ambuye anat kwa iye, Pita; pakuti iye ndiye cotengera canga cosankhika, cakunyamula dzina langa pamaso pa amitundu ndi mafumu ndi ana a Israyeli (Machitidwe 9:15).**

Chifukwa Paulo anaitanidwa ndi Mulungu pa utumiki wopita kwa anthu a zikhalidwe zina, njira zake ndi zofunika pofuna kumvetsetsa kukula kwa mpingo polumikiza. Werengani nkhani ya kutembenuka mtima kwa Paulo mu Machitidwe 9. Zina zonse za buku la Machitidwe ndi nkhani ya ntchito ya umishoni kwa mitundu ya dziko. Ambiri mwa mabuku a Chipangano chatsopano ndi makalata otsatira kwa mipingo imene anadzala mmadera osiyanasiyana (Aroma ndi Aheleni).

## NJIRA ZA MTUMWI PAULO

Paulo anasankhidwa ndi Mulungu ngati chitsanzo chathu:

**Komatu mwa ici anandicitira cifundo, kuti mwa ine, woyamba, Yesu Kristu akaonetsere kuleza mtima kwace konse kukhale citsanzo ca kwa iwo adzakhulupirira pa iye m'tsogolo kufikira moyo wosatha (I Timoteo 1:16).**

Ichi ndi chifukwa njira za Paulo zikhoza kukhala ngati chitsanzo pa kukula kwa mpingo polumikiza. Izi ndi zina mwa mfundo za kukula polumikiza mu utumiki wa Paulo:

### **CHOLINGA CHABWINO:**

Paulo amalimbikitsidwa ndi nyengo za amitundu zopanda Yesu (Amitundu ndiye kuti mitundu yonse imene si Israyeli).

**Momwemo kumbukirani, kuti kale inu amitundu m'thupi, ochedwa kusadulidwa ndi iwo ochedwa mdulidwe m'thupi, umene udacitika ndi manja; 12kuti nthawi ija munali opanda Kristu, alendo a padera ndi mbumba ya Israyeli, ndi alendo alibe kanthu ndi mapangano a malonjezano, opanda ciyembekezo, ndi opanda Mulungu m'dziko lapansi (Aefeso 2:11-12).**

Amaumilizidwa ndi chidwi cha lamulo:

**Ine ndiri wamangawa wa Ahelene ndi wa akunja, wa anzeru ndi wa opusa. 15Cotero, momwe ndingakhoze ine, ndirikufuna kulalikira Uthenga Wabwino kwa inunso a ku Roma (Aroma 1:14-15).**

Paulo amalimbikitsidwa ndi khumbo lomvera masomphenya opatsidwa ndi Mulungu:

**Potero, Mfumu Agripa, sindinakhala ine wosamvera masomphenya a Kumwamba (Machitidwe 26:16)**

Amalimbikitsidwa ndi changu ndi katundu wa pa Mulungu:

**Pamene Paulo analindira iwo pa Atene, anabvutidwa mtima pamene anaona mudzi wonse wadzala ndi mafano (Machitidwe 17:16)**

Amalimbikitsidwa ndi chikondi choyera:

**Koma m'zonse tidzitsimikfzira ife tokha monga atumiki a Mulungu, m'kupirira kwambiri, m'zisautso, m'zikakamizo, m'zopsinja**

**M'mayeredwe, m'cidziwitso, m'cilekerero, m'kukoma mtima, mwa Mzimu Woyera, m'cikondi cosanyenga (II Akorinto 6:4,6)**

### **ZOFUKIKA KOYAMBIRIRA:**

Paulo anali ndi zinthu zofunikira. Zinthu zimene zinali phindu kwa iye... maphunziro, katundu, chuma, maudio, ndi zina... anaziyesa zopanda kanthu ku uzimu. Chokhacho chimene chinampindulira kwa Yesu chinali choyambirira:

**Komatu zonse zimene zinandipindulira, zomwezo ndinaziyesa citayiko cifukwa ca Kristu.**

**Komatu zeni zeninso ndiyesa zonse zikhale citayiko cifukwa ca mapambanidwe a cizindikiritso ca Kristu Yesu Ambuye wanga, cifukwa ca Iyeyu ndinatayikitsa zinthu zonse, ndipo ndiziyesa zapadzala, kuti ndikadzionjezere Kristu (Afilipi 3:7-8)**

Zinthu zanu zofunikira zikuyenera kukhala:

1. Ubale wanu ndi Mulungu.
2. Ubale wanu ku thupi la Khristu (kuphatikizapo banja lanu ngati gawo la thupilo).
3. Utumiki wanu kwa Mulungu.

Ubale umabwera pambuyo pa utumiki pa zifukwa ziwiri:

1. Simungatumikire pamene ubale wanu siuli bwino ndi Mulungu.
2. Simungatumikire pamene ubale wanu siuli bwino ndi anthu ena. Ziwalo za thupi la Khristu (kuphatikizapo banja lanu) sizingalandire utumiki wanu pamene ubale wanu ndi ena siuli bwino.

#### **MAWU A MULUNGU:**

Utumiki wa Paulo unakhazikika pa Mau a Mulungu. Pamene Mau a Mulungu amafalikira ku zikhalidwe za anthu ena, mipingo imafalikira:

**Koma mau a Mulungu anakula, nacurukitsa (Machitidwe 12:24)**

**Cotero mau a Ambuye anacuruka mwamphamvu nalakika (Machitidwe 19:20)**

**Kotero Mipingoyo inalimbikitsidwa m'cikhulupiriro, nacuruka m'ciwerengo cao tsiku ndi tsiku (Machitidwe 16:5)**

#### **UTHENGA WA UTHENGA WABWINO:**

Uthenga wabwino wa Ufumu wa Mulungu wa Paulo. Sanasemphanitse ndi ntchito za za umishoni kwa maiko osowa ndi mphamvu ya kulalikira uthenga wabwino. Sanagwiritse ntchito machitidwe ake kuti akope anthu ambiri. Anthu amakhuzidwa ndi mphamvu ya Mulungu.

**Pakuti Uthenga Wabwino sundicititsa manyazi; pakuti uti mphamvu ya Mulungu yakupulumutsa munthu ali yense wakukhulupira; kuyambira Myuda, ndiponso Mhelene (Aroma 1:16).**

#### **PEMPHERO:**

Paulo anapempherera chitsogozo cha Mulungu polalikira uthenga wabwino kwa anthu a zikhalidwe zina:

**Ndipo pa kutumikira Ambuye iwowa, ndi kusala cakudya, Mzimu Woyera anati, Mundipatulire Ine Bamaba ndi Saulo ku nchito imene odinawaitanirako.**

**Pamenepo, m'mene adasala cakudya ndi kupemphera ndi kuika manja pa iwo, anawatumiza amuke (Machitidwe 13:2-3)**

### **MZIMU WOYERA:**

Mzimu Woyera anali mtsogoleri wa utumwi wa Paulo. Mwachitsanzo, mu nyengo ina...

**... atawaletsa Mzimu Woyera kuti asalalikire mau m'Asiya (Machitidwe 16:6)**

### **ULALIKI, CHIPHUNZITSO, KUCHITIRA UMBONI:**

Paulo anatsata malangizo a kutumwa kwakukulu kolalikira, kuphunzitsa ndi kuchitira umboni wa uthenga wabwino.

**Ndipo tsiku loyamba la sabata, posonkhana ife kunyema mkate, Paulo anawafotokozera mau, popeza anati acoke m'mawa mwace; ndipo ananena cinenere kufikira pakati pa usiku... (Machitidwe 20:7)**

**Kuti sindinakubisirani zinthu zopindulira, osazilalikira kwa inu, ndi kukuphunzitsani inu pabwalo ndi m'nyumba m'nyumba, ndi kucitira umboni Ayuda ndi Ahelene wa kutembenuza mtima kulinga kwa Mulungu, ndi cikhulupiro colinga kwa Ambuye wathu Yesu Kristu (Machitidwe 20:20-21).**

Sizokwanira kulumikizana mu uthenga wabwino okha. Unthenga ukuyenera kuperekedwa mu njira imene ingamveke kwa anthu omvera. Mawu, chilankhulo, machitidwe ena ofalisira akuyenera kusinthidwa ndi cholinga chakuti uthenga umveke. Paulo anazindikira ndi kuchita izi (onani Machitidwe 21:37-40 ndi 22:2). Ndipo 26:18 amapereka njira imene kulumikizana kwamphamvu kungachitikire palalikira uthenga wabwino kw anthu ndi zikhalidwe zina. Mulungu anatuma Paulo kwa amitundu...

**...Kukawatsegulira maso ao, kuti atembenuke kucokera kumdima, kulinga kukuunika, ndi kucokera ulamuliro wa Satana kulinga kwa Mulungu, kuti alandire iwo cikhululukiro ca macimo, ndi colowa mwa iwo akuyeretsewa ndi cikhulupiro ca mwa Ine (Machitidwe 26:18).**

Uthenga ukuyenera kuperekedwa mu njira yotha:

1. Kutsekula maso a anthu.

2. Kuti atuluke mu mdima wa uzimu kulowa mu kuunika.
3. Kuti achoke ku mphamvu ya Satana mkupita kwa Mulungu.
4. Kuti alandire chikhululukiro cha machimo awo polandira chipulumutso.
5. Kuti alandire cholowa cha uzimu mwa chiyeretso cha chikhulupiriro.

Chikhalidwe chimene munthu wakhalamo chimalosera zinthu zisanu mmadera awa:

Chilankhulo chake: mmene amalankhulira ndi kulumikizana maganizo ake.

Maonedwe ake a dziko: mmene amalionera ndi kulimvetsa dzikoli.

Zikhulupiriro zake: chipembedzo mu za mphamvu za uzimu, njira ndi maganizo ake.

Zimene amayendera: makhalidwe ake ndi anthu ena, zilimbikitso ndi njira za mmene amapangira ziganizo.

Makhalidwe ake: mmene amachitira, amakhalira, makhalidwe a zikhalidwe zawo zoyenera.

Machitidwe 26:18 amakambapo za izi, mukhoza kuwerenga. Pali nkhani ya chiyanikhulo, maonedwe a dziko, zikhulupiriro ndi kusintha kwa makhalidwe.

## **KUONETSERA MPHAMVU**

Paulo sanangolankhula za uthenga wabwino ayi, komanso amaonetsera mphamvu ya Mulungu:

**Mu mphamvu ya zizindikilo ndi zozizwitsa, mu mphamvu ya Mzimu Woyera; koteru kuti ine kuyambira ku Yerusalemu ndi kuzungulirako kufikira ku Iluriko, ndinakwanitsa Uthenga Wabwino wa Kristu (Aroma 15:19)**

## **KUDZALA MIPINGO:**

Paulo sanangofalitsa uthenga wabwino keneko ndi kuwasiya okha obadwa mwatsopano. Amapanga gulu la okhulupirira amene otembenuka mtima amakhala nawo. Amadzala mipingo mmadera.

1. Ogwira ntchito atumidwa: Machitidwe 13:1-4; 15:39-40

Ogwira ntchito amaphunzitsaidwa ndi kutumidwa kukafika mmadera ena. Okhulupirira a mmipingo ya pakhomu amathandiza, kutuma, ndi kuyanjana ndi iwo amene Mulungu anawapatulira ku ntchito.

2. Anthu analumikizana: Machitidwe 13:14-16; 14:1; 16:13-15

Mmadera ambiri, Paulo anayetsesa kulumikizana ndi atsogoleri a mu sunagoge. Anayesera kukhala ndi chidziwitso ndi thandizo la atsogoleri a pamalo. Magulu komanso anthu anatsata zolinga zokhala ndi gulu la anthu ambiri omvera uthenga wabwino.

3. Uthenga unaperekedwa: Machitidwe 13:17; 16:31

Uthenga unaperekedwa mu ulaliki, chiphunzitso, kuchitira umboni ndi kuonetsera mphamvu ya Mulungu. Njira zosiyana zinagwira ntchito molingana ndi mmene zinalili pofuna kulupereka uthenga kwa anthu. Mmadera ena amalalikira mu sunagoge (Machitidwe 14:1). Pomwe ena, anthu amene amalandira amaikidwa mmagulu ena apadera (Machitidwe 19:9). Mautumiki osiyana kwa anthu amachitika mmadera ena (Machitidwe 13:42) ndipo chilankhulo chimasinthidwa ponetsetsa kuti uthenga ukuperekedwa moyenera (Machitidwe 22:2).

4. Omvera amatembenuka: Machitidwe 13:48; 16:14-15

Kulumikizana bwino kwa uthenga wabwino kunachokera mu kutembenuka, ndi anthu amene amalandira uthenga wa chipulumutso ndi kulapa kwa machimo awo.

5. Okhulupirira anasonkhana: Machitidwe 13:43

Paulo sanasite ulaliki ndi kutembenuza anthu. Amawasonkhanitsa okhulupirira kukhala pa mpingo wad era. Okhulupirirawa amakhala mu thupi la chiyanjano ndi mwambo wa mpingo. Nthawi komanso malo zimayikidwa zoti azisonkhana pamodzi ngati mpingo.

6. Chikhulupiriro chitsimikizidwa: Machitidwe 14:21, 22; 15:41

Monga zaonetsedwa pa kutuma kwakukulu mu Machitidwe 28:19-20, chiphunzitso chimatsatira kutembenuka mtima. Chiphunzitso ichi, molingana ndi mpingo chinaumba okhulupirirawa pa maziko a moyo wawo wa chikhristu mu ufumu wa Mulungu. Zokhuza “chitsimikizo cha chikhulupiriro” zimalimbikitsa kukula mmoyo wauzimu, ndi kuthandiza okhulupirira kuzindikira mphatso zawo za uzimu ndi kukhala ziwalo zamphamvu mu thupi la Khristu.

7. Atsogoleri apatulidwa: Machitidwe 14:23

Ngati okhulupirira okhwima, atsogoleri omwe akulitsidwa ndi Mulungu amayenerezedwa pa utumiki wotsogolera mu mpingo. Akukuakulu anasankhidwa ku mpingo womwe amasonkhana osti kutumizidwa kuchokra ku mpingo wina kapena ku dziko lina. Mpingo uliwonse umakhala ndi madongosolo a kayendetsedwe ka mpingo kochokera Mbaibulo, kabwino ndi koyenera.

8. Mpingo unayamikiridwa: Machitidwe 14:23; 16:40

Pamene atsogoleri ali pamalo ndi kuyamba kugwira ntchito moyenera, kudalira “odzala mpingo” kumatha. Pakuti kusintha koyenera kunachitika kuchokera ku likulu la mpingo kupita ku mpingo watsopano. Mpingo “unayamikidwa” pochita bwino kwawo ngati thupi lokhulupirira.

9. Maubale anapitilira: Machitidwe 15:36; 18:23

Ubale unapitilira pakati pa okhulupirira ndi odzala mpingo (Paulo) ndi likulu la mpingo (Yerusalemu). Maubalewa amakhazikikanso pakati pa chiyanjano chatsopano cha iwo ndi mipingo ina mmadera ndi cholinga chofuna kufalitsa uthenga.

**MASOMPHENYA A DZIKO LONSE:**

Paulo anali ndi dongosolo la lenileni la machitidwe ake. Baibulo limaulula kuti anali ndi chidwi ku mAsiya, Galatiya, Makedoniya ndi ena amene anali ndi mmadera amenewo nthawi imeneyo:

Filipo: (Machitidwe 16) uwu unali mzinda wotsogolera ku Makedoniya.

Tesalonika: (Machitidwe 17:1-10) uwu unali waukulu ndi wachumua.

Akorinto: (Machitidwe 18:1-11) wa chuma wa Metulopolisi ku Helene.

Aefeso: (Machitidwe 19:1-10) kumene misewu yaikulu ya ufumu wa Chiroma unadutsa kummawa. Madoko komanso malo a malonda.

Paulo anadziwa kutiangathe kufikira anthu ambiri mu mizinda. Anadziwanso kuti kusintha kumayamba mu mzinda kenako ku malo akumudzi.

Mizinda ya malondayi ndi malo okopa alendo inali ndi anthu ambiri amalonda ndi zolinga zina. Moti alendo amamva nawo uthenga wabwino pamene amapita kwawo. Paulo anayendera mizinda mkukhazikitsa ntchito ua umishoni. Pamene amachoka ku Yerusalemu, anapita kudera lina ku Tarisi ndi Antiokeya. Werengani mavesi awa: Machitidwe 11:25-30; 13:1-3; 19:1-20; 16:8; 19:21; 23:11; 28:14-31. Aroma 1:9-15; 15:24, 28).

### **MALO OLANDILIKA:**

Njira za Paulo zokulitsa mpingo zinachitika chifukwa cha anthu amene amalandira uthenga wa Paulo. Ku Mateyu 10, Yesu anawauza ophunzira ake kuti asapite ku Samariya kapena kwa anthu a mitundu koma kwa Israyeli. Nthawiyi inali ya bwino koma kwa ana a Israyeli. Magulu ena a anthu sinali nthawi yawo yolandira uthenga.

Ngakhale pakati pa Ayuda, ophunzira amayenera kulalikira kwa iwo amene akanalandira uthenga. Amayenera kugawira iwo amene amalandira ndi kuchitabe choncho ngakhale amakumana ndi osalandira uthenga. Amayenera apereke mphamvu zawo kwa madera amene amalandira uthenga.

Paulo anatsata ndithu njira imeneyi. pamene ayuda amakana uthenga wabwino, Paulo amapita kwa amitundu (Machitidwe 13:42-51). Pamene Atene sanakonzeka, Paulo amapita Kwa Akorinto. Ndipo ku Akorinto Paulo anachoka kwa ayuda ndi amitundu. A Helene amene amalandira uthenga anakondwera ndikubatzidwa atakhulupirira (Machitidwe 18:5-11). Mulungu anavomereza ntchito ya Paulo mmasomphenya pomuza kuti akhalebe ku Akorinto opanda mantha ndi kulalikira Khristu (Machitidwe 18:5-11). Pamene mikumano ikuchitika mmasunagoge mkuamamukana iye, Paulo anayamba mipingo imene imalandira mauthenga ake. Pamene chizunzo chimamutulutsa kunja, amapita ku madera ena.

### **ANTHU AKE:**

Paulo amaika chidwi pofikira anthu a mtundu wake ndi uthenga wabwino:

**Abale, kufunitsa kwa mtima wanga ndi pemphero langa limene ndiwapempherera kwa Mulungu, ndilo, kuti apulumuke (Aroma 10:1).**

### **ANTHU OSAFIKILIDWA:**

Paulo anasankha madera amene uthenga wa Khristu sunafikeko:

**Ndipo coteru ndinaciyesa cinthu caulemu kulalikira Uthenga Wabwino, pa malopo Kristu asanachullidwe kale, kuti ndisamange nyumba pa maziko a munthu wina.**

**Koma monga kwalembedwa; Iwo amene uthenga wace sunawafikire, adzaona, Ndipo iwo amene sanamve, adzadziwitsa (Aroma 15:20-21)**

### **MAGULU A ANTHU**

Paulo anagwira ntchito ndi magulu a anthu mkati mzinda ndi madera. Mwachitsanzo, analalikira kwa Ahelene ndi ayuda ku Antiyokeya (Machitidwe 13:42). Gulu la anthu linali la mtundu wa chikhalidwe, chiyankhulo chofanana. Ndi kofunikira kumaona mudzi kapena mzinda mu magulu a zikhalidwe zawo ndi kupanga dongosolo la kukulitsa mu kulumikiza.

Mwachitsanzo, mzinda umodzi ku Amerika muli anthu ambiri olankhula chi spanishi, chingerezi ndi chimwenye. Kukula pa kulumikiza kumanga mipingo mu mizinda imeneyi muyenera kuona magulu onse a anthuwa. Kudala mipingo mkati mwa anthu a magulu osiyana kumapititsa uthenga wabwino patsogolo. Pakuti anthu a maguluwa amalankhula zilankhulo zosiyana ndipo ndi a zikhalidwe zosiyanso. Choncho palibe chimene chingatchinge uthenga wabwino kaya zilankhulo kapena zikhalidwe. Mu phunziro latha mwaphunzira kuti anthu amene amakhala limodzi, amalankhula zilankhulo zofanana ndipo ali ndi zikhalidwe zofanana.

Anthu amene ali ngati ife, akhoza kugawidwa mkukhala mmagulu a ang'ono ndi cholinga chofalitsa uthenga. Mwachitsanzo, mumachita izi pokhala ndi magulu a maphunziro a sunde sukulu molingana ndi zaka zawo. Mukhonzanso kuchita izi pamene mukufuna kufikira anthu amabiri a mmagulu.

Harvestime international Institute ali ndi phunziro la “*Kuzindikira Malo*” limene limathandiza kudziwa malo ofunika pa utumuki. Taganiza kuti mukhale ndi phunziroli pa kudzala mpingo.

Phunziroli likuthandizani mmalo:

1. Kudziwa anthu amene mukawafikire. Ndi anthu amagulu ati osiyana amene mukawafikire mmizinda kapena mmadera. Ndi ndani amene mukufuna kukafikira? Zipembedzo zawo, zikhalidwe ndi zilankhulo zawo.
2. Kudzindikira zosowa zawo za ku uzimu. Mwachitsanzo, kodi mkofunika kudzala mpingo pakati pa anthu a chilankhulo cha chisena. Mwina zosowa zawo zikutumikiridwa koma amene amalankhula zilankhulo zina sakuthandizidwa.



3. Kudziwa kulandilidwa kwa uthenga wabwino:
4. Kudziwa njira zimene mukagwiritse ntchito pofikira anthu onse. Kodi afikilidwa bwanji? Nanga ndi ndani amene afikire? Mukuyenera kuwafikira monse mmene angamvere ndi kumvetsetsa mwa zikhalidwe zawo. Mwachtsanzo, ngati gulu lina silingawerenge, kulalikira kowapatsa zowerenga sikungawathandize powafikira ndi uthenga.

### **KUFUNA KUSINTHA MALINGANA NDI ZIKHALIDWE:**

Paulo anafunitsitsa kusintha kwa anthu osiyana zikhalidwe ndi muteso mmadera (onani I Akorinto 9:16-23). Munthu amasunthika ndi chikhalidwe chimene wakulilamo. Anthu a zikhalidwe zosiyana amasiyananso mu zochita.

### **KUSIYANA KWA ZIKHALIDWE**

Paulo sanagofuna kusintha pa zikhalidwe zokha ayi, koma sanalole kuti uthenga wabwino utchingidwe ndi zikhalidwe.

Ku maiko a aluya, ngati wokhulupirira watsopano afuna kusiya mpingo wa pabanja lake chifukwa cha chikhulupiriro chake, amakhala limodzi ndi anthu ofanana naye chikhulupiriro mu mpingo. Onse amalankhula chiyankhulo chimodzi ndi kukhala ndi makhalidwe amodzi. Koma ku maiko ena kumene chikhristu chimati munthu ayenera kusiya chikhalidwe chake ndi kuyamba kukhala ndi achikhulupiriro chimodzi, uthenga wabwino umafalikira mochedwa. Zikhalidwe zina zimalemekezedwa kuposa za anthu ena. Mitundu, zikhalidwe zonsezi ndi zofunikira kwambiri.

Mu Chipangano Chatsopano, pamene munthu wakhala khristu sizimatanthauza kuti wasiya kukhala mu wosatira chi Yuda. Ngakhale wamitundu sayenera kulandira mdulidwe wa chiyuda. Komayambiriro kunali mavuto pa ayuda amene amaika lamulo pa amitundu polalola kuti azidulidwa ngati atembenuka mtima. Koma Paulo ananena kuti ameneyu anali katundu wosayenera kusenza. Mukhoza kuwerenga za izi pa Machitidwe 15.

(Chidziwitso: tikamakamba za “chikhalidwe” timakamba za makhalidwe osiyana potengera zikhalidwe za anthu ndi mtundu zimene sizimaphwanya malamulo a Mulungu. Machitidwe a uchimo samaloledwa.

### **NTHAWI:**

Paulo amasinthanso nthawi imene amakhala nawo mu zikhalidwe za anthu malingana ndi zosowa zawo. Mmallo ena amakhalamo masiku ochepe. Onani Machitidwe 21:4. Ndipo malo ena amakhalako nthawi yaitali, onani Machitidwe 14:28. Anali woyendayenda ndipo dongosolo lake limatsogozedwa ndi Mzimu Woyera.

### **KULANKHULA KWA ANTHU AMBIRI:**

Paulo amalankhula uthenga wake kwa anthu ambiri. Anagwiritsa ntchito mwayi wolankhula kwa anthu ambiri:

**Ndipo kunali pa Ikoniyo kuti analowa pamodzi m'sunagoge wa Ayuda, nalankhula kotero, kuti khamu lalikuru la Ayuda ndi Ahelene anakhulupira (Machitidwe 14:1)**

### **KUKHALA WOPHUNZIRA:**

Paulo analalikira ku khamu la anthu komanso amadziwa kufunika kopereka moyo wake kwa anthu ochepa amene anli ofunika okhala ndi kuthekera kophunzitsa ena. Timoteo anali mmodzi wa anthuwa komanso Tito ndi Yohane Marko, amene nthawi ina anakanidwa pa maphunziro a kukhala wophunzira (Machitidwe 15:36-40). Anali Paulo amene Mzimu Woyera anamuulira zolinga za Mulungu pa wokhulupirira onse kuti achulukane mu uzimu (II Timoteo 2:2).

Kugwira ntchito limodzi ndi okhulupirira ena monga Banabasi ndi Sila, ndi ophunzira ena amene anawaphunzitsa, kunachulukitsa utumiki wa Paulo mtumwi. Pa ulendo wake wachiwiri ndi wachitatu, Paulo anlemba za thandizo la amene anagwira nawo ntchito limodzi amene anli mzika za madera awo kumene anakonza kuti agwireko ntchito.

Iyi ndi mfundo yaikulu. Anthu a ku afilika akhoza kufikira anzawo a ku Afilika momwense anthu a mitundu ina. Chifukwa amalankhula chilankhulo chofanana, komanso zikhalidwe zawo zofanana.

### **MIPINGO YOIMA PAWOKHA:**

Paulo anadzala mipingo yoima pawokha. Ngakhale inali pa ubale ndi likulu la mpingowo kumbali ya chiyanjano chawo ndi utsogoleri, simadalira mpingo waukulu. Paulo samatenga thandizo la umishoni kapena iwo kuonetsa kuti Paulo antengako thandizo lopita ku mipingo ina ya zikhalidwe zina. Amapeza yekha thandizo la mipingo imene amadzala imene inalonso yokonzeka kuima payokha posadalira thandizo la kwina.

Nkhani zonse za chuma zothandizira kukula kwa mpingo zikuyenera kupanga anthu kuti azizilamulira okha. Ngati mpingo ulandira thandizo kuchokera ku mipingo ina, ndiye kuti mpingowo ukudalira amenewo. Ngati mpingo wothandizawo walephera, ndiye kuti mpingo umene ukudalirawo udzalepheranso. Ngati ubale wa maiko suli bwino, mpingo udzakumana ndi mavuto ngati thandizo lasiya kubwera.

Ambuye yemweyo amene anasandutsa madzi kukhala vinyo ndi kuchulukitsa mkate ndi nsomba zimene anadyetsa khamu la anthu ndi wokuthanso kubweretsa chuma chofunikira kufalisira uthenga.

Ulamuliro wogwiritsa ntchito mphatso za mzimu ukyenera kupatsidwa ku mpingo watsopano kamodzi ndi utsogoleri umene ulipo pa mpingo watsopano. Pamene Paulo anasankha akulu a mpingo, anasankhidwa kuchokera pakati pa anthu osati kuchokera kwina kwake.

**Cifukwa ca ici ndinakusiya iwe m'Krete, kuti ukalongosole zosowa, nukaike akuru m'midzi yonse, monga ndinakulamulira (Tito 1:5)**

Paulo anagwiritsa ntchito mipingo yatsopano mmadera onse amene amapita monga pemphero, kupereka, ndi ngati ogwira ntchito limodzi okulitsa mpingo mchiwerengero, ndi polumikiza ndi anthu ena. Onani Machitidwe 20:4, Aefeso 6:19 ndi Afilipi 1:5,7; 4:14-16.

Mpingo uliwonse umene Paulo anadzala unali likulu latsopano la kuchulukana ku uzimu.

**Pakuti kuturuka kwa inu kudamveka mau a Ambuye, osati m'Makedoniya ndi Akaya mokha, komatu m'malo monse cikhulupiriro canu ca kwa Mulungu cidaturuka; kotero kuti sikufunika kwa ife kulankhula kanthu (I Atesalonika 1:8)**

Paulo anadzala mipingo yambiri pa Mau a Mulungu ndi thanthwe, Yesu Khristu. Sanaikhazikitse pa bungwe kapena mpingo kapena umunthu wake. Kubweretsa kudalira sikumaphunzitsa kuima pawekha.

## MAYESO ODZIYETSA NOKHA

1. Lembani Vesi Lotsogolera kuchokera pamtima.

---

---

---

---

2. Lembani tanthauzo la mawu oti “kukula kwa mpingo kolumikiza”

---

---

---

3. Tchulani vesi imene imakamba za dongosolo la Khristu la “kukulitsa mpingo polumikiza”

---

---

4. Ndi ndani amene anali mtsogoleri mu Chipangano Chatsopano pa “kukulitsa mpingo polumikiza” kwa amitundu?

---

---

5. Lembani chidule cha njira zimene Paulo angwiritsa ntchito pofalitsa uthenga wabwino kwa anthu a zikhalidwe zina.

---

---

---

---

---

---

---

---

(Mayankho a mafunsowa akupezeka kumapeto kwenikweni kwa bukuli)

## KUPITILIZA KUPHUNZIRA

1. Mpingo wa ku Antiokeya unadzalidwa ndi mpingo wa ku Yerusalemu. Chitatha chizunzo cha Stefano, okhulupirira ambiri anathawa ku Yerusalemu. Ena anabwera ku mzinda wa Antiokeya ku Siriya, mzinda waukulu ku ufumu wa Chiroma. Kumeneko anakakhazikitsa mpingo (Machitidwe 11:19-21).

Ophunzira kwa nthawi yoyamba anatchedwa akhristu ku Antiokeya. Uwu unali mpingo woyamba kwa anthu amene sanali ayuda koma anli pd chiyanjano chabwino. Aheleni amitundu ndiwo amene anali mu mpingowo. Antiokeya unakhalano mzinda waukulu wa mipingo ya Chipangano Chatsopano. Utumiki umene tili nawo pano umachokera ku Antiokeya, osati ku Yerusalemu kumene anthu ake anali a chikhalidwe cha chiyuda basi.

2. Kufala kwa uthenga wabwino kwa Paulo mu zikhalidwe za anthu ena chidule chake ndi ichi mu maulendo wake wachitatu wa umishoni:

Ulendo woyamba:	Machitidwe 13:1-14:28
Ulendo wachiwiri:	Machitidwe 15:36-18:22
Ulendo wachitatu:	Machitidwe 18:23-21:14

3. Werengani umboni wa Paulo mu Machitidwe 22:

Asanatembukire kwa Khristu:	Machitidwe 22:3-5
Kutembenuka mtima:	Machitidwe 22:6-11
Utumiki wake:	Machitidwe 22:12-16
Ntchito yake ya umishoni:	Machitidwe 22:17-21

4. Werengani zambiri zokhuza Paulo mmene anayendera ulendo wake ku Aefeso:

Anthu anakumana:	Machitidwe 18:19; 19:1,8,9
Uthenga wabwino unaperekedwa:	Machitidwe 19:4,9,10
Omvera anatembenuka:	Machitidwe 19:5,18
Okhulupirira anasonhkana:	Machitidwe 19:9-10
Chikhulupiriro chinatsimikizidwa:	Machitidwe 20:20, 27
Atsogoleri anapatulidwa:	Machitidwe 20:17,28; I Timoteo 1:3,4;
Mpingo unayamikidwa:	Machitidwe 20:17; Aefeso 1:1-3,15,16

5. Kodi kukula kwa mpingo polumikiza mu chipangano chatsopano kumachita bwino? Onetsetsani izi:

... Ndipo panakhala cimwemwe cacikuru m'mudzimo (Samariya): Machitidwe 8:8

... Ndipo anamuona iye onse akukhala ku Luda ndi ku Sarona, natembenukira kwa Ambuye amenewa: Machitidwe 9:35

... Koma mau a Mulungu anakula, nacurukitsa (Machitidwe 12:24).

... Ndipo mau a Ambuye anabukitsidwa m'dziko lonse (Machitidwe 13:49)

... Kotero Mipingoyo inalimbikitsidwa m'cikhulupiriro, nacuruka m'ciwerengo cao tsiku ndi tsiku (Machitidwe 16:5)

... Ndipo anacita comweco zaka ziwiri; kotero kuti onseakukhala m'Asiya anamva mau a Ambuye, Ayuda ndi Ahelene (Machitidwe 19:10)

...Cotero mau a Ambuye anacuruka mwamphamvu nalakika (Machitidwe 19:20)

...mu mphamvu ya zizindikilo ndi zozizwitsa, mu mphamvu ya Mzimu Woyera; kotero kuti ine kuyambira ku Yerusalemu ndi kuzungulirako kufikira ku Iluriko, ndinakwanitsa Uthenga Wabwino wa Kristu; ndipo cotero ndinaciyesa cinthu caulemu kulalikira Uthenga Wabwino, pa malopo Kristu asanachulldwe kale, kuti ndisamange nyumba pa maziko a munthu wina (Aroma 15:19)

6. Muyeso wa anthu ndi malo a anthu amene anatembenuka mtima amaonetsera za mmene mpingo wa chipangano chatsopano unalumikizana mmagulu, muzikhalidwe, ndi mmadera ndi uthenga wabwino.

## CHAPUTALA CHA 10

### ZISANKHO KAPENA OPHUNZIRA?

#### ZOLINGA:

Pakutha pa chaputalachi muyenera:

- Kulemba Vesi Lotsogolera kuchokera pamtima.
- Kupereka tanthauza la “kutembenuka.”
- Kupereka tanthauzo la “wophunzira.”
- Kulemba zinthu zitatu zofunika pa kukhala wophunzira.
- Kudziwa mfundo 9 za kukhala wophunzira zimene zikuonetseredwa pa Yesu ndi ophunzira ake.
- Kulemba zinthu 9 za kukhala wophunzira weniweni.
- Longosolani yesero lenileni la wophunzira.

#### VESI LOTSOGOLERA:

**Pomwepo Yesu anati kwa ophunzira ace, Ngati munthu afuna kudza pambuyo panga, adzikane yekha, natenge mtanda wace, nanditsate Ine (Mateyu 16:24)**

#### MAWU OYAMBA

Mwamvapo zambiri za nkhani ya “Kutuma Kwakukulu” kwa Yesu, koma kodi mumamvetsa zenizeni za umishoni umene Yesu anapatsa ophunzira ake? Kodi lamulo linali longokhala ndi anthu atsopano? Kodi anawatsimikizira kuti atha kupanga maulendo mmizinda ndi kumanga mipingo yaikulu? Kodi anawauza za zinthu zofunikira monga chakudya ndi zovala za a umphawi?

Tiyeni tiwerengenso malangizowa kachiwiri:

**Cifukwa cace mukani, phunzitsani anthu a mitundu yonse, ndi kuwabatiza iwo m'dzina la Atate, ndi la Mwana, ndi la Mzimu Woyera:**

**ndi kuwaphunzitsa, asunge zinthu zonse zimene ndinakulamulirani inu; ndipo onani, Ine ndiri pamodzi ndi inu masiku onse, kufikira cimariziro ca nthawi ya pansi pano (Mateyu 28:19-20)**

koyambirira kupita kunali kwa amitundu yonse, kuwaphunzitsa uthenga wabwino ndi kuwabatiza ndi kukhala nawo pa ziphunzitsa a zimene Yesu analamulira.

Ichi chinali choyamba ndi chofunikira. Mukhoza kukhala moyo wanu mu njira zambiri. Mukhoza kuchita ntchito zabwino ngati kuthandiza a umphawi. Mukhoza kumanga mipingo yaikulu. Mukhoza kupanga misonkhano yaikulu ya chipembedzo.

Koma mukuyenera kuchita chinthu chimodzi ngati mukufuna kuwaniritsa zimene Yesu amanena: Mukuyenera kuchita nawo pofikira dziko lapansi ndi uthenga wabwino. Zinthu zonse ngati kutumikira osauka, kumanga mipingo ndi zina, ndi zofunika pakuti zingothandizira ku chofunika chachikulu.

Koma kufikira anthu a mitundu yonse ndi kuposa kulumikiza anthu ku malo a chitsankho cha Yesu. Pofuna kukwaniritsa kutuma kwakukuluku mukuyenera kupita chitsogolo kupitilira kukhala wophunzira.

### **CHISANKHO KAPENA WOPHUNZIRA?**

Mitundu iwiri ya ziphunzitso ikupezeka pa kutuma kwakukula kwa Yesu:

#### **KOYAMBA: KUPHUNZITSA ANTHU KUTI APULUMUTSIDWE**

Anthu akuyenera kumva Mau a Mulungu ndi cholinga choti achitepo kanthu, kulapa ku machimo ndi kubadwa mwatsopano. Chipunzitso chimenechi ndi “uvangeli”:

**Cifukwa cace mukani, phunzitsani anthu a mitundu yonse, ndi kuwabatiza iwo m'dzina la Atate, ndi la Mwana, ndi la Mzimu Woyera (Mateyu 28:19).**

Okhulupirira atsopano nthawi zina amatchedwa “otembenuka mtima.” Munthu wotembenuka ndi wokhulupirira mwa Yesu amene wabadwa mwatsopano mwa chikhulupiriro ndi kukhala gawo limodzi la Ufumu wa Mulungu. (Harvestime International Institute ali ndi phunziro lotchedwa “Chotupitsa ngati Ulaliki” limene limapereka maphunziro a ulaliki kwa anthu amene ndi atsopano mu chikhulupiriro.

#### **CHACHIWIRI: CHIPHUNZITSO PAMBUYO PA KUTEMBENUKA:**

Mutatha kupnzitsidwa za Uthnega Wabwino ndipo mwabwera kwa Yesu, mukuyenera kuphunzira za mmene mungamutsatire Iye.

**Ndi kuwaphunzitsa, asunge zinthu zonse zimene ndinakulamulirani inu; ndipo onani, Ine ndiri pamodzi ndi inu masiku onse, kufikira cimariziro ca nthawi ya panso pano (Mateyu 28:19-20)**

Kutumwa kwa Yesu kumaulula kuti chiphunzitso chopitilira chimayenera kubwera munthu atatha kutembenuka ndi kubatizidwa. Obadwa mwatsopano akuyenera kulangizidwa mmene Yesu anaphunzitsira. Ntchito imeneyi imatchedwa “kuyendera anthu” kapena “kudyetsa nkhusa” kapena “kupanga ophunzira.”



## **TANTHAUZO LA KUPANGA OPHUNZIRA**

Dongosolo la Yesu ndi lokuti mutsogolere otembenuka mtima kukhala ophunzira. Wophunzirandiye amene watembenuka ndi kukhazikika pa maziko a chikhulupiriro cha chikhristu ndi kuthekera kupanganso ophunzira ena ndi kuwatsogolera. Mawu oti “wophunzira” ndiye kuti mwana, amene ali ku sukulu, amene amaphunzira potsatira. Zikuposa mzeru za mmutu. Uku ndi kuphunzira kumene kumasinthha makhalidwe a munthu.

### **CHISANKHO CHA WOPHUNZIRA**

Chisankho ndi gawo lokhalo loyamba pa kukhala wophunzira woona. Otembenuka mtima ayenera kupita chitsogolo pa chisankho chawo chokhala ziwalo za thupi la Yesu zokonzeka kupanganso ophunzira ena. Kupeza ophunzira ena ndi zofunikira, koma kuwaphunzitsa kutsatira ndi kukhala okhwima ku uzimu ndiye zofunikanso. Aliyense amene mukumphunzitsa, mumpange kuti akhalale wophunzira weniweni kuti nayenso aphunzitse ena.

Ili ndi dongosolo la Mbaibulo la kukhala wophunzira molingana ndi mmene Yesu anaphunzitsira. Anasankha ophunzira khumi ndi awiri, nawaphunzitsa kuti nawonso aphunzitse ena. Pamene mukuphunzira chaputala cha 4 cha phunziro ili, dongosolo loti “aliyense aphunzitse” limabweretsa kukulukana kwa okhulupirira, mipingo komanso zipembedzo.

Koma nthawi zonse dziwani zolinga zanu bwino. Sikuti mukuphunzitsa ndi cholinga chopanga utumiki wanu kapena mpingo wanu. Cholinga ndi chakuti mufikire anthu a mitundu yonse molingana ndi Yesu. Kukwaniritsa kutuma kwakukulu sikukutengera mzeru kapena luso lapadera, komano pa kuumba ndi kudzipereka kwa ophunzira.

Ulaliki umabweretsa anthu kutembenuka mtima. Kupereka mwambo kumapanga ophunzira amene akhoza kulalikirira, ndi kutembenuza anthu ndi kuwapanga kukhala ophunzira. Ndipo izi zimapitilira chonchi.

### **KUKHALA WOPHUNZIRA**

Werengani Luka 9:57-62 mu Baibulo lanu. Mu ndimeyi anthu atatu anampeza Yesu ndi khumbo lofuna kukhala ophunzira. Kwa yense, Yesu anaulula machitidwe osiyana okhala wophunzira kuti amafuna:

#### **1. KUWERENGERA MTENGO: Luka 9:57-58**

Munthu woyamba akanamtsata Yesu opandapo kudikira kuti ayitanidwe. Anayesera kukhala wophunzira mwakufuna kwa iye yekha. Koma Yesu anamuchenjeza kuti samvetsa bwino tanthauzo la kukhala wophunzira. Kukhala wophunzira sikuti munthu umangozifunitsa kwa Mulungu ayi, koma ndi maitanidwe a kwa Mulungu. Yesu anaati, “ukanditsata ine, izi ndi zimene udzakumana nazo.” Analongosola kuti kukhala wophunzira umalipira mtengo wake. Sizingakwaniritsidwe ndi kuchita mwa iwe wekha.

## 2. KUCHITA ZOYENERA: Luka 9:59-60

Munthu wachiwiri amene anaitanidwa ndi Yesu kuti “amutsate.” Ku “mutsata” ndiye kuti kubwera pambuyo pa wina amene ali patsogolo, kutsatira chitsanzo. Zimakhuza zomwe umakhulupirira ndi kumvera. Pamene Yesu anaitana ophunzira ake 12, anawapempha kuti amutsatire ndi kumutsata. Sanalongosole za mmene njira yake inalili. Sanawapatse tsatanetsatane wa dongosolo la moyo.

Ophunzira akuyenera kusiya moyo wakale mbuyo chifukwa cha maitanidwe okha basi. Zosankho ndi nsembe zimene izi zimatengera sizidziwika. Wotsatirayo amasiya moyo wachitetezo ndi kukhala moyo wonga ngati wopanda chitetezo mmaso a dziko. Sikukhala kudzipereka ku dongosolo koma kwa munthuyo. Munthuyo ndiye Yesu Khristu.

Mu ndime ya Luka, mmene munthuyu anayankhira ku maitanidwe omtsata Yesu anali “uyambe wavutikira ine kaye...” amafuna kumutsata Yesu, koma sichinali chinthu choyamba pa moyo wake. Yesu sanaganizirepo kuti wotsatira wa iye adzakana zosowa za makolo ake (onani Yohane 19:25-27). Ndi nkhani ya zinthu zoyamba zimene ndi zofunika mu nkhaniyi. Munthuyi amafuna kukaika makolo ake koyamba. Mu nthawi yofunikira iyi ndi pamene Yesu anamuitana kuti amutsatire iye, pasapezeke chinachake chotchinga maitanidwe usanayankhe.

Mu ndime ina Yesu analongosola mwachindunji pa nkhani ya “kutsatira” imene imafuna:

**Pomwepo Yesu anati kwa ophunzira ace, Ngati munthu afuna kudza pambuyo panga, adzikane yekha, natenge mtanda wace, nanditsate Ine (Mateyu 16:24).**

Kudzikana wekha kukuyenera kukhala koyamba usanayambe kunyamula mtanda. Makhaliidwe akale ndi a uchimo akanidwe. (werengani Aroma 7-8 mmene Paulo anavutikira ndi moyo wake). Keneko motha kutenga mtanda. Mtanda ndi chizindikiro cha nsembe, kuwawa, kukanidwa, mavuto, chitonzo pochita chifuniro cha Mulungu. Mtanda ukhoza kukhalanso maitanidwe a kufa chifukwa cha dzina la Khristu.

“kusenza mtanda sizimakamba za zomelera za moyo. Izi ndi za kwa anthu onse. Pakuti ndi ziphinjo, mayesero, kukhumudwa, kuwawadwa chifukwa cha moyo wochimwa wa mdziko. Wokhulupirira sanaikidwe kunja kwa zowawazi. Nayenso amamva kuwawa, amadwala, kukumana ndi ngozi, moto, zopisa za dziko chifukwa cha uchimo. Koma zowawazi sizimatenga mtanda. Kunyamula mtanda ndi kuchokera mu kufuna kwa munthu osti zokakamizidwa ndi zophinja za dziko ayi. Ndipo ndi zopitilira (tsiku ndi tsiku) kusankha kudzikana ku zokhuma za thupi ndi cholinga chomvera Mulungu.

Kunyamula mtanda ndi kofunikira pa kukhala wophunzira. Yesu anati, “Aliyense amene sanyamula mtanda ndi kunditsata sayenera ine.” Kunyamula mtanda sikosangalasa chifukwa ndi nkhani yodzikaniza. Koma ikuyenera kuchitika mwa ufulu chifukwa cha Yesu ndi cholinga chofuna kukhala wophunzira. Kunyamula mtanda, kukupangiseni kusiya zonse za dziko lapansi. Ngati mtima wanu uli pa ndalama ndi zinthu zina, ndiye kuti mwachulukidwa kuti simungatengenso mtanda. Ngati nthawi yanu imatha ndi zinthu za dziko lapansi ndi za thupi, ndiye kuti manja anu aledmedwa sangatengenso mtanda. Mutatha kudzikana nokha ndi kutenga

mtanda, chotstira ndiko kumutsata. Mukuyenera kusiya zonse za moyo wakale ndi maubale a kale a uchimo.

Izi sizitanthauza kuti wophunzira aliyense asiye ntchito yake ayi mdi nyumba yake. Koma akutanthauza kusintha kwa makhalidwe a munthu. Mwa njira ina zikhoza kutanthauza kusiya nyumba, ntchito kapena okonedwa chifukwa cha uthenga wabwino. Mukuyenera kutsatira kumene Yesu akutsogolera. Kukhala wophunzira kukuyenera kukhala koyambirira.

### **ZOLINGA CHENICHENI: Luka 9:61-62**

Munthu wachitatu mu buku la Luka 9:757-62 amafuna kumutsata Yesu, koma amafuna kutero mu njira yake. Kupita kukatsanzika banja lake chinali chodziwika koma Yesu anamiutana kuti amutsate. Kodi cholinga chenicheni chinali chani mmoyo wake? Kukhala wophunzira kapena kuchita zinthu zake? Cholinga cha munthuyi chinali chosakhazikika. Amabwerera mbuyo ndi zomwe amachita kale ndi zatsopano zimene Yesu anamuitanira.

### **NJIRA NDI UTHENGA WA OPHUNZIRA**

Kuitanidwa kukhala wophunzira kumakhuza kutumidwa kuphunzitsa mitundu yonse. Njira ya ophunzira inali yochitira umboni. Yesu anati, “mudzakhala mboni zanga” Machitidwe 1:8. Kutsindika sikunali kwambiri pa zimene akadachita mkukhala. Koma zimene zikadakula mu zimene akanakhala. Kumapeto, otsatira Yesu anadzitenga okha kukhala mboni. Kumapeto a moyo wake, Paulo anati:

**Pamenepo pothandizidwa ndi Mulungu, ndiimirira kufikira lero lino, ndi kuwacitira umboni ang'ono ndi akuru, posanena kanthu kena koma zimene aneneri ndi Mose ananenazidzafika; 23kuti Kristu akamve zowawa, kuti iye, woyamba mwa kuuka kwa akufa, adzalalikira kuunika kwa anthu ndi kwa amitundu (Machitidwe 26:22-23)**

Kuchitira umboni kwa ophunzira kunali kulalikira, kuphunzitsa ndi kuonetsera mphamvu ya Mulungu mwa zozizwa ndi machiritso. Uthenga wa umboni wawo unali uthenga wabwino wa ufumu wa Mulungu:

**Ndipo uthenga uwu wabwino wa Ufumu udzalalikidwa pa dziko lonse lapansi, ukhale mboni kwa anthu h mitundu yonse; ndipo pomwepo cidzafika cimariziro (Mateyu 24:14).**

**Pakuti ndinapereka kwa inu poyamba, cimenenso ndinalandira, kuti Kristuanafera zoipa zathu, mongamwa malembo; 4ndi kuti anaikidwa; ndi kutianaukitsidwa tsiku lacityatu, monga mwa malembo (I Akorinto 15:3-4)**

Izi ndi zimene Paulo anazitcha kuti “choonadi cha uthenga wabwino” (Agalatiya 2:5). Uthenga wina unali wosaloledwa (Agalatiya 1:8).

### **YESU NDI OPHUNZIRA**

Yesu anali ndi ophunzira ake kwa zaka zitatu ndi theka za utumiki wa ntchito imene Mulungu anamutumira kuti akachite. Imeneyi inali ntchito yapamwamba kwambiri. Amakwanitsa kuyendera malo ochepa mu nthawinso yochepayo ndi kufikira anthu ochepa.

Kufuna kutsimikiza mathero a ntchito yake, Yesu anapanga ophunzira ngati chofunikira kwambiri. Amadziwa kuti ophunzira ake adzapanga ophunzira ena ndi kufikira anthu ambir ku midzi ndi mizinda imene Yesu sanakhale ndi mwayi ofikako.

Yesu akanakhala ndi nthawi yonse yodyetsa ndi kuveka osauka. Akanamanga mpingo waukulu ku Yerusalemu. Panali njira zambiri zimene akanatha kugwiritsa ntchito ntchito. Koma Yesu anasankha mafungulo aakulu a kuchulukana ku uzimu. Anadziwa kuti kuika moyo wake mwa okhulupirika ochepa ulendo wochulukitsa umene sudzatha uyamba. Chidwi chake sichinali kufikira khamu, koma pa anthu amene anali ndi kuthekera kufikira makamu a anthu.

Sizitengera kuti mukukhala dera liti, khaya muli ku mzinda waukulu, kaya ku midzi yakytali, munamva uthenga wabwino chifukwa cha kukhulupirika kwa ophunzira a Yesu. Titati tibwerere mbuyo ku mbiri ya uthenga wabwino, unafalikira mpaka utakupezani, njirayo ndiye kuti ikanabwerera kumene kunali ophunzira ake.

Yesu ndiye chitsanzo cha ophunzira. Ngati mutsata chitsanzo chake, mudzazindikira kuti ophunzira woberekana sachokera ku maphunziro a atsogoleri. Yesu anaona kufunikira kwa kupereka mwambo.

Powerenga ubale wa pakati pa Yesu ndi akuphunzira ake, mfundo zambiri za kukhala ophunzira zimaonekera. Izi ndi zofunika pa nkhani ya kukhala ophunzira:

## **1. KUSANKHA:**

Kusankhidwa kwa ophunzira 12 kukupezeka pa Mateyu 5:1; 10:2-4; Marko 3:13-19 ndi Luka 6:12-16. Kusankhidwa kwa 70 aja kukupezeka ku Luka 10:1-16. Kusankhaku chinali chinthu choyamba mu dongosolo lopanga ophunzira. Pamene Yesu anasankha ophunzira, anaitana ngati anthu wamba. Ena anali osaphunzira ndipo anali ndi zolakwika ndi zolephera.

Zakhala zikunenedwa kuti ngati ophunzira 12 aja anayamba awonedwa kaye ndi mpingo wa utumwi mu nthawi yathu ino, sakapatsidwa ntchito yotumikira. Koma Yesu anakhazikika pa kuthekera kwawo osati zooka zawo. Sanawasankhe chifukwa cha mmene analili koma chifukwa cha chimene akanakhala. Anayang'ana kutsogolo kupitilira mavuto awo.

Wokhulupirira aliyense ayenera kupatsidwa mwambo ndi wina wake, simungakwanitse kupanga ophunzira wina aliyense. Ndinu munthu mmodzi yekha ndipo muli ndi malire ku chiwerengero cha anthu ophunzira amene mungawapange mu nthawi imodzi. Ichi ndi chifukwa chake kupanga ophunzira kukuyenera kuchitika mmalo amene mpingo wanu ulili. Mbusa aliyense amakhala ndi chitsimikizo kuti wotembenuka mtima aliyense amaphunzitsidwa ndi okhulupirira okhwima mu uzimu.

Kodi Yesu anasankha bwanji ophunzira:

Koyamba, podalira ndi Mulungu:

**Sindikhoza kucita kanthu kwa Ine ndekha; monga momwe ndimva ndiweruza; ndipo maweruzidwe anga ali olungama; cifukwa kuti sinditsata cifuniro canga, koma cifuniro ca Iye ondituma Ine (Yohane 5:30)**

Kachiwiri, anapemphera, Luka 6:12-13 amakamba kuti Yesu anapereka nthawi yake yonse usiku kupemphera asanasankhe ophunzira amene amawafuna.

Kachitatu, Yesu anayamba kuwaitana ophunzira ake. Anthu sadzabera kwa inu kuti mukhale ophunzira wa Yesu. Mukuyenera kuchitapo kanthu powayitana. Mwa mphamvu ya Mulungu mukuyenera “kupanga” ophunzira.

Kachinayi, Yesu analongosola za mmene kukhala ophunzira kumakhalira. Monga mwaphunzira, ophunzira akuyenera awerengere mtengo wake, kuika zoyambirira, ndi kuipanga ntchitoyi kukhala cholinga chenicheni pa moyo.

Kukhala wophunziranso kumafuna okhulupirika ndi kutha kuphunzitsa ena. Paulo anamuza Timoteo kuti asankhe anthu okhulupirika ndi odzipereka ku zinthu zimene anaphunzitsidwa. Anthu amenewa akuyenera kukhala ndi kuthekera kophunzitsa ena. Zinthu ziwiri izi ndi zofunika pa kuchulukitsa. Ngati munthu Sali okhulupirika, sangathe kukwaniritsa udindo wochulukana ku uzimu. Ngati ali wokhulupirira koma sakwanitsa kuphunzitsa, ndiye kuti adzalephera.

Paulo analankhula za okhulupirira amene akadali ndi kuthekera kophunzitsa ena koma osakhwima ku uzimu kuti atha kutero. Anthuwa ndiye kuti sanakonzekere kukhala ophunzira enieni. Akuyenera kulangizidwa mu maziko a chikhulupirio. Kukhala ophunzira kumafuna “anthu okhulupirika” otha kuphunzitsa enanso.

Anthu okhulupirika sikuti amakhala opanda vuto. Musasokoneze kukhala ophunzira ndi ungwiro. Musakhazikike pa mavuto a munthu amene akufuna kukhala ophunzira. Muyang’ane kuthekera kwawo. Kukhala ophunzira kumatenga nthawi kuti munthu akhale “wangwiro” monga mmene zilili pa Aefeso 4. Ngakhale anthu okhulupirika amakhalanso ndi zofooka zoti athane nazo monga mmene analili oyamba aja.

Dziko limatenga anthu aluso mkuwapatsa zochita. Amakhazikika pa luko lawo la ntchito. Mulungu anati kutenga okhulupirika a makhalidwe abwino ndipo amawapatsa maluso a uzimu ndi kuthekera. Anthu okhulupirika amapezeka kuti akwaniritse cholinga cha Mulungu. Pamene Yesu anaitana Simoni ndi Andrey, mwachangu anasiya maukonde awo. Mawu oti “mwachangu amanthauza kuozeza kwawo.

Pamene mwasankha anthu oti akhale ophunzira ayenera kupezeka. Amayenera kufuna kupanga ophunzira ndikukhala choyamba ku moyo wawo. Anthu okhulupirikawa amakhala olimbikitsidwa ndi masomphenya a uzimu. Pamene Yesu anampatsa Petro ndi Andrey, masomphenya osodza anthu, zinawalimbikitsa kusiya maukonde awo. Anthu okhulupirika

amakhala ndi njala ya Mau a Mulungu, ngati mmene Yesu anachitira ndi ophunzira ake. Mitima yawo inatekeseka ndi iwo pamene amawagawira Malemba (Luka 24:32,45). Amafuna ndi kukhumba kuphunzitsidwa.

## **2. MAGULU:**

Pamene Yesu anaitana ophunzira ake, anwaitana kuti akhale ndi Iye. Amakhalira limodzi, mmautumiki onse komanso mu nyengo zonse. Kukhala ophunzira sikubwera chifukwa cha misonkhano kapena maphunziro tsiku lolambira. Mukuyenera kukhala pa ubale ndi iwo amene ndi ophunziranso. Muyenera mugawane nawo moyo wanu ndi iwo.

## **3. KUDZIPATULA**

Kuchokera mu chiyanjano chimene anali nacho ndi Yesu, kudzipatula kunayamba. Yesu anaitana ophunzira ake kuti adzipatule ku umuthu osati ku mpingo kapena bungwe. Kudzipatulira kwa Mulungu kumafuna kumvera kwatunthu ku Mau ndi cholinga chake. Onani Yohane 4:34; 5:30; 15:10; 17:4; and Luka 22:42).

## **4. MASOMPHENYA:**

Yesu anawalimbikitsa ophunzira ake pa kuwapatsa masomphenya a uzimu. Anawaitanira ku ntchito yaikulu kwambiri kuposa imene iwo amaidziwa mmoyo wawo wa tsiku ndi tsiku. Anawaitana ophunzira ake kukhala asodzi a anthu (Mateyu 4:19). Anawapatsa masomphenya a dziko lonse pa zokolola za uzimu (Yohane 4:35). Anawatsimikizira ndi mavumbulutso a ufumu wa Mulungu (Mateyu 13).

## **5. MALANGIZO:**

Malangizo amene Yesu amawapatsa amagwirizana ndi masomphenya a uzimu. Ngati wophunzira wa Yesu amayenera kuphunzitsa zimene Yesu anaphunzitsa. Ili ndi gawo limodzi la kutuma kwakukulu kopezeka pa Mateyu 28:20. Chidwi chikuyenera kukhala pa chiphunzitso cha Yesu ndipo zimene zimaululika pa ziphunzitsozi zikhale zimene mpingo uyenera kumachita.

Maphunziro a Harvestime International Institute amapereka maphunziro a kukhala wophunzira. Ndipo ndi chaputala chomalizira pa phunziroli. Komanso ali ndi phunziro limene limatchedwa “Luso pa Kaphunzitsidwe” limene limakuphunzitsani inu kuti muthenso kuphunzitsa anthu ena monga mmene Yesu anaphunzitsira.

Pamene mukuphunzitsa zimene Yesu anaphunzitsa, mumaphunzitsa zonse zimene zili mu Mau a Mulungu chifukwa choti zakhazikika pa Chipangano Chatsopano monga Yesu anati:

**Ndipo anati kwa iwo, Awa ndi mauwo ndinalankhula nanu, paja ndinakhala ndi inu, kuti ziyenera kukwanitsidwa zonse zolembedwa za Ine m'cilamulo ca Mose, ndi aneneri, ndi masalmo...**

**ndipo anati kwa iwo, Kotero kwalembedwa, kuti Kristu amve zowawa, nauke kwa akufa tsiku lacityatu;**

**ndi kuti kulalikiidwe m'dzina lace kulapa ndi kukhululukidwa kwa macimo kwa mitundu yonse, kuyambira ku Yerusalemu (Luka 24:44, 46-47)**

## **6. KUONETSERA:**

Yesu sanaphunzitse kuchokera pa zolankhula zokha ayi. Amaonetseranso zimene amaphunzitsa u machiritso kwa odwala. Anali ndi mphamvu yotulutsa ziwanda ndi ulamuliro pa Satana. Anaika chidwi pa osauka nawapatsa chakudya. Ophunzira sanali ophunzira okha, komanso anali mboni pa zimene Yesu amachita ndi mphamvu ya Mulungu. “Cimene cinaliko kuyambira paciyambi, cimene tidacimva, cimene tidaciona m'maso mwathu, cimene tidacipenyenera, ndipo manja athu adacigwira ca Mau a moyo (I Yohane 1:1).

Yesu anaphunzitsa nakhala chitsanzo. Anaonetsera zimene anaphunzitsa ndi mmene anakhallira ndi kutumikira. Ndipo anati:

**Pakuti ndakupatsani inu citsanzo, kuti, monga Ine ndakucitirani inu, inunso mucite (Yohane 13:15)**

Kuonetsera kwa mphamvu kumapangitsa anthu kuti akhale ndi chidwi ku uthenga:

**Ndipo makamuwo ndi mtima umodzi anasamalira zonedwa ndi Filipo, pamene anamva, napenya zizindikilo zimene anazicita (Machitdwe 8:6)**

Paulo sanalankhule za choonadi cha uthenga wokha (Agalatiya 2:5) komanso za mphamvu ya uthenga wabwino (Aroma 1:16). Analengeza ndi kuonetsera uthenga (I Akorinto 2:1,4).

Chifukwa cha kufunika kwa kuonetsera mphamvu mu kuchulukitsa, Harvestime International Institute ali ndi phunziro lotchedwa “Mfundo za Mphamvu” ku maphunziro amenewa.

## **7. KUTENGA NAWO MBALI:**

Chidziwitso chokhal sichipindula. Kuti uchite bwino, chidziwitso chiyenera chigwire ntchito. Keneko imafika nthawi yoti muchitepo kanthu. Ophunzira samangomvetsera ndi kuonera ziphunzitsa za Yesu ndi chionetsero cha mphamvu koma amtenga nawonso mbali. Kuphunzitsi chithu sizikwanira kuti utha kuphunzira. Kuphunzitsa kokha kuli ngati kuyera oparesoni ya mu ubongo powerenga mabuku.

Ophunzira akuyenera kukhala ndi luso kapena mzeru za kachitidwe ka zinthu ka zimene akuphunzira. Akuyenera kudziwa za mmene angalalikire uthenga, kupempherera odwala, ndi kutulutsa ziwanda. Yesu amapereka mwayi umenewu kwa ophunzira ake. Werengani pa Marko 6:7-13 ndi Luka 9:1-6. Yesu anawatuma ophunzira ake kuti akayesere zimene anawaphunzitsa. Onetsetsani kuti ophunzira anu ali ochita mawu osati ongomva kokha.

## **8. KUYANG'ANIRA**

Pamene ophunzira a Yesu anabwerera ku utumiki umene Yesu anawatuma, Yesu anasanthula ntchito yawo (Luka 9:10). Mu maphunziro onse amen anachita nawo Yesu amawayng'anira ophunzira ake. Samawasiya wokha kuti azilimbana nazo zinthu. Amakhala nawo kuti awakonzere, kuwadzudzula ndi kuwalimbikitsa.

Simungayerekeze kuti ntchitoyi mukhoza kuichita chifukwa mwamuonetsera wogwira ntchito machitidwe ake, ndi kutuma ndi chiyembekezo chonse. Mukuyenera kumuyang'anira. Monga ophunzira amakumana ndi zokhumudwitsa ndi zoletsa, mukuyenera kuwaphunzitsa za mmene angakumaire ndi zimenezi. Kuyang'anira nthawi zina kumatchedwa "kulondola." Paulo amayang'anira komanso "kulondola" ophunzira ake:

**Atakhala kumeneko nthawi, anacoka, napita pa dziko la Galatiya ndi Frugiya m'dziko m'dziko, nakhazikitsaakuphunzira onse (Machitidwe 18:23)**

**nalimbikitsa mitima ya akuphunzira, nadandauliraiwo kuti akhalebe m'cikhulupiriro, ndi kuti tiyenera kulowa m'ufumu wa Mulungu ndi zisautso zambiri (Machitidwe 14:22)**

#### **KUPATSA ENA NTCHITO:**

Gawo lomaliza la kukhala wophunzira linali pamene Yesu amapatsa ophunzira ake chochita pa kukhala anthu opanga ophunzira ena. Anawapatsa ntchito ya kuchulukitsa ku uzimu kudziko lonse lapansi.

#### **MAKHALIDWE A WOPHUNZIRA WENIWENI**

Ophunzira ayesu akuyenera kukhala okhulupirira okhwima ndi kuonetsa chipatso cha Mzimu Woyera ngati chizindikiro mmoyo wawo komanso mphatso za mzimu zikhale zochitachita mmautumiki awo.

Pali makhalidwe ambiri a kukhala wophunzira weniweni wa Yesu pamene mukuona zimene Mau a Mulungu akufotokozera, koma Yesu anakhazikika pa makhalidwe 9. Wophunzira ndiye amene:

##### **1. AMASIYA ZINTHU ZONSE:**

Amasiya zonse ndi kuyamba kumutsata Yesu.

**Cifukwa cace tsono, yense wa inu amene sakaniza zonse ali nazo, sakhoza kukhala wophunzira wanga (Luka 14:33)**

##### **2. KUDZIKANA WEKHA:**

Wophunzira woona ayenera kudzikana yekha ndi kunyamula mtanda mwaufulu:



**Pomwepo Yesu anati kwa ophunzira ace, Ngati munthu afuna kudza pambuyo panga, adzikane yekha, natenge mtanda wace, nanditsate Ine (Mateyu 16:24)**

**Ndipo amene ali yense sasenza mtanda wace wa mwini yekha, ndi kudza pambuyo panga, sakhoza kukhala wophunzira wanga (Mateyu 14:27)**

### **3. KUTSATIRA YESU:**

**Pomwepo Yesu anati kwa ophunzira ace, Ngati munthu afuna kudza pambuyo panga, adzikane yekha, natenge mtanda wace, nanditsate Ine (Mateyu 16:24)**

### **4. KUPANGA UFUMU WA MULUNGU KUKHALA WOYAMBA:**

**Cifukwa cace musadere nkhawa, ndi kuti, Tidzadya ciani? kapena, Tidzamwa ciani? kapena, Tidzabvala ciani**

**Koma muthange mwafuna Ufumu wace ndi cilungamo cace, ndipo zonse zimenezo zidzaonjzedwa kwa inu (Mateyu 6:31,33)**

### **5. KUONETSERA CHIKONDI CHA MULUNGU:**

**Ndikupatsani inu lamulo latsopano, kuti mukondane wina ndi mnzace; monga ndakonda Inu, kuti inunso mukondane wina ndi mnzace. 351 Mwa ici adzazindikira onse kuti muli akuphunzira anga, ngati muli naco cikondano wina ndi mnzace (Yohane 13:34-35)**

### **6. KUKHAMA MMAWU:**

**...Ngati mukhala inu m'mau anga, muli akuphunzira anga ndithu (Yohane 8:31)**

Mawu oti “kukhala” amanthauza kuti kupitilira. Wophunzira amakhala akuphunzira mopitilira ndi kugwiritsa ntchito Mau a Mulungu.

### **7. NDI OMVERA:**

Kukhala mu Mau kumaposa kuphunzira. Uku ndi kuchita zimene mwaphunzira. Ndiye kumvera. Sizikwanira kuwerenga, kuphunzira kapena kuloweza Mau. Amayenera apange chikhalidwe cha munthu. Kukhala mu Mau kumaphtikizapo kumvera.

### **8. NDI OTUMIKIRA:**

**Kumkwanira wophunzira kuti akhale monga mphunzitsi wace, ndi kapolo monga mbuye (Mateyu 10:25)**

**Sikudzakhala comweco kwa inu ai; koma amene ali yense akafuna kukhala wamkuru mwa inu, adzakhala mtumiki wanu;**

**Ndipo amene ali yense akafuna kukhala woyamba mwa inu, adzakhala kapolo wanu**

**Monga Mwana wa munthu sanadza kutumikiridwa koma kutumikira, ndi kupereka moyo wace dipo la anthu ambiri (Mateyu 20:26-28)**

## **9. KULEMEKEZA MULUNGU MWA KUBEREKA ZIPATSO:**

Wophunzira ayenera kulemekeza Mulungu pobereka zipatso:

**Mwa ici alemekezedwa Atate wanga, kuti mubale cipatso cambiri; ndipo mudzakhala akuphunzira anga (Yohane 15:8)**

Pamene mubala chipatso cha ku uzimu, mumakuza chipatso cha Mzimu Woyera mu moyo wanu (Agalatiya 5:20-23). Mumabala chipatso poberekana ku uzimu (Yohane 15:1-16)

### **YESERO LENILENI LA WOPHUNZIRA**

Yesero lenileni la wophunzira ndi zimene zimzchitika pamene simukupezeka ndi iwo amene munawaphunzitsa. Kodi mumakhalabe okhulupirika ku zimene munaphunzitsidwa? Kodi mumaphunzitsa ena amene ali ndi kuthekera kochulukana? Ngati ndi choncho ndiye kuti kukhala wophunzira kwanu kuli kopambana:

**Wophunzira saposaphunzitsi wace; koma yense, m'mene atakonzedwa mtima, adzafanana ndi mphunzitsi wace (Luka 6:40)**

Mu maphunziro anu ndi ena, yembekezerani mavuto monga mmene Yesu anakumana nawo...

-Munthawi ina yake, Petro, Yakobo ndi Yohane anawonetsa maganizo a udani popempha moto kuchokera kumwamba kuti uwononge mudzi wa Samariya umene sumalandira uthenga (Luka 9:51-55).

-Petro anamkana Yesu katatu (Luka 22:54-62).

-Onse atatu amagona mmunda wa Getsemane pamene anauzidwa kuti apemphere (Luka 22:45-46).

Koma anthu ochepawa anali oyenera kupereka nthawi yawo ku utumiki wa Yesu. Yesu anatsimikira kukhala anthu okhulupirika, posatengera zofooka ndi zolephera zawo. Panthawi imene Yesu sanali ndi iwo anakhalabe ophunzira ochulukitsa ku maiko onse a dziko lapansi. Yesu anati:

**Zotuta zicurukadi koma anchito ali owerengeka (Mateyu 9:37)**

Anthu otuta zokolola oyenera kututa zokolola za uzimu ndi ochepa. Kodi mwakonzeka kupereka moyo wanu kukhala gawo limodzi la ochepawa?

## MAYESO ODZIYETSA NOKHA

1. Lembani Vesi Lotsogolera kuchokera pamtima.

---

---

---

2. Kodi mawu oti “kutembenuka” akutanthauza chiyani?

---

---

---

3. Perekani tanthauzo la mawu oti “wophunzira.”

---

---

---

4. Lembani mfundo zitatu zachidule cha maitanidwe a kukhala wophunzira

---

---

---

---

---

5. Lembani mfundo 9 zimene ndi zofunika kukhala wophunzira zimene mwaphunzira zokhuza Yesu ndi ophunzira ake.

---

---

---

---

---

---

6. Lembani makhalidwe 9 a kukhala wophunzira weniweni.

---

---

---

---

---

7. Kodi yesero lenileni la wophunzira ndi liti?

---

---

---

(Mayankho a mafunsowa akupezeka kumapeto kwenikweni kwa bukuli)



## KUPITILIZA KUPHUNZIRA

1. Kupereka mwambo kuli ngatinso “kudyetsa nkhosa” mawu amene amaonetsedwa Mbaibulo za mmene mbusa angasamalire nkhosa zake.

Mulungu ali ngati mbusa: Ahebri 13:20; Masalmo 80:1-2 ndi Ezekieli 34:11

Yesu ali ngati mbusa wa nkhosa: Yohane 10:11-18

Mbusa ndi wotsogolera, woyang’anira kapena mlonda wa nkhosa. Amazipulumutsa ku choipa, namanga mabala, kuzikonda ndi kudzidyetsa. Werengani Mateyu 9:36-38; Marko 3:14- 15; Yohane 21:15-17; Machitidwe 20:28.

2. Kuitana kwambiri kwa Yesu Khristu ndi kobwerezabwereza. Mawu oti “unditsate” agwiritsidwa ntchito koposa ka 20. Mwachitsanzo Simoni ndi Andreyu; Mateyu 4:19; Marko 1:17. Onani zitsanzo zina.
3. Mawu oti “ophunzira” sakupezeka Muchipangano Chakale, koma mfundo za kupereka mwambo zikupezekamo. Mwachitsanzo Yoswa anali wophunzira kwa Mose (Deuteronomo 3:28). Perekani zitsanzo zina.
4. Onani mmene Paulo anachitira kalondolondo kwa ophunzira ake:

Ndi kalata: I Atesalonika 1:1

Ndi pemphero: I Atesalonika 1:2; 3:10

Potuma nthumwi: I Atesalonika 3:1-5

Popita yekha I Atesalonika 2:18

## CHAPUTALA CHA 11

### KUKULA MOPINIMBIRA

#### ZOLINGA:

Paakutha pa chaputalachi muyenera:

- Kulemba Vesi Lotsogolera kuchokera pamtima.
- Kupereka tanthauzo la mawu oti “kupinimbira.”
- Kuzindikira zinthu zimene zimatchinga kukula ku uzimu ndi kuchulukana.
- Kupereka zithandizo zimene Baibulo limapereka pokonza mavuto amenewa.

#### VESI LOTSOGOLERA:

**Wodala munthuyo wosayenda mu uphungu wa oipa, Kapena wosaimirira m'njira ya ocimwa, Kapena wosakhala pansu pa bwalo la onyozu.**

**Komatu m'cilamulo ca Yehova muli cikondwerero cace, Ndipo m'cilamulo cace amalingima usana ndi usiku.**

**Ndiye akunga mtengo wooka pa mitsinje ya madzi; Wakupatsa cipatso cace pa nyengo yace, Tsamba lace lomwe losafota; Ndipo zonse azicita apindula nazo (Masalmo 1:1-3)**

### MAWU OYAMBA

Pali zinthu zambiri zimene zimakhudza kukula kwa munthu. Kuperewera kwa chakudya choyenera kumatchinga kukulaku. Matendanso a mitundumitundu amakhudza kukula. Pamene kukula kukusowa mthupi, pakuyenera kukhala chopulumukirapo chimene chingakonze vutoli kupanda kutero kukula kupinimbira. Pamene kukula kuli kopinimbira, thupi silikulanso bwino.

Pamene mukuphunzira phunziroli, Baibulo limaonetsera mpingo ngati thupi la munthu. Pokhala thupi la munthu, makulidwe amakhudzidwa ndi zinthu zina. Nthawi zina mavuto amachitika mu mpingo ndiwo amene amalepheretsa kukula ku uzimu. Pamene kukula mu uzimu kuli kopinimbira, mpingo umalephera kukula. Pakusowa anthu ndi ophunzira ndi kusowa kwa kukhwima mu uzimu.

Yesu anati, “ndidzamanga mpingo.” Sitingabweretse kuchulukana tokha, koma tikhoza kuchotsa zinthu zimene zimalepheretsa kukula. Pamene tikutero, ndiye kuti tikupanga malo ati kukula kungachitike. Chaputala ichi chikuonetsa mavuto amene amalepheretsa kuchulukana. Pa vuto lililonse pali Vesi yake imene ingakonze vutolo.

### KUKULA KOPINIMBIRA

**VUTO: KUSOWA CHAKUDYA CHA UZIMU.**

Thupi la munthu liyenera kupatsidwa chakudya ndi madzi kupanda kutero limafa. Thupi la uzimu liyenera kupatsidwanso chakudya ndi madzi kupanda kutero limafa. Mipingo ina simaphunzitsa Mau a Mulungu koma amaphunzitsa ziphunzitso za anthu. Amanena zimene anthu afuna kudzimva (II Timoteo 4:3). Kuperewera zakudya za ku uzimu kumabweretsa njala ya Mau a Mulungu (Amosi 8:11-12). Ena amanh=gophunzita “mkaka” wa mau ndipo anthu sakula ku uzimu. Okhulupirira amanyalanyaza kuwerenga Mau a Mulungu kapena sasanthula maziko a choonadi cha ngati “nyama” ya Mau a Mulungu. Monga thupi limafa popanda chakudya, thupi la uziminsi limafa.

### **YANKHO:**

Kutsindikanso kobwereza pa Mau a Mulungu (Aroma 10:17). Phunzitsani mkaka ndi nyama ya Mau a Mulungu (I Akorinto 3:1, I Petro 2:22 ndi Ahebri 5:12-14). Thupi la munthu silingadalire mkaka konse. Ngakhale mwana wang’ono ayenera kuphunzira kudya chakudya cholimba. Mau a Mulungu ndi mkate wa moyo wa uzimu.

### **VUTO: KUSOWA MASOMPHENYA.**

Baibulo limati “popanda masomphenya anthu amasochera” (Miyambo 29:18). Masomphenya a uzimu a anthu ena ndi amalire kubanja ndi kudera lawo. Ena amatanganidwa ndi malo ena akutali ndi zinthu za mayina a chilendo, pamene anthu kunja kwa mpingo akufa opanda Yesu.

### **YANKHO:**

Pakuyenera kukhala kufanana masomphenya azochitika zathu ndi za uzimu. Mpingo ukuyenera kukhala ndi masomphenya a dziko lonse koma osasiyanso iwo amene ali mdera lathu. Awa ndi masomphenya amene Yesu anapatsa ophunzira ake a zokolola za uzimu zimene zapsa kale mmunda. Mundawu ndi dziko. Werengani Yonane 4.

### **VUTO: KUKULA KOCHIPA.**

Werengani fanizo la ofetsa mu Marko 4:1-20. Pamene mbewu ya Mau a Mulungu sikhala ndi muzu mmoyo wanu, mumakhala ndi kukula kochipa. Pamene chizunzo ndi zovuta zabwera mumafa ku uzimu (Marko 4:17).

### **YANKHO:**

Phunzitsani anthu kuti kuwerenga, kumva ndi kuphunzitsa Mau a Mulungu sikokwanira. Akuyenera kukhala ochita Mau a Mulungu. Akuyenera kusintha moyo wawo (Yakobo 1:22-25). Ndi pakulowa kwa Mau mumtima kumene kumabweretsa kusintha (Masalmo 119:130).

### **VUTO: KUSOWA KUTSADZA**

Mipingo kwanthawi yaitali yakhala yosabereka mu njira zawo ndi dongosolo lawo. Pamene zochitikazi zisizadwidwa, kubala zipatso kumatha. Popanda kutsadza, Pang’ono ndi pang’ono imfa imabwera imakononga moyo. Pamene mtengo sunatsadwidwe ukhoza kumakula moongoka



koma uli wakufa. Palibe zipatso, kukula komanso kuchulukana. Mtengo kukhalapo koma opanda moyo. Izi ndi chomodzimodzi ndi kudziko la uzimu.

**YANKHO:**

Nthambi zosabereka ziyenera kudulidwa ndi cholinga chofuna choti mtengowo ubereke zipatso zambiri. Kudziko la uzimu tikuyenera kudula ntchito zosathandiza mmoyo wathu ndi mumpingo wathu. Njira ndi ndondomeko zimene sizimabweretsa athu kwa Yesu ndi ophunzira zichotsedwe. Mikumano iwonedwenso, kaya ndi ndondomeko ziunukilidwenso ngati ndi zothandiza.

**VUTO: KULEPHERA KUDZIWA MALO AMENE ANGALANDIRE UTHENGA:**

Mu fanizo la ofetsa mu Marko 4:1-20, panali dothi labwino ndi lina losakhala bwino. Kukula kochepa kumachitika mu dothi losakhala bwino.

**YANKHO:**

Pali malo ena amene ali ndi mwayi wochepa wochulukana. Ndipo pali malo ena amene amakhalaokonzeka pa zokolola za uzimu amene amapereka mwayi olalikira uthenga wabwino. Anthu oyenera ayenera adziwike ndi kuchitapo kanthu kwa anthu amenewa. Pamene Paulo anamva Mzimu Woyera kuti akubweretsa anthu amitundu kukhala ophunzira ku Antiokeya, mwachangu anachoka ku Tarisi mkupita ku Antiokeya. Pamene nthawi inali isanakwane ku mAsiya, Paulo anakhalabe kumene mpakana Mulungu anamutsekula maso. Khazikikani ku malo kumene kuli kuthekera. Pitolizani kufesa ndi kudikira nthawi yoyenera kuti mudzatute zikapsa.

**VUTO: ZOFUNIKA ZOLAKWIKWA.**

Atsogoleri a uzimu ali ndi zofunika zimene ndi zolakwika pamene ali ndi chidwi ndi zochita za mpingo kuposa pemphero ndi kutumikira Mau a Mulungu. Zofunika zimakhala zachiwiri monga mamangidwe ndi tchito zina. Kukoza mpingo kumakhala kofunika kuposa utumwi.

**YANKHO:**

Yesu sanalankhulepo za mamangidwe apamamba. Akhristu amapanga zochita zambiri. Ngakhale izi sizolakwika, koma kuchulukana kumalephereka pamene chidwi chikukhala pa mamangidwe osati kulalikira ndi kupanga ophunzira. Vuto la zofunika ndi ziti ndi mayankho ake zikupezeka ku Machitidwe 6:1-6. Pamene atsogoleri aika chidwi pa pemphero ndi kutumikira Mau a Mulungu kuchulukana kumabwera (Machitidwe 6:7).

**VUTO: UTUMIKI WOSAGWIRIZANA NDI ANTHU**

Mipingo ina yasiya kukula chifukwa choti utumiki sugwirizana ndi anthu. Mwina mtumiki sakhala mmodzi wa anthuwo. Amakhala wa chikhalidwe china zimene ndi zovuta kupereka uthenga mu chiyankhulo chimene angamve.

**YANKHO:**

Atsogolera ayenera kuchokera ku mpingo umene akuchokera ngati kuli kotheka pamene mpingo wadzalidwa (Tito 1:5). Atsogolera a kudera amene ali ndi chikhalidwe ndi chiyankhulo cha kumaloko amatha kulumikizana ndi anthu a kumeneko mosavuta.

### **VUTO: “BWERANI MUWONE” OSATI “PITANI MUKAWAUZE”**

Mipingo yambiri yatenga njira ya “bwerani” osti “pitani” imene Yesu analamulira. Mipingoyi imakhala ndi mikumano ndi dongosolo limene limakopa anthu osakhulupirira “kubwera” ku mpingo. Sapita ku dziko kukawapeza ndi uthenga wabwino ndi kuwabweretsa ku mpingo. Amatsekula zitseko mkumadikira anthu kuti abwere, koma palibe amene amabwera. Mu mpingo umenewu mamembala amakangalika ndi mikumano, misonkhano, maphunziro mmalo mwa maulaliki otuluka.

### **YANKHO:**

Mpingo ukuyenera kukhala wogwirira ntchito Mulungu mdzikoli. Koma mpingo wakhala okangalika kusiyana ndi kukhala maziko a Mulungu otumiza ophunzira mmunda wa dziko kukachulukana. Mpingo ukuyenera kusiya kudzitumikira wokha ndi kuyamba kutumikira dziko. Mpingo ukhale malo amene okhulupirira alandirapo maphunziro ndi kukonzekerdwa kupita ku dziko lapansi kumene kuli ochimwa ndi kuwatengera kwa Yesu. Njira ya Yesu yopita iyenera kutsindikizidwa (Mateyu 28:19; Machitidwe 1:8).

### **VUTO: TCHIMO LOSAVOMEREZA**

Tchimo losavomereza mmoyo wa membala wa mpingo limatchinga kukula moyo wauzimu.

### **YANKHO:**

Werengani malangizo a Paulo kwa mpingo wa kwa Akorinto othana ndi tchimo losavomereza kwa munthu (I Akorinto 5:11-13). Ngati membala yi walapa, akuyenera kulandilidwanso (Onani II Akorinto 2:4-8).

### **VUTO: MAVUTO A MUNTHU OSATHA:**

Mikangano imakhala mu mpingo ngati membala wa mpingo akali ndi mangawa ndi munthu wina. Ngati sakhala pamodzi kufuna kuthetsa magawano amayamba. Mavuto osatha amalepheretsa kuchulukana.

### **YANKHO:**

Mateyu 18:15-17 amapereka malangizo othetsa mavuto pakati pa anthu mu thupi la Yesu. Werengani chitsanzo cha Paulo ndi Banaba mu Machitidwe 15:36-41. Ngati mavutowa atha bwinobwino, ngakhala kugawana kungabweretse kuchulukana mu ufumu wa Mulungu.

### **VUTO: UTSOGOLERA WA UZIMU WOSAYENERA:**

Kukula kumakhudzidwa ngati atsogoleri safikira makhalidwe a uzimu opezeka Mbaibulo. Miyeso ya atsogoleri a mpingo oikidwa ndi Mulungu ndi zoyenereza ku uzimu. Sasamala za maphunziro a munthu ndi kuthekera kwa munthu kuyerekeza ndi makhalidwe a uzimu wa munthu (onani I Samueli 16:7).

**YANKHO:**

Mtaogoleri ayenera kusiya udindo wake kufikira aika “nyumba yake” (moyo wake wa uzimu ndi banja lake) mmalo mwake. Atsogoleri ayenera kukhala ndi zowayenereza zomwe zili mu I Timoteo 3 ndi Tito 1:5-9.

**VUTO: KUKANA KUSINTHA.**

Anthu ali ndi chikhalidwe chokana kusintha. Ambiri amakhutira ndi zinthu zimene zakhala zikuyendera kwa zaka 40 zapitazo. Sakonda kuvomereza zinthu zatsopano.

**YANKHO:**

Kumbukirani kuti cholinga cha mpingo ndi kuchita maualiki ndi kuchulukana ku uzimu sikumasintha. Njira zokwaniritsa cholingachi zimatha. Ndi zoona kuti tiyenera kugwiritsa ntchito njira za Mbaibulo za mpingo woyamba, koma dziko lasintha kuchokera nthawi imene ija. Sitingakane njira zatsopano chifukwa sizimapezeka Mbaibulo. Monga makina a computer, ma disiki a uthenga wabwino amene Paulo sanagwiritse ntchito. Pakuti kunalibe nthawi imeneyo.

**VUTO: MAVUTO A KULUMIKIZANA**

Kuchulukana kumalephereka ngati palibe kulumikizana bwino pa uthenga wabwino. Atumiki amayeera kusangalasa anthu awo ndi mawu a pamwamba ndi kuonetsa chidziwitso cha maphunziro awo a umulungu. Poto amalemphera kulumikizana ndi zosowa za anthu. Ntchito zawo sizigwirizana ndi mawu awo.

**YANKHO:**

Uthenga ukuyenera kufalisidwa mu njira yoti anthu amvestere. Alaliki, aphunzitsi ndi avangeli ayenera kupereka uthenga mu muyeso wa anthu amene akuwalalikira mmalo mwa mawu a akulu ndi kuonetsa chidziwitso. Pamene Yesu amaphunzitsa, anthu amamvetsera ndi kumvetsetsa (Marko 12:37).

Mmene uthenga ukuperekedwa uyenera kusinthidwa molingana ndi mmene anthu alili pa maphunziro awo (Aroma 1:14). Kulumikizana kwa mmawu ukuyenera kugwirizana ndi makhalidwe a moyo. Tikuyenera kukhala ochita mawu ndi olengeza mawu. Kulengeza kwa chikhulupiriro chatu kumakhala kopambana pamene zinthu za Mulungu zikuonekera mmoyo wathu (Filemoni 6).

**VUTO: KUSIYANA KWA ZIKHALIDWE, DERA NDI ZIPEMBEDZO.**

Mipingo ina simakwanitsa kufikira anthu mdera lawo chifukwa “Sali ngati ife.” Samatumikira kwa iwo amene ndi osiyana chikhalidwe, mtundu, ngakhale chiyankhulo. Mpingo ina imakana kuwoloka malire posafuna kuti anthu a dera lina akhale a mumpingo mwawo. Ena amakana chiyanjano ndi mipingo ina. Ena anazipatula kudziko moti sangachulukane chifukwa samalumikizana ndi osakhulupirira.

### **YANKHO:**

Onani Aefeso 2:14. Palibe makoma a kusiyana mwa Yesu. Mpingo wamanga makoma a kusiyana amene akuyenera kuchotsedwa. Tikuyenera kudutsa chikhalidwe chathu, chiyankhulo, dera komanso zipembedzo ndi cholinga choti tikafikire anthu onse. Tikuyenera kusiya pambali zomemera ndi machimo ndi kuyamba kuika chidwi pa kufikira anthu a dziko lonse ndi uthega wabwino (Ahebri 12:1-2). Sitikuyenera kudzipatula kudziko, koma tikhale mdzikoli koma osachita nawo ntchito za uchimo (Yohane 17:15). Kudzipatula kudziko sizitanthauza kusiyana kapena kusalana.

### **VUTO: KUKHALA ONERERA OSATI OTENGA NAWO MBALI**

Onera ndi anthu amene amangoyang’anira koma satenga now mbali mu zochitika za Mulungu. Samaberekana mu uzimu. Amanyalanyaza kulalikira ndi kupanga ophunzira kwa atumiki “ophunzira.” Mpingo wodzala ndi anthu ononerera sumakula.

### **YANKHO:**

Munthu wina aliyense adziwe udindo wake pa lamulo la Yesu pa Mateyu 28:19-20. Anthu akuyenera kutsogoleredwa kuti agwiritse ntchito mphatso zawo za uzimu ndi cholinga chakuti mpingo ukule bwino (Timoteo 1:6). Atumiki ayenera kukonzekeretsa anthu ku utumiki (Aefeso 4:12). Munthu aliyense akhale wochitachita, ndi khomo lililonse likhale malo a ulakili (II Timoteo 2:2).

### **VUTO: OTEMBENUKA SAKHALA OPHUNZIRA**

Okhulupirira atsopano sakula kukhala ophunzira. Amabwerera ku moyo wawo wakale kapena kukhala ana mu uzimu amene sakwanitsa kuchulukana ku uzimu.

### **YANKHO:**

Okhulupirira tsopano ayenera kuumbidwa ndi kukonzekeredwa ku utumiki ngati kuchulukana kupitilire. Ulaliki sukhala okwanira kufikira wotembenuka mtima akhala wamphamvu wa Yesu. Chiphuncityso chikuyenera kuchitika ukaliki pamene zikuchitika (Mateyu 28:19-20).

### **VUTO: MANTHA**

Kuopa kulempera ndi mdani wamkulu pa kuchulukana. Werengani fanizo la matalente pa Mateyu 25:14-30. Kapolo amene amaopa sanachite bwino. Sanachulukane mu uzimu.

## **YANKHO:**

Khalani pa ubale ndi Mulungu mwachikondi osti mwa mantha (I Yohane 4:18).

## **VUTO: CHIDWI PA NTCHITO OSATI KULAMBIRA**

Dongosolo, ndondomeko ndi zochitika za mpingo zikhoza kutenga malo a malambiro. Mwambo wa mapemphero ukhoza kukhala wa zolemegeza, kupereka ndalama ndi zina.

## **YANKHO:**

Ikani koyambirira zinthu zofunika mu mpingo. Chikondi ndi kulambira Mulungu zikhale koyamba. Chikondi ndi utumiki kwa ena zibwere pambuyo. Mapulogalamu ena amabwera pambuyo pa zochitika ziwiri zazakuluzi (Mateyu 12:29-31).

## **VUTO: KUTUMIKIRA DERA OSATI ANTHU.**

Pali zosowa zambiri lero mu dziko lathupi. Pali osauka ambiri amene afunika chakudya, zovala, ndi malo okhala. Pali anthu amene afunika mankhwala ndi ntchito. Pali mavuto ena a kayendetsedwe ka boma, maphunziro amene akufunika kukonzedwa. Izi ndi zosowa zenizeni zimene mpingo ungather kutumikira anthuwa mu dzina la Yesu. Koma nthawi zambiri chidwi chathu chimakhala kutumikira dera osati kupulumutsa moyo wa anthu.

## **YANKHO:**

Mkazi amene anali ndi Yesu pachitsime amafuna madzi a kuthupi koma Yesu anampatsa chosowa chake chenicheni cha ku zuimu (onani Yohane 4). Maitanidwe a akulu a mpingo sikutumikira dera, koma kupulumutsa anthu amene ndi ovutika ku uzimu. Kutenga nawo mbali mu zochitika ndi kuchita mwa nzeru sikudzapangitsa anthu anjala kufuna mkate wa moyo.

## **VUTO: KUSAKHULUPIRIRA**

Werengani nkhani ya Israyeli pa malire a dziko lolonjezedwa la Mulungu (Numeri 13). Israyeli sanalowe mdziko la malonjezano chifukwa chosakhulupirira. Anabwerera mbuyo mu chipululu muja ndipo mbadwo onse unatha kwa zaka 40.

Wokhulupirira aliyense ndi mpingo uliwonse ayenera afike pa “Kadesi” pa malo a uzimu. Akhoza kupita chitsogolo mu chikhulupiriro mkufusa malonjezo a Mulungu, kapena abwerera mbuyo mkusakhulupirira kwawo mkufa ku uzimu.

## **YANKHO:**

Kusakhulupirira kumalepheretsa kukula komanso kuchulukana. Mpingo ukuyenera kukhulupirira kuti kukwaniritsa chipambano pa ulaliki ndi kupanga phunzira kwagona pa chikhulupiriro (Marko 6:15). Kukhulupirira kutenga malo a kusakhulupirira. Chikhulupiriro chimakula ndi Mau

a Mulungu. Anthu ayenera kuchita zinthu mwachikhulupiriro. Ndipo chikhulupiriro chikhale ndi ntchito yake (Yakobo 2:26).

### **VUTO: UNYINJI OSATI KHALIDWE**

Chidwi pa unyinjira osati khalidwe kumabweretsa nthu osakhwima mu uzimu. Zimatheka kukhala ndi anthu ambiri koma olephera kukhala ophunzira ndi osakhwima.

### **YANKHO:**

Onaninso chaputala cha 6 cha phunziroli. Gwiritsani ntchito mfundo kuti mukule ku uzimu.

### **VUTO: ANTHU AMASOCHERA MU KHAMU LA ANTHU.**

Pamene mpingo ukukula, anthu “amataika mu gulu la anthu.” Amayamba kuzimvu kuti alipo ambiri. Sipakhala kulumikizana, kusamalana ndi chidwi. Chidwi chimakhala pa khamu osati pa munthu.

### **YANKHO:**

Moyo umodzi ndi wopambana kuposa dziko lonse (Mateyu 16:26). Ngakhle tiyenera kukhuzidwa ndi dziko lonse, koma tisachotse chidwi chathu pa munthu mu khamu. Anthu amabadwa mu uzimu kwa nthawi imodzi koma amataika payekha.

Palibe chithu ngati kutembenuka mtima kwa gulu. Ngakhale gulu litembenuka ku ulaliki, munthu aliyense amapanga chisankho yekha. Tisaike chidwi chathu pa khamu la anthu ndi kuiwala munthu mmodzi. Yesu amaitana munthu mu khamu la anthu mkuyamba kumutumikira. Kuyamba mautumiki ang’ono ndi njira imodzi yosunga utumiki wa anthu mu khamu ndipo kuchulukana mumpingo kumatheka.

### **VUTO: TIMAGULU TA MUMPINGO**

Nthawi zina “timagulu” tiyamba mu mpingo. Awa ndi magulu a ang’ono a anthu amene amakhala pamodzi ndi cholinga chofuna kusiyantsa kapena kukana kuyanjana ndi anzawo. Gululi limalola anthu ena kukhala nawo koma ena amawakana.

### **YANKHO:**

Baibulo limaphunzitsa kuti mchitidwe oterewo ndi wolakwika. Werengani Yakobo 2:1-10. Chikhulupiriro choterechi chimafuna kulapa chifukwa ndi tchimo.

### **VUTO: GULU LAMOYO, KOMA ANTHU AKUFA**

Gulu ndi lofunika, koma kukula mu uzimu kumalephereka pamene chidwi chili pa gulu osati kukhala ndi moyo wa Mulungu. Miyambo, malamulo, ndi zikhulupiriro zimachotsa uzimu

weniweni (Marko 7:13), gulu la mumpingo likhoza kukhala ndi moyo ndithu, koma anthu amene ndi moyo weniweni wa uzimu mthupi umafa ngati palibe moyo wauzimu.

Mipingo yoterryi imakhala ndi ndondomeko zabwino ndipo amakhala ndi “dzina limene amachitira izi” koma ku uzimu akufa (Chibvumbulutso 3:1). Moyo wa uzimu umafa. Amakhala ndi maonekedwe a chipembedzo koma mphamvu yake adaikana (II Timoteo 3:5)

#### **YANKHO:**

Mpingo umafanizidwa ngati thupi. Thupi ndi lamoyo, osati chith cha ziwalo ayi. Gulu silingapereke moyo. Koma chithu cha moyo chingathe kupereka moyo. Moyo wa thupi la mpingo ukuyenera uphunzitsidwe ndipo utumiki utsindikidwe (I Akorinto 12).

#### **VUTO: KUSOWA CHIKONDI**

Mpingo ukhoza kukhala ndi machitichita a uzimu, koma opanda chikondi. Anthu samachezeka. Samakondana wina ndi nzake. Pamakhala chiwawa, udani, malingaliro oyipa kwa wina.

#### **YANKHO:**

Utumiki uliwonse, mpatso iliyonse ndi ntchito iliyonse ya munthu kapena mpingo ili chabe popanda chikondi. Werengani ndi kugwiritsa ntchito I Akorinto 13.

#### **VUTO: KUSOWA KWA ZINTHU**

Anthu ndi ndalama ndi zinthu zofunika pa kuchulukana. Kukula kukhoza kukhala kopinimbira pamene palibe anthu odzipereka ku masomphenya. Kosowa kwa thandizo la ndalama kungalepheretse kukula ndi kutukuka kwa mpingo.

#### **YANKHO:**

Tsindikani za Ufumu wa Mulungu osati kukamba za utumiki wa munthi. Yesu analonjeza kuti zinthu zonse zimene tizifuna tidzapatsidwa tikachita zimene zili pa Mateyu 6:33. Pemphererani anthu oyenera kugwira ntchito ya Mulungu kuti akakolole kholola la uzimu mmunda (Mateyu 9:37-38).

## MAYESO ODZIYETSA NOKHA

1. Lembani Vesi Lotsogolera kuchokera pamtima.

---

---

---

---

---

2. Perekani tanthauzo la kukula “mopinimbira.”

---

---

3. Werengani zitsanzo za nyengo za mipingo yambiri mmene zilili. Zindikirani mavuto ndi kupereka mayankho ake a Mbaibulo.

Chitsanzo A. Akazi awiri mumpingo samalankhulana wina ndi mzake. Mkazi A anayankhula zinthu zosakhala bwino kwa mkazi B. Kodi mungapereke yankho laotani?

---

---

---

Chitsanzo B. Usiku wa sabata iliyonse mpingo umakhala ndi zochitika, koma anthu ochepa ndiwo amene amabwera kwa Ambuye. Kodi pamenepa vuto ndi chiyani? Yankho ndi liti?

---

---

---

Chitsanzo C. Okhulupirira atsopano ochepa ndiwo amene amapezeka ku mpingo mwakanthawi, kenako amabwereranso ku zintchito zawo zakale za uchimo. Ena amakhalabe mu mpingo, koma makanda mu uzimu. Kodi vuto ndi chiyani? Nanga yankho ndi liti?

---

---

---

(Mayankho a mafunsowa akupezeka kumapeto kwenikweni kwa bukuli)



## **KUPITILIZA KUPHUNZIRA**

1. Bwerezani mavuto a kukula mu uzimu amene akambidwa mu chaputalachi. Pangani mndandanda wa zinthu za mumpingo wanu zimene zimalepheretsa kukula ndi kuchulukana. Kodi mavutowa mungawakonza bwanji?
2. Onaninso phunziro ndi kudziwa zinthu zimene zimalepheretsa kukula kwa moyo wanu wa uzimu. Kodi mavutowa mungawathetse bwanji?
3. Unguzani mpingo wanu ndi moyo wanu wa uzimu. Kodi zinthuzi zikulepheretsa kukula kwa moyo wanu wa uzimu kupatula zimene zatchulidwa mu chaputalachi? Ngati ndi choncho lembani mndandanda wa mavutowa ndi kupeza mayankho mu Baibulo.
4. Werengani makalata 7 a kumpingo mu Chibvumbulutso chaputala 2-3. Lembani mndandanda wa mavuto omwe amene amapezeka mmipingoyi ndi mayankho ake ochokera kwa Mzimu Woyera.

## CHAPUTALA CHA 12

### MALO OCHITIRAPO MAPHUNZIRO

#### ZOLINGA:

Pakutha pa chaputalachi muyenera:

- Kulemba Vesi Lotsogolera kuchokera pamtima.
- Kudziwa njira zimene Paulo anagwiritsa ntchito pophunzitsa okhulupirira a ku Aefeso.
- Kulongosolo malo ochitirapo maphunziro ku Aefeso.
- Kulongosola cholinga chokhala ndi malo ochitirapo maphunziro.
- Kulemba chidule cha malangizo oyambitsa malo achitirapo maphunziro.
- Kuyambitsa malo ochitirapo maphunziro.

#### VESI LOTSOGOLERA:

**Koma pamene ena anaumitsa mtima ndi kusamvera, nanenera zoipa Njirayo pamaso pa anthu, anawacokera, napatutsa akuphunzira, nafotokozerana masiku onse m'sukulu ya Turano.**

**Ndipo anacita comweco zaka ziwiri; kotero kuti onseakukhala m'Asiya anamva mau a Ambuye, Ayuda ndi Ahelene (Machitidwe 19:9-10).**

### MAWU OYAMBA

Musanayambe kuphunzira chaputalachi, werengani Machitidwe 19:1-20. Ndimeyi imakamba za utumiki wa Paulo ku mzinda wa Aefeso kumene Paulo anagwiritsa ntchito njira zapadera za kuchulukana ku uzimu. Anakhazikitsa malo ochitirapo maphunziro. Mu chaputala ichi muphunzira mmene mungachulukanire kudzera mu utumiki okhala ndi malo ochitirapo maphunziro.

### NJIRA YA AEFESO

Pamene Paulo anafika ku Aefeso, anafufuza ophunzira amene analiko. Anthuwa amenewa anali atamva kale ndi kulandira uthenga wabwino mkukhala otsatira Yesu (Machitidwe 19:1).

Okhulupirira atsopanowa amafunika kupitiliza maphunziro ndi cholinga choti akhale atumiki amphamvu mu mzinda mwawo. Chidwi choyamba cha Paulo chinali kuphunzitsa ophunzirawa zokhudza Ufumu wa Mulungu.

Paulo anawaphunzitsa kudzera mu zimene amadziwa ndipo chinthu choyamba chimene anachita kunali kuwatsogolera ku moyo watsopano wa uzimu, ndiwo ubatizo wa Mzimu Woyera (onani Machitidwe 19:2-8). Kudzera mu chionetsero cha mphamvu ya Mulungu mmoyo wake, Paulo

anawaphunzitsa chitsanzo chake. Anachitira umboni za mphamvu zambiri zimene anachita mu dzina la Yesu (Machitidwe 19:11-12). Iwo amene sanali otsatira enieni a Yesu anafika poyera mkulapa (Machitidwe 19:13-17). Otembenuka mtima amapezeka ambiri (Machitidwe 19:17-20).

Pamene panali chitsutso pa uthenga wabwino kuchokera kwa atsogoleri a malamulo, Paulo anakhazikitsa malo ochitirapo maphunziro a ophunzira a Yesu ku Aefeso:

**Koma pamene ena anaumitsa mtima ndi kusamvera, nanenera zoipa Njirayo pamaso pa anthu, anawacokera, napatutsa akuphunzira, nafotokozerana masiku onse m'sukulu ya Turano (Machitidwe 19:9-10).**

Malo amene Paulo anakhazikitsa amapereka maphunziro a zaka ziwiri kwa ophunzira. Cholinga cha sukuluyi chinali kufuna kuchulukitsa ophunzira amene akhoza kufalitsa uthenga wabwino:

**Ndipo anacita comweco zaka ziwiri; kotero kuti onseakukhala m'Asiya anamva mau a Ambuye, Ayuda ndi Ahelene (Machitidwe 19:10).**

Malo a maphunzirowa analibe malire pa chikhalidwe. Ophunzira amatumikira kwa ayuda ndi amitundu omwe. Sukuluyi inalibenso malire pa dera. Ophunzira samatumikira mu mzinda wawo wa Aefeso okha, koma anafika mu chigawo chonse cha m'Asiya. Malo amaphunziro amene Paulo anakhazikitsa anakwaniritsa cholingachi:

**Ndipo anacita comweco zaka ziwiri; kotero kuti onseakukhala m'Asiya anamva mau a Ambuye, Ayuda ndi Ahelene (Machitidwe 19:9-10).**

**Cotero mau a Ambuye anacuruka mwamphamvu nalakika (Machitidwe 19:20)**

Sukulu yak u Aefeso inaphunzitsa okhulupirira kuti akhale atumiki amphamvu a uthenga wabwino. Ophunzirawa anachulukana mu uzimu kufikira onse amene anali mu m'Asiya ndi Mau a Mulungu. Pokhazikitsa malowa Paulo anachulukitsa utumiki wake.

## **NTCHITO YOPITILIRA**

Werengani Machitidwe 19:23-41 ndi 20:1. Kupanga komanso kugulitsa kwa zinthu za matsenga, mabuku, ndi zina anali malonda a akulu ku Aefeso. Pamene anthu analapa machimo awo ndi kuyamba kutsata njira ya uthenga wabwino, sanagulenso katunduyi zimene zimagwira ntchito pa chipembedzo cha mafano. Zonse zimene anagula kale anaziotcha.

Amalonda amene amapezamo phindu mu zogulisa zawo anakwiya. Moti mpungwepungwe unayamba koma kumapeto, Paulo anachoka ku mzindako. Koma atngochoka Paulo, anasiya chinachake chofunika kwambiri. Anasiya gulu limene linali ophunzira amene amafalitsa uthenga wabwino. Anasiya malo ochitirapo maphunziro amene anapitilira kutsogoleraanthu obadwa mwatsopano mkukhala ophunzira. Malo amene Paulo anakhazikitsa anapitilira kuchuluka ngakhale mu nthawi imene sanali ku mzindako.

## **CHOSOWA CHALERO**

Chosowa chokhala ndi malo ochitira maphunziro chilipobe lero. Pamene anthu atembenuka mtima mkuchuluka, ndi zofunikira kuti akuphunzitsaidwa. Ophunzirawa ayenera kupatsidwa udindo wofikira anzawo ndi uthenga wabwino.

Pamene dziko likukumana ndi kusintha kwa maboma, atumiki ambiri amishoni amakakamizidwa kuchoka dziko limene akutumikira. Ngati kuchulukana kupitilre mu nthawi imene iwo kulibe, akuyenera kusiya malo ochitira maphunziro ngati mmene zinalili ku Aefeso.

Zotsalira za chaputalachi zikupereka malangizo okhazikitsa malowa. Akhoza kuyambika ndi ka gulu kakang'ono ka mipingo kapena ndi munthu mmodzi amene ngati Paulo anagwira masomphenya ochulukitsa mu njira imeneyi.

## **KODI TINGAKHAZIKITSE BWANJI MALO OCHITIRAPO MAPHUNZIRO**

Pofuna kuyamba malo ochitirapo maphunziro:

### **1. FUNANI DONGOSOLO LA MULUNGU:**

Ngakhale Paulo anaphunzitsa ophunzira kulikonse amatumikira, sanakhazikitsa malo a maphunziro kulikonse amapita. Mwaphunzira njira zambiri za kuchulukana ku uzimu mu phunziroli. Cholinga cha Mulungu cha kuchulukana kwa ophunzira ndiko kufalisa uthenga wabwino basi. Njira zimene anagwiritsa ntchito pofuna kufikira cholingachi zinali zosiyana.

Gawo loyamba lokhazikitsa malo ochitira maphunziro ndi kufunafuna chifuniro cha Mulungu. Harvestime International Institute amapereka phunziro mutu wake, “Kudziwa Kulankhula kwa Mulungu” limene lingakuthandizeni kumvetsa mmene Mulungu amaululira chifuniro chake kwa munthu. Podziwa kuti dongosolo la Mulungu limasiyana potengera malo, chikhalidwe, chosowa komanso njira za dongosolo la malowo zimasiyana.

### **2. KUMVETSA CHOLINGA:**

Mukuyenera kumvetsa bwino cholinga chokhala ndi malo ochitirapo maphunziro molingana ndi chitsanzo cha Aefeso. Cholinga cha sukuluyi sikuphunzitsa anthu kupeza mapepala a ntchito, malonda, kampani kapena ulimi ayi. Makoleji ndi masukulu a maluso amapanga izi.

Sukulu yaku Aefeso inaphunzitsa ophunzira ndi kuwakonzekeeretsa ku ntchito ya utumiki. Cholinga chinali kufalisa uthenga wabwino ku dziko lonse ndi kwa anthu a mitundu yonse. Okhulupirira atsopano anaphunzitsidwa kukhala ophunzira ndi kupitilira kuchulukana. Ena mwa ophunzirawa anali ochita malonda kapena alimi. Koma sukuluyi sinawaphunzitse mu zimenezi koma mu kukhala okhulupirira ochitachita kaya akugwira kumsika kapena ndinu otumikira nthawi yonse.

Malo ochitira maphunziro sanatenge malo a mpingo. Okhulupirira amapitilira kusonkhana mu sunagoge, amene anali malo amodzi osonkhanira a mpingo woyamba. Okhulupirira ayenera kupitilira kusonkhana mmipingo ya kumadera ndi kunyumba kwawo. Sukulu ya Aefeso inali

mbali yopitiliza ntchito ya mpingo. Sukuluyi sinatenge malo a utumiki wa mpingo, koma kukulisa. Cholinga cha maphunzirowa si kuchotsa malo ena ophunzitsira bwino ayi pofalisa uthenga.

Ndi cha nzeru kulemba cholinga cha sukuluyi. Izi zimatchedwa “Mawu a Cholinga.” Zimakuthandizirani kukhala owona ku cholinga cha malo ochitira maphunzirowa. Harvestime International Institute ali ndi phunziro lotchedwa “Dongosolo la Zolinga” limene lingathe kukuthandizani kulemba mawu a cholinga.

### **3. KHALANI NDI DONGOSOLO LA NDALAMA**

Ili ndi dongosolo loyerekeza mitengo ya katundu amene mudzafune. Zinthu zimene mugwiritse ntchito pa skuluyi, mmene mulengezere kwa anthu, ndi ndondomeko ya maphunziro anu. Izi zimafuna ndalama imene mudzagwiritse ntchito. Ngati muli ndi ndalama yoyambisira sukulu, mukuyenera kupanga dongosolo la ndalamazi. Pamenepa mukuyenera kulemba mitengo ya zinthu imene mwakonza.

Ngati ndalama mulibe yoyambisira sukulu, pempherani kuti Mulungu akupatseni ndalama. Ngati gulu la mpingo ndi limene likufuna kuyambitsa malowa, mwina mpingo uliwonse utha kupereka zimene angathe, komanso ophunzira atha kupereka imene angathe. Kusowa kwa ndalama kusakupangiseni kusayambitsa sukuluyi. Gwiritsani ntchito maphunziro a Harvestime International Institute ndipo yambani sukulu kunyumba kapena malo amene simupereka ndalama. Aphunzitsi kapena othandizira akhoza kudzipereka kuphunzitsa ophunzira.

### **4. SANKHANI MALO**

Mzinda wa ku Aefeso umene Paulo anasankha kuti ukhale malo ochitirapo maphunziro unali wotanganidwa ndi malonda. Unali malo okopa alendo ndi likulu la zamatsenga ndi mafano a Mulungu wa mkazi wotchedwa Diyana. Zinthu izi zinapangitsa kuti anthu ambiri azikakhala kumeneko. Kufikira anthu a ku Aefeso ndi uthenga unali mwayi wawo wa maphunziro. Osati chifukwa uthenga ukanalalikiwa kwa anthu ambiyi ayi, koma kunali mwayi wofikira anthu zikwi amene amabwera kumeneko ngati alendo ndi amalonda amene amabwerera kwawo atamva uthenga. Ngati ophunzira amatha kuphunzira mmene amachitira za matsenga ndi ziwanda ndiye kuti akhoza kutumikira madera ena ndi mphamvu yaoipa ya Satana. Paulo sanawachotse ophunzirawa mu nyengo zawo ndi cholinga choti alandire maphunziro. Anawaphunzitsa mu nyengo imene inali yodziwika kwa iwo. Anakhalabe ku malo awo ndi mu chiyankhulo chawo. Paulo anasankha malo oyenera a sukulu ya maphunziro. Mufunseni Mulungu akutsogolereni pamene mukufuna malo ochitirapo maphunziro.

Pamene mukuganiza za malo, dzifunseni mafunsowa:

Koyamba: Kodi malowa anthu amafikapo kuti angalandire maphunziro?

Anthu akuyenera kutha kuzapedza maphunziro. Ngati mulu kumudzi sukuluyo ikhale malo oti anthu atha kuyenda. Kaya ndi mu mzinda anthu ayende kappa pa galimoto. Kaya ndi malo a zochitika, anthu ambiri athe kufikapo.

Kachiwiri: Kodi malowo ali kwabwino?

Kwa Aefeso kunali malo abwino ochitira malonda. Ngati mkotheke malowo akhale koteru amene anthu pachikhalidwe amatha kubwerako kudzapanga zinhtu zina. Makamaka kumene kuli chiwerengero cha anthu ambiri. Musaope kaya malowo kuli malinga a Satana, pakuti izi zidzathandiza ophunzira kuona zimene akuphunzira.

Kachitatu: Kodi ndi zipangizo zANJI zimene mugwiritse ntchito?

Sizofunika kumanga malo a maphunziro a chilendo, Paulo anagwiritsa ntchito zipangizo zimene zinalipo kale. Mungayambitse sukuluyi mmasukulu, mumpingo, ndi malo a zochitika. Ngati mkotheke malo akhale opanda mbali. Malo amene si ampingo ayi pofuna kupereka mwayi kwa anthu onse. Abusa ena amaopa kuti anthu awo apita ku mipingo ina. Mipingo ina simalola anthu awo kupita ku mipingo ina. Maganizowa si abwino, ngakhale alipo.

## **5. SANKHANI DONGOSOLO LA MAPHUNZIRO OYENERA:**

Dongosolo la maphunzira ndi maphunziro amene mwakonza kuti aziphunzitsidwa. Onentsetsani kuti maphunzirowo akhale amene akwaniritsa cholinga chophunzitsa ndi kukonzekeretsa atumuki. Mwachitsanzo phunziro la mmene mungamvere kulankhula kwa Mulungu ndi lofunika pokwaniritsa cholinga cha sukulu kusiyana ndi phunziro la mbiri ya mpingo wanu.

Maphunzirowa aziika chidwi pa zimene Yesu anaphunzitsa kwa anthu wamba amene anasanduka pohunzira oflaitisa uthenga wabwino. Ndipo akhale ochkera Mbaibulo. Maphunziro amenewa akupezeka kudzera kwa Harvestime International Institute. Posasankha maphunzirowa muonenso mpahunziro a anthu amene mukufuna kuwaphunzitsa. Kodi amatha kulemba ndi kuwerenga? Nanga amalankhula chiyankhulo chanji, kulemba ndi kuwerenga? Kodi muzafuna owamasulira ziyankhulo kapena ayi?

## **6. SANKHANI APHUNZITSI NDI OGWIRA NTCHITO ZINA**

Mfuseni Mulungu akutsogoleleni posankha aphunzitsi. Onentsetsani kuti mukugwirizana ndi cholinga cha sukuluyo ndi maphunziro amene mukuphunzitsa. Maphunziro a aphunzitsi ndi ofunika kuwaonanso. Akhale okhoza kuphunzitsa ophunzira molingana ndi maphunziro awo. Koma koposa zonse moyo wawo wa uzimu ndi mphatso zawo ndizofunikanso. Sankhani okhulupirira amene ali ndi mphatso yophunzitsa.

Kupatula aphunzitsi sankhani ogwira ntchito ena amene azikonza malo ophunzirira. Amene akuyenera kumalankhula zambiri za sukuluyo ndi ena.

## **7. LENGEZETSANI SUKULUYO**

Anthu sangabwere kusukuluko ngati sanamvepo zoti ilipo. Mukuyenera kulengeza uthenga wa sukuluyo ku mudzi, mzinda ndi kumene mufuna kutumikira. Mmene mungalengezere zitengera ndala zimene muli nazo ndi malo. Ngati ndi mudzi wochepe ndiye kuti mokhoza

kumangoyendera, momwemonso ku mpingo. Kaya mukhoza kulankhulana ndi abusa anzanu zokhuza sukuluyo. Mu mzinda uthenga umavuta kufalisa chifukwa cha chiwerengero chochuluka. Izi ndi zina mwa njira zimene mungasate kufalisa uthenga wa sukuluyo.

Kuyenda mmipingo. Pezani mipingo imene ili mdera lanu poimba mafoni kwa abusa kenako awuzeni za masomphenya anu. Apempheni kuti awuze mpingo wonse za masomphenya anuwo mu mwambo wa mapemphero.

Nkhani za mu mpingo: Ngati mpingo wanu umalengezetsa nkhani kwa mamembala anu, konzekerani kukalengezetsako za sukuluyi.

Nkhani zoulutsidwa: Konzekeraninso kukasiya uthenga wa sukulu yaniyi ku nyumba imene amalembako ndi kufalitsa nkhani.

Mauthenga ofalitsidwa: Mukhozanso kuika uthengawu mutaulamba bwino mmasukulu, mmitengo komanso malo amene aanthu amapezekako ambiri. Pemphani chilolezo kwa akuluakulu mmalowa.

Zochitika za akhristu: Ngati pali mwambo waukulu, umene waitana anthu ambiri a mumpingowo, pemphani atsogoleri kuti alengezetse za sukulu yanuyo ku mwambo wa zochitikazo.

Njira zina ndi monga kupereka makalata kwa anthu, kupezeka ku malo amene atsogoleri amakhalako. Komanso tumizani mauthenga ku mipingo yosiyanasiyana kwa abusa. Kuonjezera apo, gwiritsani nchito mabungwe a chikhristu amene ali mdera lanu. Pamphani atsogoleri kuti akupatseni mwayi wolengezetsa uthanga kwa anthu awo mu mikumano yawo.

## **8. CHITANI MKUMANO WOYAMBA:**

Kukumana koyamba mkalasi ndi kofunika kwambiri. Kukuyenera kukhala kwa abusa ndi okhulupirira onse opezeka mderalo. Zimene mungachite ndi monga:

- a. Kuwalandira aphunzitsi ndi ogwira ntchito ena.
- b. Kufotokoza cholinga cha sukulu ya maphunziro.
- c. Kufotokozapo za dongosolo la maphunziro ake.
- d. Kupemphera, kulambira ndi kuyimba.
- e. Kuyesera kuphunzitsa ngati chitsanzo
- f. Pemphero lotsekera zonse.
- g. Kulembetsa kwa iwo amene awonetsa chidwi choyamba. Izi zichitike kumapeto koma musanaseke. Ophunzira akumane ndi aphunzitsi awo ndi kutenga dongosolo la maphunziro awo. Izi ziwalimbikitsa kulembetsa ndi kumaliza maphunziro awo.

## **9. MAPHUNZIRO OPITILIRA**

Izi ndi zina zimene mungamachite pamene sukulu yayambika: kukonzekera, kusunga nthawi, kupemphera, kubwereza zomwe mwaphunzitsa, kugwiritsa ntchito njira zophunzitsira

zosiyanasiyana, lolerani kuyenda kwa Mzimu Woyera ndipo tsogolerani ophunzira kuti ayambe kugwiritsa ntchito zimene aphunzira. Komanso apatseni ophunzira ntchito yokachita kwawo pa zimene aphunzira

Kumbukirani: cholinga cha sukuluyi ndi kukonzekeretsa ophunzira kupita kulikonse ndi uthenga wabwino.



## MAYESO ODZIYETSA NOKHA

1. Lembani Vesi Yotsogolera kuchokea pamtima

---

---

---

2. Kodi ndi njira ziti zimene Paulo anagwiritsa ntchito kukphunzitsa okhulupirira a ku Aefeso?

---

---

---

---

3. Fotokozani za malo ochitirapo maphunziro a ku Aefeso.

---

---

---

4. Kodi cholinga cha kukhala ndi malo ochitira maphunziro ndi chiyani?

---

---

---

5. Perekani chidule cha malangizo amene aperekedwa pofuna kutsekula sukulu ya maphunziro.

---

---

---

---

---

---

(Mayankho a mafunsowa akupezeka kumapeto kwenikweni kwa bukuli)

## **KUPITILIZA KUPHUNZIRA**

1. Eliya anali ndi sukulu ya aneneri mu Chipangano Chatsopano ndipo anali otsogolera (onani II Mafumu 2:4). Poganzira utumiki wa aneneri, kodi ndi maphunziro anji amene akuyenera kukhala nawo?
2. Harvestime International Institute imapereka maphunziro amene akhoza kugwiritsidwa ntchito ku sukulu yamaphunziro potenga maphunziro akewa. Sukuluyi ili ndi pulogalamu yoyendayenda ya akhristu komanso iwo amene ali ndi njala yotumikira Mulungu. Maphunzirowa amakamba za zimene Yesu anaphunzitsa ndi kusintha anthu wamba kukhala okhulupirika potengera uthenga kudziko lapansi ndi kuonetsera mphamvu yake. Maphunziro ake agawidwa mmagawo monga chiyambi cha maphunziro ndi mabuku asanu ndi limodzi a maphunziro.

## MAYANKHO A MAFUNSO ODZIYETSA NOKHA

### CHAPUTALA CHA 1:

1. Ndipo Yesu ananena nao, Idzani pambuyo panga, ndipo ndidzakusandutsani inu asodzi a anthu (Marko 1:17).
2. Lamulo loyamba ndi lomaliza la Yesu kwa ophunzira ake linali lowapanga kuti achulukane. Onani Marko 1:17 ndi Machitidwe 1:8.
3. Kuchulukana ndi kukhala ambiri mu chiwerengero poberekana. Kuchulukana ndi njira yochulukitsa. Pamene chinthu chikuchulukana chimachuluka nthawi ndi nthawi.
4. Kuchulukana ku uzimu kumachitikanso ku uzimu. Wokhulupirira amagawana uthenga wabwibo ndi anthu ena, ndi kuwatsogolera kukhala okhazikika mwa Yesu.
5. Njira ndi ndongosolo lokwaniritsa cholinga chathu.
6. Ndondomeko ndi dongosolo la njira zimene zaikidwa pamodzi pofuna kufikira cholinga.
7. Ndondomeko za njira zochulukana mu uzimu ndi dongosolo la njira limene limapangitsa okhulupirira kufikira cholinga chawo chochulukana ku uzimu.
8. Fananitsani chidule chanu ndi zimene mwaphunzira mu chaputala choyamba.

### CHAPUTALA CHA 2:

1. Pakuti wapeputsa tsiku la tinthu tating'ono ndani? (Zakariya 4:10).
2. Fanizirani chidule chanu ndi zomwe mwaphunzira mu chaputala cha 2.
3. Kukula mmadera, mu chikhalidwe, mu chiwerengero ndi mu uzimu.
4. Ena mwa mavesi awa akhoza kugwiritsidwa ntchito: Numeri 1:1-3; 2:23-24; 26:1-4; Mateyu 9:13; Luka 15:7; 19:10 Machitidwe 1:15; 2:41; 4:4; 6:7; 9:32; 12:24; 16:5; 19:20; 28:30-31; Yohane 3:16; II Petro 3:9
5. Fanizirani chidule chanu ndi zimene mwaphunzira mu chaputala cha 2.
6. a. Zonama                      b. Zonama

### CHAPUTALA CHA 3:

1. Ndipo ndi mafanizo otere ambiri analankhula nao mau, monga anakhoza kumva (Marko 4:33)
2. Fanizo ndi nkhani imene imachokera mu zochitika za anthu koma imakhala ndi tanthauzo la kumwamba kapena la uzimu.
3. Kumvetsetsa choonadi cha uzimu chimene chimaphunzitsidwa mmapemphero kunapatsidwa kwa ophunzira chifukwa anapatsidwa maganizo a uzimu. Iwo amene analibe uzimu amalephera kumvetsa.
4. Onani zimene zili mu mafanizo mu chaputala cha 3.

#### **CHAPUTALA CHA 4:**

1. Ndipo zimene wazimva kwa ine mwa mboni zambiri, zomwezi uikize kwa anthu okhulupirika, amene adzadziwa kuphunzitsa enanso (II Timoteo 2:2)
2. Kuchitira umboni ndi kuwauza anthu zimene wazimva, ndi kukumana nazo. Mu nyumba ya malamulo, mboni ndiye amene amanena za munthu kapena chinthu. Monga mboni, timanena za Yesu ndi dongosolo la chipulumutso kwa anthu onse.
3. Atumiki amene sanasankhidwe ndi amene amapezeka mu mpingo wa Mulungu. Kapena kuti ndi anthu onse a Mulungu. Ena amatchedwa otumikira koma osati nthawi zonse mu mpingo.
4. Mawu oti “akulu a mpingo” ndi atumiki amene anasankhidwa kutumikira mumpingo. Iwo amene utumiki umakhala gawo la moyo wawo amene amakhala olembedwa ndi mpingo.
5. Maitanidwe a anthu amene satumikira nthawi yonse ndi a kwa okhulupirira onse amene ndi “ansembe” kapena atumiki a uthenga wabwino.
6. Dongosolo la Mulungu likupezeka pa Machitidwe 1:8. Mzimu Woyera ndiye mphamvu ypoangitsa kuchulukana, Yesu ndiye uthenga wopita kudziko lonse. Okhulupirira ndiwo zotengera za uthengawu.
7. Andreyana ndi Hananiya.
8. Yambani kugawana uthenga wabwino ndi achibale, anzanu ndi ogwira ntchito limodzi. Uthenga umafala mwachangu kwa magulu amenewa.

#### **CHAPUTALA CHA 5:**

1. Ndiponso Ine ndinena kwa iwe, kuti iwe ndiwe Petro, ndipo pa thanthwe ili ndidzakhazika Mpingo wanga; ndipo makomo a dziko la akufa sadzaulaka uwo (Mateyu 16:18-19).
2. Okhulupirira onse mwa Yesu abadwanso kachiwiri mu ufumu wa Mulungu.
3. Mpingo unabadwa mwa Mzimu Woyera pa tsiku la Pentekosite. Onani Machitidwe 4.
4. Fanizirani mayankho anu ndi zitsanzo za mu chaputala cha 5.
5. Kulambira, kutumikira, chiyanjano ndi utumwi.
6. Onani zokambirana za mu chaputala cha 5.
7. Onani zokhambira za mu chaputala cha 5.

#### **CHAPUTALA CHA 6:**

1. Pakuti kunamkomera Atate kuti mwa iye cidzalo conse cikhalire (Akolose 1:19).
2. Kukula mkati ndi kukula mu uzimu ndi kuumbika kwa mamembala a mpingo. Uku ndi kukula kwa makhalidwe abwino osati kukula mu chiwerengero.
3. Kukula mu uzimu ndi kuchuluka kwa uzimu kumene kumabwera chifukwa chakukula kwa moyo wa uzimu mmoyo wa okhulupirira.
4. Onani zokambirana za mu chaputala cha 6.
5. Onani zokambirana za mu chaputala cha 6.
6. Onani zokhambirana za mu chaputala cha 6.

#### **CHAPUTALA CHA 7:**

1. Ndipo mau a Mulungu anakula; ndipo ciwerengero ca akuphunzira cidacurukatu ku Yerusalemu (Machitidwe 6:7).
2. Kukula mu chiwerengero ndi pamene okhulupirira apezera okhulupirira nzake kwa Yesu ndi kuwabweretsa chiyanjano pa mpingo wawo. Zotsatira zake zimakhala kukula mu chiwerengero cha mpingo.
3. Fanizirani ndi chidule chanu pa zokambirana za mu chaputala cha 7.

4. Fanizirani ndi mayankho anu pa zokambirana za mu chaputala cha 7.

### **CHAPUTALA CHA 8:**

1. Kotero Mipingoyo inalimbikitsidwa m'cikhulupiriro, nacuruka m'ciwerengo cao tsiku ndi tsiku (Machitidwe 16:5).
2. Kukula mmadera kumachitika pamene mpingo uyambitsa mpingo wina mu zikhalidwe zofanana. Mpingo watsopanowo ndi nthambi ina ya “likulu” la mpingo monga mmene zimzkhallira mdziko kholo ndi mwana.
3. Kudzala mpingo ndi kukula ndi kulumikiza kwa mpingo. Mmodzi amadzala mpingo watsopano monga mlimi wodzala mbeu. Mbue zimabereka mtengo watsopano wofanana ndi kholo la mbeu ija.
4. Anthu a ku mpingo wa ku Yerusalemu anabalalikana chifukwa cha chizunzo. Anapita mmalo osiyanasiyana kulalikira uthenga ndipo anthu amatembenuka mtima.
5. Izi ndi njira zokulitsira mpingo:
  - mpingo kudzala mpingo wina
  - mpingo kugwirizana kudzala mpingo
  - mpingo waukulu kugawana mkupanga mpingo iwiri kapena yoposera apo.
  - munthu wokhulupirira kupita kumalo ena kukayambitsa mpingo.
6. Pali mitundu ingapo ya kukula mmadera kwa mipingo:
  - mpingo kukatumikira ku madera ena
  - mpingo kukatumikira kumadera a mitundu ina
  - mpingo ya cholinga chapadera.
7. Zofunikira za Mbaibulo ndi kudzala mipingo mmalo osafikilidwa, malo osalandilika, mmizinda keneko mmidzi.
8. Uthenga umene umabadwitsa mipingo ndi wochokera Mbaibulo, wokamba za Khristu, wofikira chosowa.

### **CHAPUTALA CHA 9:**

1. ...Kukawatsegulira maso ao, kuti atembenuke kucokera kumdima, kulinga kukuunika, ndi kucokera ulamuliro wa Satana kulinga kwa Mulungu, kuti alandire iwo cikhululukiro ca macimo, ndi colowa mwa iwo akuyeretsewa ndi cikhulupiriro ca mwa Ine (Machitidwe 26:18).
2. Kukula kolumikiza ndi pamene mpingo ukula polalikira ku madera ena, a zilankhulo zina, mitundu ya anthu ena amene ndi osiyana zikhalidwe.

3. Machitidwe 1:8. Uthenga wabwino umayenera kupita kutali kuchokera ku Yerusalemu kufika ku “malekedzero a dziko” lapansi.
4. Mtumwi Paulo.
5. Fanizirani chidule chanu ndi zomwe zili mu chaputala cha 9.

### CHAPUTALA CHA 10:

1. Pomwepo Yesu anati kwa ophunzira ace, Ngati munthu afuna kudza pambuyo panga, adzikane yekha, natenge mtanda wace, nanditsate Ine (Mateyu 16:24).
2. Mawu oti “kutembenuka” amakamba za wokhulupirira watsopano mwa Yesu amene wabadwa mwatsopano mwa chikhulupiriro mkukhala gawo la ufumu wa Mulungu.
3. Mawu oti “wophunzira” ndi munthu amene watembenuka mtima mkukhazikika pa maziko a chikristu ndipo amakhala wokonzeka kupanga ophunzira ena. Wophunzira ali ngati mwana wa sukulu amene amaphuzira potsatira. Ndi kuposa kukhala ndi mzeru. Ndi kuphunzira kumene kumasintha makhalidwe a moyo wamunthuyo.
4. Zinthu zofunika pa kukhala wophunzira ndi kuwerengera mtengo wake, kuchita zofunika, ndi kukhala ndi cholinga chenicheni.
5. Mfundo 9 zofunika pa kukhala wophunzira ndi:

Kusankha	malangizo	chiyanjano
Chionetsero	kudzipatula	kutenga nawo mbali
Kuyang'anira	kupatsa ena zochita	masomphenya
6. Wophuzira ndiye amene:

Amazikaniza yekha	amasiya zonse	amakhala Mmau
Amatsatira Yesu	amakhala womvera	amakhala wotumikira
Ufumu umakhala choyamba	amabala chipatso	amaonetsera chikondi
7. Yesero lenileni la wophunzira ndi zimene zimachitika pamene simukupezeka ndi ophunzira anu. Kodi amakhalabe okhulupirika ndi kuphunzitsa ena amene ali ndi kuthekera kopitilira kuchulukana?

### CHAPUTALA CHA 11:

1. Wodala munthuyo wosayenda mu uphungu wa oipa, Kapena wosaimirira m'njira ya ocimwa, Kapena wosakhala pansa pa bwalo la onyoza. Komatu m'cilamulo ca Yehova muli cikondwerero cace; Ndipo m'cilamulo cace amalingima usana ndi usiku. Ndiye akunga mtengo wooka pa mitsinje ya madzi; Wakupatsa cipatso cace pa nyengo yace, Tsamba lace lomwe losafota; Ndipo zonse azicita apindula nazo (Masalmo 1:1-3).

2. Pamene kukula kuli kopinimbira kudziko, thupi silimakula moyenera. Pamene kuluka kwa uzimu kuli kopinimbira, anthu sakula mu uzimu ndipo mpingo sukulanso.
3. Chitsanzo A: Mlango wolakwiridwa ayenera atsati malangizo amene ali pa Mateyu 18:15-17

Chitsanzo B: Mpingo ukuyenera kugwiritsa ntchito njira ya “bwerani” osati ya “pitani.” Pakhoza kukhala ntchito zina zosayenera zimene ziyenera kusadzidwa.

Chitsanzo C: Mpingowo mkutheka sumaphunzitsa anthu atsopano mwa Yesu kuti akhale ophunzira.

## **CHAPUTALA CHA 12:**

1. Koma pamene ena anaumitsa mtima ndi kusamvera, nanenera zoipa Njirayo pamaso pa anthu, anawacokera, napatutsa akuphunzira, nafotokozera masiku onse m'sukulu ya Turano (Machitidwe 19:9-10).
2. Paulo anaphunzitsa zimene anakumana nazo (Machitidwe 19:2-8), poonetsa chitsanzo (Machitidwe 19:11-12), ndi pochititsa maphunziro (Machitidwe 19:9).
3. Malo ochitira maphunziro a ku Aefeso amapereka maphunziro a zaka ziwiri amene amaphunzitsa atumiki mu zikhalidwe ndi mmadera pofafalita uthenga wabwino (Machitidwe 19:10-20).
4. Cholinga cha kukhala ndi malo ochitira maphunziro ndi kuphunzitsa ophunzira ndi kuwakonzekeeretsa ku ntchito ya utumiki.
5. Fanizirani chidule chanu ndi zomwe zili mu chaputala cha 12.